# Kutsatira Yesu Pamodzi

## Katekismu Wa Mpingo Wa Nazarene Mu Africa

*Dr. Theodore P. Esselstyn*

*"Following Jesus Together"*
*Chichewa*

Katekisimu
Wa Mpingo Wa Nazarene
Mu Africa

**KUTSATIRA YESU PAMODZI**

## KUTSATIRA YESU PAMODZI
**Katekisimu Wa Mpingo Wa Nazarene Mu Africa**

---

## ZA M'KATIMU


| Mutu | | Tsamba |
|---|---|---|
| | Mawu Otsogolera (Foreword) | 5 |
| | Mawu Oyamba (Preface) | 7 |
| 1. | Mpingo Wa Nazarene | 9 |
| 2. | Zimene Timakhulupilira Mwa Mulungu | 15 |
| 3. | Munthu Ndi Chipulumutso Chake | 22 |
| 4. | Chipulumutso Ndi Chiyeretso | 29 |
| 5. | Buku Lopatulika Ndilo Limatitsogolera m'Moyo Wathu | 37 |
| 6. | Anazarene Amakula m'Chisomo | 43 |
| 7. | Kuona Zokhudzana Ndi Moyo | 49 |
| 8. | Mpingo Wa Chikhristu | 58 |
| 9. | Mbiri Ya Mpingo Wa Nazarene | 64 |
| 10. | Chigawo Cha Africa | 71 |
| 11. | Anazarene Amagwira Ntchito Pamodzi | 77 |
| 12. | Africa Adziwe Yesu | 84 |


---

**FOLLOWING JESUS TOGETHER**
an Orientation to the
Church of the Nazarene in Africa
Theodore P. Esselstyn, Author

Catechism in Chichewa


Buku ili limasindikizidwa ndi a Africa Nazarene Publications. Buku ili likhoza kugulidwa ku Mpingo wa Nazarene. P. O. Box 90566, Bangwe Blantyre 9, Malawi. Sikuloledwa kuti maphunziro awa asindikizidwenso popanda chilolezo.

## MAWU OTSOGOLERA (*FOREWORD*)

Ndimakumbukirabe msonkhano wa pachaka wa chigawo *(district)* womwe ndidaphunzira kuti kalasi la pamayeso la patchalitchi limakhala la chaka chathunthu.

Choonadichi chinadza m'chidziwitso changa nditatsimikizira pamsokhano wa pachaka kuti iwo ayenera kulandira chiwerengero china cha anthu m'banja la Anazarene chaka chimenecho. M'modzi wa abusa akuluakulu muchigawocho anaima ndi kunena kuti zimenezi sizingatheke chifukwa zimenezi zingatenge chaka kwa munthu wongotembenuka mtima kumene, makamakanso kuyambira nthawi yonse membala watsopanoyo atalandiridwa mukalasi la pamayeso, kuti amalize maphunziro omuyenereza kukhala membala wa Mpingo wa Nazarene.

Izi zidandipatsa maganizo ndi kukambirana zoti pazitenga miyezi itatu ali mukalasi la mayeso pophunzira katekisimu wamakono yemwe angalembedwe m'maganizo a uzimu, ogwirizana ndiponso momwe mungalembedwe pakutha pa maphunziro a miyezi itatu ya abusa.

Chitsulo chiyenera kupindidwa pomwe chatentha ndi kufiira. Maphunziro akukula kwa mpingo amatiuza kuti nthawi yoti nkumutsogolera Mkhristu kuti akhwime mu uzimu ndi miyezi yoyambirira atangotembenuka mtima, pomwe chimwemwe chili "chosasimbika" ndipo moyo watsopanowu ukangoyamba. Ndi chimodzimodzi ndikubadwa kuthupi - m'zaka zawo adakali aang'ono, ana amakhoza kusintha kuposa nthawi yoti akula kale. Popitirira kufufuza, ndinaona kuti, kalasi lomwe limakhalapo la pamayeso ndi lomwe limakhala la chaka m'malo mompatsa ufulu ndi mtendere zomwe anazipeza atangobadwa kumene.

Titakambirana makhwerero a utsogoleriwa, tinaona kuti panalibenso wina woyenera kuti nkulemba buku la katekisimu kuposa Dokotala T. Esselstyn, yemwe ndi mkulu woyendetsa ntchito za sukulu za ubusa mu chigawo cha Africa.

Dokotala Esselstyn sikuti ndi mphunzitsi amene anaphunzira kwambiri kokha, komanso anakulira ku Africa, ndiye kuti ndi woyenera kugwira ntchitoyi chifukwa ndi womvetsetsa miyambo ndi chikhalidwe cha mu Africa ndi kudziwa kusiyanitsa pakati pa zofunika ndi zosafunika.

Kulembedwa koyamba kwa katekisimu kunali kovuta kuti tingasindikize kwenikweni, komanso kulondoloza kwenikweni kuti tisaphonye pakuti panali kufunika ntchito yaikulu.

Pamene tasindikiza koyamba KATEKISIMU WA MPINGO WA NAZARENE wa chigawo cha Africa, tikuyamikira ntchito yaikulu ya Dokotala T. Esselstyn ndi pemphero lake kuti abusa athu onse, matchalitchi awo, makamakanso Akhristu atsopano apeze thandizo lomwe akulifuna ndi kuliyembekeza.

Bukuli likhale chida chachikulu m'manja mwa anthu athu kuti Mulungu akalemekezeke.

*Richard F. Zanner*

Dokotala Richard F. Zanner
Mkulu wa Mpingo wa Nazarene mu Africa
*(Regional Director, Africa)*

---

Abusa J. F. Huff ndimtsogoleri watsopano muAfrica kuyambira mwezi wa April 2000 mmalo a Dr. r. f. Zanner

## MAWU OYAMBA (*PREFACE*)

Cholinga cha bukuli ndicho kuthandiza mbusa pophunzitsa mamembala atsopano (apamayeso). Lakonzedwa kuti liphunzitse maphunziro khumi ndi awiri. Maphunziro amenewa angaphunzitsidwe pophunzitsa phunziro limodzi pasabata lililonse, kapenanso mbusa akhoza kuphunzitsa maphunziro ambiri nthawi imodzi, poyesa kuchepetsa sabata zophunzitsira maphunzirowa.

Cholinga ndicho kuthandiza mamembala kuti asangomvetsetsa za mpingo, komanso aphunzire kukhala ndi kugwira ntchito mwamphamvu mu mpingo. Pali njira zomwe timaphunzitsira chikhulupiriro cha Mpingo wa Nazarene nthawi zonse. Mbiri ya mpingo imathandiza mamembala atsopano kuti amvetse chiyambi cha ziphunzitso za Mpingo wa Nazarene, ndi mgwirizano wawo ndi mipingo ina. Komanso m'mene mpingo umakumanirana ndi zinthu m'dziko zomwe anthu amachita mosalemekeza Mulungu. Ife a Mpingo wa Nazarene tikhoza kulisintha dziko lapansi. Tiyenera kutsatira Yesu pamodzi, kukhala moyo wathu wotsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Chikhristu sichinthu chochitenge ngati mulu wa zikhulupiriro koma njira yabwino ndi ya chigonjetso. Pomaliza, ntchito ya Mpingo wa Nazarene kwa anthu a ku Africa ndi dziko lonse lapansi yakonzedwa.

Bukuli linapemphedwa ndi Regional Executive Committee ya Mpingo wa Nazarene mu Africa. Ikuimira ntchito ya anthu ambiri omwe athandiza posonkhanitsa, kusankha ndi kufufuza, ndipo akhoza ndi kulemba zoyenera kusindikizidwa. Tiyenera kutchulapo maina awa: E. H. Litswele, A. Alexander, D. Mathebula, H. Pieterse, C. Mathebula ndi gulu la anthu ogwira ntchito yosindikiza mabuku ya Africa Nazarene Publications motsogozedwa ndi Mai M. Moyer.

A Theodore P. Esselstyn, Mlembi

---

Abusa Steve Doerr - Literature Co-ordinator watsopano mmalo a Mai Maryel Moyer.

## MPINGO WA NAZARENE

### Kodi Mpingo Wa Nazarene Ndi Chiyani?

Mpingo wa Nazarene ndi banja la anthu okhulupirira mwa Yesu Khristu amene anagwirizana kuti azipembedza ndi kutumikira Mulungu pamodzi ndi kuyesetsa kukhala monga Iye.

Chiyanjano cha Mpingo wa Nazarene chinafika kumaiko oposera zana limodzi (100) m'dziko lonse lapansi. Ndipo Likulu La Mpingo *(International Headquaters)* lili ku Kansas City, Missouri ku America. Pa Msonkhano Waukulu *(General Assembly)* umene udachitika m'chaka cha 1985, mpingowu unagawidwa muzigawo khumi ndi zisanu (15) ndipo chimodzi mwa izo ndi chigawo cha Africa.

### Kodi Ndi Anthu Otani Amene Amatchedwa Anazarene?

Munthu aliyense amene walowa mu Mpingo wa Nazarene amachitira umboni za chipulumutso ndipo amafunitsitsa kulandira Mzimu Woyera kuti azikhala mwa iye. Kuonjezera apo, munthuyo amachitiranso umboni kuti adzathandiza mpingo m'njira iliyonse kuti upite mtsogolo pantchito yake yofalitsa Uthenga Wabwino.

Anazarene amamupempha Mulungu kuti awakhululukire zochimwa zawo zonse. Iwo achoka ku uchimo ndipo akufunitsitsa kuchita ntchito zabwino. Akufunanso kuti Mzimu Woyera wa Mulungu azilamulira miyoyo yawo ndi kumawatsogolera kuti akule m'Chikhristu ndi kubala zipatso za Mzimu m'moyo mwawo. Izi zitathauza kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu ndi kuchita chifuniro cha lungu chokha.

### Kodi Makhahlidwe A Anazarene Ndi Otani?

Malamulo Ena Osiyanasiyana *(General Rules)* M'BUKU LA MALAMULO NDI MAYENDETSEDWE (*Manual*) amatifotokozera mwatsatanetsatane za makhalidwe a Anazarene:

Anazarene amapewa choipa ndipo nthawi zonse amachita zabwino ndi kukhala m'chiyanjano chabwino ndi mpingo wawo.

Tikawerenga Buku Lopatulika pa *Agalatia 5:22* timamva za

makhalidwe amene timawaganizira kuti ndi ofunikira kwambiri, ponena za zipatso za Mzimu zoyenera pamoyo wa munthu. Zipatsozi ndi chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima ndi kudziletsa. Izi ndizo zimafotokoza m'mene munthu alili. Ndipo zimene munthu amachita zimasonyeza m'mene iyeyo alili. BUKU LOPATULIKA limatiuza kawirikawiri kuti ife ndife atumiki. *Afilipi 2:1-11* akutikumbutsa ife kuti tiyenera kufunitsitsa kukhala ndi "mtima wofanana ndi Yesu Khristu" ndi cholinga chofuna kutumikira Mulungu mwini wake ndi anzathu. Anatikumbutsanso kuti pamene ife tikutumikira anzathu ndiye kuti tilikumutumikira Iye *(Mateyu 25:31-46)*.

Timachita moyenera tikamagwira ntchito tonse pamodzi kuyamika ndi kupembedza Mulungu wathu komanso utumiki wathu kwa anzathu. Mpingo uyenera kukhala wogwirizana ndipo munthu aliyense ndipo ayenera kutenga mbali yake monga mwa zimene iye angachite komanso ndi mtima wake wonse pakubwera kutchalichi kawirikawiri ndi kukapereka zopereka monga ndalama.

## Kodi Cholinga Cha Mpingo Wa Nazarene Ndi Chiyani?

Timakhulupirira kuti Mulungu anayambitsa Mpingo wa Nazarene kudziko lonse lapansi kuti uphunzitse choonadi chenicheni cha m'Buku Lopatulika kuti Akhristu akhoza komanso ayenera kukhala m'njira yoyenera, yopanda chikayiko imene ingathe kugonjetsa tchimo kudzera mumphamvu ya Mzimu Woyera yemwe akugwira ntchito mwa iwo. A John Wesley adanena kuti chimenechi ndi "Chikhristu Changwiro".

Choonadi chimene Mpingo wa Nazarene umaphunzitsachi chimatipatsa ife chiyembekezo, chiyanjano ndi Mulungu komanso kugwirizana ndi kuyanjana ndi Akhristu anzathu chifukwa cholinga chake chenicheni ndi kuyanjanitsa munthu ndi Mulungu. Chiyanjano cha munthu ndi Mulungu ndicho chiyambi cha kukhalitsana bwino pabanja pamodzi ngakhalenso anthu amene tayandikana nawo kapena kugwira nawo ntchito, ndi kuzindikira kuti ndife ofunikira pamaso pa Mulungu.

## Chifukwa Chiyani Anazarene Ali Ndi Buku La Malamulo Ndi Mayendetsedwe A Mpingo *(Manual)*?

Buku la malamulo ndi mayendetsedwe *(Manual)* la Mpingo wa Nazarene linalembedwa ndi nthumwi za ku Msokhano Waukulu *(General Assembly)*. Nthumwizi zimakomana kamodzi pakapita zaka zinai ndi

kukambirana za malamulo a m'buku la Malamulo *(Manual)* ndipo ngati pali mfundo zina zoti zisinthidwe, bungweli limasintha mfundozo ndi kusindikiza buku latsopano. M'bukuli ndi m'mene mumalembedwa Mayendetsedwe A Mpingo *(Constitution of the Church)*, mawu onena za mbiri yakale ya mpingo, zimene mpingo umakhulupirira ndi malamulo apadera ovomerezeka kuti munthu akhale membala wa mpingo. Mbali yaikulu ya bukuli amalemba za kayendetsedwe ka mpingo, madisitilikiti, zigawo ndi matchalitchi. Amalembanso za mfundo zofunikira kuzitsata monga ngati Mkhristu akafuna kukhala mbusa ndi m'menenso mpingo ungamuthandizire Mkhristu wopezeka ndi mlandu.

Potsatira malamulo a m'BUKU LA MALAMULO NDI MAYENDETSEDWE zimathandiza kuti kayendetsedwe ka Mpingo Wa Nazarene m'dziko lonse lapansi kakhale kofanana.

## Kodi Mpingo Wa Nazarene Unayamba Bwanji?

Mpingo wa Nazarene unayamba m'chaka cha 1908 mumzinda wa Pilot Point ku Texas, America. Mpingowu unakhazikitsidwa kuchokera ku mipingo yosiyanasiyana ya ku America yomwe imakhulupilira ndi kulalikira chiphunzitso cha chiyeretso.

Misonkhano yambiri yolalikira ya chiyeretso inachitika m'madera ambiri ku America, ku England, m'zaka za 1850 kupita mtsogolo kotero kuti magulu ambiri okhulupirira za chiyeretso anakhazikitsidwa. Ndipo magulu amenewa anagwirizana ndi kupanga mipingo ya chiyeretso. M'zaka zapitanzo, mipingo yoposa khumi ndi isanu ndi umodzi (16) yakhala ikugwirizana ndi kukhala mpingo umodzi wotchedwa Nazarene. Dokotala Phineas F. Bresee wa ku Los Angeles, California ku America anali m'modzi wa atsogoleri amene anakhazikitsa Mpingo wa Nazarenewu.

Kuyambira pachiyambi Mpingo wa Nazarene unali ndi cholinga chofalitsa Uthenga Wabwino kudziko lonse lapansi. Bungwe la amishoni ndilo linali ndi udindo wofalitsa uthengawu kudziko lonse lapansi. Ndipo ku America ndi kumene Mpingo wa Nazarene unakula mofulumira.

## Kodi Anazarene Amapembedza Motani?

Misonkhano ya chipembedzo m'Mipingo Ya Nazarene ndi yosiyana padziko lonse lapansi. Zilankhulo, miyambo, mavalidwe, maimbidwe, kamangidwe ndi kakhalidwe ndi kosiyana kwambiri. Komabe, pali zina

zofunika zomwe ndi zofanana.

Kulalikira Mawu a Mulungu ndicho chofunika koposa. Pachifukwa ichi, matchalitchi a Nazarene amakhala ndi gome *(pulpit)* kutsogolo, cha pakati kuti uthengawu umveke bwino. Timakhulupirira kuti Uthenga Wabwino uzichokera m'Buku Lopatulika. Tizilalikira Mawu a Mulungu ndiwo amene amatitsogolera.

Ulaliki wa Nazarene ndi wachitsitsimutso chifukwa umakwaniritsa zosowa za anthu. Guwa limakhala lotseguka monga malo amene tikhoza kupita ndi kukapemphera kuti machimo athu akhululukidwe kapena kumuuza Mulungu nkhawa ndi zosowa zathu. Ulaliki ndi miyambo yathu zimalimbikitsa munthu kukhala ndi kuyenda m'chifuniro cha Mulungu. Choncho, mapemphero a kuguwa komwe munthu angapemphere mothandizidwa ndi Akhristu ena ndi ofunikira kwambiri.

Kutamanda, kupemphera, chimwemwe, zopereka zothokoza zawo ndi umboni ndi zofunika kwambiri popembedza kwa Anazarene. Timachita izi poimba nyimbo ndi makolasi, komanso pochitira umboni za ntchito ya Mulungu ndi m'miyoyo yathu ndi umboni ndi zofunika pamsonkhano wa Nazarene. Zida zoimbira m'matchalitchi a Nazarene zimakhala zosiyanasiyana komanso matchalitchi ambiri, monga kuno ku Africa, ambiri amalemekeza Mulungu m'nyimbo opanda zida zoyimbira.

Kupembedza kwa Anazarene kumadziwikanso ndi kupereka. Timakhulupirira kuti zonse zimene tili nazo zili chabe. Pachifukwa ichi, timakhulupirira kuti tiyenera kupereka chachikhumi pandalama zathu, zokolola zathu ndi zina zomwe tingakhale nazo. Mfundo yonena za chachikhumi inalembedwa momveka bwino m'Chipangano Chakale (*Levitiko 27, Deuteronomo 12, ndi Malaki 3*), koma Aisraeli anatembenuza lamulo la boma m'malo mwa nthambi ya chipembedzo *(Mateyu 23:23)*. Yesu Khristu ananena momveka bwino kuti zonse zimene tili nazo ndi za Mulungu osati chachikhumi chokha *(Marko 8:34-38; Mateyu 25:14-30)*. Pakupembedza, Anazarene amapewa kuphatikiza miyambo yopanda tanthauzo yomwe imaonetsa ngati kuti Chikhristu ndi chipembedzo cha matsenga. Mwachitsanzo, kuvala mikanjo kapena "zovala zina za tchalitchi kokha" nzosafunikira kwenikweni, pakuti palibe chovala chimene chingampangitse munthu kuti akhale woyera. Mulungu amafuna kuyera kwa mumtima. Makandulo, zonunkhiritsa m'tchalitchi, kuvala mitanda kapena mapemphero olembedwa ndi kumanena mobwerezabwereza zonsezi zilibe ntchito

kuchipembedzo chathu.

Nthawi yopembedza ndiyo nthawi ya chiyanjano, kumvera, kupemphererana ndi kuyamika Mulungu. Popembedza munthu ayenera kuika mtima wake wonse osati kungodzionetsera chabe. Pakuti kudzionetsera kukapitirira muyezo sikusonyeza makhalidwe a uzimu a munthu koma umunthu wake.

Mwachidule, msonkhano wabwino wa mapemphero mu Mpingo wa Nazarene ndi umene okhulupirira amakumana ndi Mulungu wawo ndi kumuthokoza ndi mtima wonse mwachikondi. Pakutero okhulupirira amayenda m'chifuniro cha Mulungu tsiku ndi tsiku. Komanso pamsonkhano wabwino woterewu wosakhulupirira Mulungu amatembenuka mitima ndi kulapa machimo awo ndi kulandira Yesu monga Mpulumutsi wawo.

## Kodi Mpingo Wa Nazarene Umakhulupirira Chiyani?

Pali mfundo khumi ndi zisanu (15) za chikhulupiriro zomwe zimanga m'Mayendetsedwe A Mpingo *(Constitution)* a Mpingo wa Nazarene. Mfundo zonsezi zili ndi umboni umene umapezeka m'Buku Lopatulika, ndipo zinalembedwa mwatsatanetsatane m'BUKU LA MALAMULO NDI MAYENDETSEDWE *(Manual)* Mwachidule timakhulupirira:

1. Mulungu m'modzi mwa atatu: Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera
2. Buku Lopatulika la Chipangano Chakale ndi Chatsopano linalembedwa motsogozedwa ndi kuuziridwa *(plenary inspiration)* ndi Mzimu Woyera kutipatsa choonadi chofunikira m'chikhulupiriro ndi moyo wa Chikhristu.
3. Kuti munthu anabadwa ndi chikhalidwe cha uchimo chomwe chinayamba ndi Adamu, choncho aliyense wobadwa atsamira chikhalidwe cha uchimo.
4. Kuti anthu osalapa machimo alibe chiyembekezo ndipo adzalandira chilango.
5. Kuti Yesu Khristu anapachikidwa pamtanda kuti apulumutse mitundu ya anthu padziko lapansi; kotero kuti yense wakulapa machimo ake ndi kukhulupirira mwa Yesu Khristu Ambuye wathu amalungamitsidwa, kubadwa mwatsopano ndi kupulumutsidwa kuchokera ku uchimo.

6. Kuti pokhulupirira Yesu Khristu munthu amabadwa mwatsopano; pambuyo pake ayenera kuyeretsedwa.

7. uti Mzimu Woyera amachitira umboni za kubadwanso mwatsopano ndiponso kuyeretsedwa kwathunthu kwa okhulupirira.

8. Kuti Ambuye wathu Yesu Khristu adzabweranso, anthu akufa adzaukitsidwa, ndipo chiweruzo chomalizira chidzachitika.

## Kodi Makhalidwe A Mkhristu Wa Nazarene Ndi Otani?

Anazarene amakhulupirira kuti makhalidwe a Khristu ndi ofunikira tsiku ndi tsiku. Yesu Khristu anawatchula makhalidwe oterewa ndi liwu limodzi "CHIKONDI". "Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga" zimenezi ananena ndi Ambuye Yesu m'buku la *Yohane 14:15.* Kumvera Mulungu, kukhulupirira kuthupi lake lomwe, Mpingo, kukhala ndi udindo kwa ife eni, kubanja lathu ndiponso kudziko lathu - zonsezi zimatheka pakakhala chikondi.

Akhristu enieni a Mpingo wa Nazarene amapita kutchalitchi mokhulupirika, kuwerenga Buku Lopatulika kawirikawiri, kupemphera ndi kuthandiza ntchito za mipingo kumatchalitchi kumene amakapemphera. Anazarene amakhala okhulupirira kumalo kumene amagwira ntchito, kumidzi yawo ndi m'dziko lawo. Iwo amadziwa kuti chipulumutso ndi mphatso ndi chisomo cha Mulungu kuti ife tikhale ndi moyo. Sichifukwa cha ntchito zabwino zomwe amachita, kapena kulembedwa dzina m'buku la mpingo, kapenanso kulandira ubatizo ayi.

→ → → → → → →

## Mutu Wachiwiri

## ZIMENE TIMAKHULUPIRIRA MWA MULUNGU

### Kodi Chikhulupiriro Chathu Chayambira Pati?

"Pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndipo kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna Iye " *(Ahebri 11:6)*. Kuyanjana kwathu ndi Mulungu kumayamba pamene tamkhulupirira Iye. Ndikosafunikira umboni kuti Mulungu alipo ndi kuti amatipatsa zosowa zathu. Ife tiyenera kungokhulupirira kuti Mulungu amakhala nafe ndipo amatisamalira, ndipo ife timachita monga mwa chikhulupiriro chimenechi. Ife Anazarene, chikhulupiriro chathu mwa Mulungu chinalembedwa momveka bwino mu mfundo yoyamba (1), yachiwiri (11), ndi yachitatu (111) m'BUKU LA MALAMULO NDI MAYENDETSEDWE pamutu womwe umafotokoza za "Zoyenera kuzikhulupirira (Mwa Mulungu)". Mfundo za chikhulupirirozi zalembedwanso m'mutu uno.

#### I. Mulungu M'modzi Mwa Atatu

1. Tikhulupirira Mulungu m'modzi wolenga za Kumwamba ndi dziko lapansi, kuti Iye yekha ndiye Mulungu, Mlengi ndi wolamulira, woyera m'chikhalidwe chake, woyera m'machitidwe ake, nadzionetsera yekha monga Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. *Mateyu 3:16-17; 28:19-20; Agalatiya 4:4-6; Genesis 1; Levitiko 19:2; Yesaya 5:16; Aefeso 2:13-18; Deuteronomo 6:4-5; Yohane 14:6-27; 6:1-7; 20:18-31; 1 Akorinto 8:6; 2 Akorinto 13:14.*

#### II. Yesu Khristu

2. Tikukhulupirira mwa Yesu Khristu Wachiwiri mwa Atatu, kuti analipo ndi Atate kuyambira pachiyambi, kuti mwa Mzimu Woyera anasandulika, nabadwa mwa Maria Namwaliyo, nakhala ndi makhalidwe awiri panthawi imodzi Umulungu ndiponso Umunthu (Mulungu-munthu). Tikhulupirira kuti Ambuye wathu Yesu Khristu adafera machimo athu, ndikuti adawukadi kwa akufa, natenganso thupi lake, nakwera Kumwamba ndipo ali kumeneko kutipembedza ife. *Mateyu 1:20-25; Machitidwe 2:22-36; 1 Timoteo 6:14-16; Aroma 8:3, 32-34; Ahebri 1:1-5; 7:22-28; Luka 1:26-35; 9:24-28; Agalatia 4:4-5; Afilipi 2:5-11; Akolose 1:12-22; Yohane 1:1-18; 1 Yohane 1:1-3; 4:2-3, 15.*

3. Tikhulupirira mwa Mzimu Woyera, Wachitatu mwa Atatuwo. kuti Iye ndiye wachikulire ngakhale tsopano ndipo ndi iyeyu amene agwira ntchito m'kati mwa Mpingo wa Khristu, kutsutsa anthu a dziko lapansi chifukwa cha uchimo, ndi kupulumutsa iwo akulapa, ndi kuyeretsa iwo akukhulupirira ndi kuwatsogolera m'choonadi chonse mwa Yesu Khristu. *Yohane 7:39; Aroma 8:1-27; Agalatia 3:1-14; I Atesalonika 4:7-8; 4:15-18, 26; Aefeso 3:14-21; 2 Atesalonika 2:13; I Petro 1:2; Machitidwe 2:33; 15:8-9 I Yohane 3:24; 4:13.*

## Kodi Timakhulupirira Mwa Mulungu M'modzi?

M'buku la Deuteronomo chaputala 6, mavesi 4 ndi 5, timawerenga kuti: "Imvani Israeli; YEHOVA Mulungu wathu, YEHOVA ndiye m'modzi, ndipo muzikonda YEHOVA Mulungu wanu ndi mtima wano wonse ndi moyo wanu wonse ndi mphamvu yanu yonse." Kuli Mulungu m'modzi yekha. Milungu ina yonse ndiyongoganiziridwa kuti ilipo ndipo ndi yopangidwa ndi manja a anthu. Milungu yotereyi ndi mafano chabe si Mulungu ayi.

## Kodi Mulungu Ali Ndi Malekezero?

Mulungu alibe malekezero. Mulungu samafa ayi. Iye ndi wamkulukulu ndi wamphamvu zonse kuposa zinthu zina zonse zimene timadziwa ife. Mulungu malekezero ake sidziko lapansi lino, koma Iye ndi amene analenga dziko lapansi naliikira malekezero m'mene lingakhalire ndi zochitika zake, zonsezi analenga mwa kufuna kwake Mulungu yekha amene amaziongolera zolengedwa zonsezi. Ife timakhulupirira kuti Mulungu ndi wachikhalire, wamuyaya, wopanda malekezero (infinite) ndi wamphamvu zonse *(transcendent)* potanthauza kuti Mulungu alibe malekezero ndipo ndi wamkulukulu kuposa zinthu zonse za pansi pano ndi za m'Mwamba.

## Kodi Pali Mgwirizano Wotani Pakati Pa Mulungu Ndi Dziko Lapansi?

Mulungu ndiye Mlengi. Ndi mphamvu yake ya chilengedwe, anakhazikitsanso malamulo pazolengedwa za padziko lapansi akuti munthu azimugwiritsa ntchito polamula padziko. Mulungu amalamulira dziko lapansi kupyolera munzeru zake zakuya ngakhale analipereka kwa anthu kuti aziliyang'anira *(Genesis 1:28).*

Posonyeza kuti Mulungu amagwira ntchito mosalekeza kudziko lapansi, ife timayamikira ntchitozo polankhula m'njira zambiri. Mwa chitsazo, timati Mulungu ndiye wachikondi, Mulungu ndi wachifundo, Mulungu samakondera ayi. Komanso Mulungu amakwiya pamene timulakwira ndipo amadzudzula amene awakonda. Iye amachitanso nsanje ngati ife tipembedza mafano. Mulungu sali ngati nsilikali wotilondalonda koma Iye ndiye bwenzi lenileni lotithandiza.

Mulungu sanatilenge ife chifukwa choti anasowa anthu ayi. Paulo akutiuza momveka bwino pa *Machitidwe a Atumwi 17:24-25* kuti Mulungu sasowa kanthu ndipo Iye akhoza kukhala popanda ife. Mulungu ndi wachikwanekwane payekha. Mulungu analenga anthu chifukwa Iye ndi wachikondi, wopatsa ndiponso mwini moyo. Mulungu siwoononga kapena wolanda kapenanso wodzikundikira.

## Kodi Mulungu Ndi Wotani?

Mulungu amatiuza kuti Iye ndi Woyera. Chiyero ndiye chikhalidwe cha Mulungu. Mulungu pokhala Woyera ndiye kuti Iye ali wachilungamo pazochitika zake zonse. Mulungu amafuna kuti munthu akhale woyera ngati Iye, ngakhale Iye amadziwa kulephera kwa munthu. Kuchokera m'chiyero chake muli chikondi, chilungamo ndi chifundo. Mulungu amatipatsa ife moyo polola kuti chikondi ndi choonadi chake, chilungamo ndi chifundo chake zizikhala m'mitima yathu.

## Yesu Amatiuza Kuti Mulungu Ndi Atate Wathu?

Ambuye Yesu amationetsa bwino lomwe kuti Mulungu ndi Atate wathu pamene ankaphunzitsa omutsatira Iye "Pemphero la Ambuye" lomwe lili pa *Mateyu 6:9-13.* Mulungu ndi atate wathu. Mu pempheroli timaona chithunzithunzi chakuti Mulungu amatisamalira ndipo kuti anatilenga ife monga ana ake. Pokhala ife tingapezeko zosowa zathu, zofuna zathu ngakhalenso kumutulira zovuta zathu.

## Kodi Kungatheke Bwanji Kuti Mwa Mulungu M'modzi Mukhale Atatu?

Ichi ndi chodabwitsa ndiponso ndi chovuta kuti timvetsetse kwenikweni chifukwa Mulungu ndi wamkulu kuposa zinthu zonse za m'Mwamba ndi za pansi zomwe. Mulungu ndi mmodzi ndipo amatiuza izi kawirikawiri *(Deuteronomo 6:5).* Koma amafuna kuti tidziwe Iye monga Mulungu m'modzi mwa atatu omwe. Ndi Mulungu Atate, Mwana,

ndi Mzimu Woyera (M'modzi mwa Atatu - *Three in One*). Ife timavomereza izi chifukwa chakuti BUKU LOPATULIKA limatitsimikizira kuti Yesu ndi Mulungu (*Yohane 1 ndi 17*), ndikutinso Mzimu Woyera ndi Mulungu *(Aroma 8:1-27; Aefeso 3:14-21)*. Pamene Mulungu anadziulula yekha kwa Mose m'buku la *Eksodo chaputala 3* anati: " INE YEMWE NDILI INE".

## Kodi Yesu Khristu Ndi Mulungu?

Yesu Khristu ndi Mulungu yemwe anadzionetsera kwa ife kudzera muchikondi, chisamaliro ndi chifundo cha Mulungu. Pa Yohane chaputala 1 amatiuza kuti "Yesu ndi Mlengi" ndiponso Yesu ndi "Mawu omwe anasandulika thupi". Ndi chinthu chodabwitsa kwa ife kuti Yesu ndi Mulungu ndiponso ndi munthu. Ndikosatheka kuti Yesu timugawe pawiri ndi kusiyanitsa pakati pa umunthu ndi umulungu wake. Chifukwa chakuti sitikhoza kusiyanitsaku, timamuona Iye monga Mulungu weniweni kapena munthu weniweni. Ichi ndi choonadi chenicheni chomwe sitikhoza kumvetsa. Koma ife timadziwa kuti kudzera mwa Khristu Yesu Mulungu amasenza mavuto athu, kulephera ndi kuzunzika kwathu. Iye anasenza machimo athu ndi kufa m'malo mwathu.

## Kodi Ambuye Yesu Anamuchitira Chiyani Munthu?

Ambuye Yesu anabadwa pansi pano nasautsidwa, ndi kupachikidwa pamtanda kuti ife tikhale ndi moyo. Mulungu anapanga munthu kuti munthu akhale pafupi ndi Mulungu, ndikutinso munthu akhale ndi gawo pogwirira ntchito limodzi ndi Mulungu m'chikondi, m'kupatsa, ndi m'chisamaliro cha moyo. *Yohane 3:16* ndilo vesi lopambana m'BUKU LOPATULIKA pofotokoza za chikondi cha Mulungu. Yesu Khristu anadza kudziko lapansi kuti wokhulupirira Iye asafe koma akhale ndi moyo wosatha. Ntchito ndi chiphunzitso cha Yesu zimatipatsa ife njira ya kumoyo wosatha, chikondi, ndi choonadi. Izi zikutsimikizika kuchokera pa *Yohane 14:6* pamene Iye ananena kuti, "Ine ndine njira ndi choonadi, ndi moyo; palibe munthu adza kwa Atate koma mwa ine."

## Kodi Yesu Ndi Wamoyo Ngakhale Lero?

Inde, Yesu Khristu ndi wamoyo ngakhale lero. Iye anagonjetsa tchimo ndi zowawa zomwe zimadza chifukwa cha uchimo. Pa chifukwa ichi, Yesu ali ndi mphamvu ya kutipulumutsa ife lero. Yesu Khristu sanagonje ku imfa. Ndipo Mulungu anamuukitsa kwa akufa *(Afilipi 2:9)*. Umu ndi

m'mene Mulungu amagwirira ntchito. Munthu akadzipereka kwathunthu kwa Mulungu, Mulungu amamupanga munthuyo kukhala dalitso kwa anthu ena.

## Kodi Yesu Amatichitira Chiyani Masiku Ano?

Ambuye Yesu amatipembedzera ife kwa Mulungu nthawi zonse. Iye ndiye Wansembe wathu Wamkulu ndipo amakhala pafupi ndi Mulungu nthawi zonse. Kotero kuti Iye yekha ndiye mthandizi wathu.

## Kodi Mzimu Woyera Ndi Mulungu?

Inde, Mzimu Woyera ndi Mulungu, ndipo taphunzira kale kuti muli Atatu mwa Mulungu m'modzi - Mulungu Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera (*Trinity* kapena *Three in One* m'chingelezi). M'buku la *Aroma 8:1-27* ndiponso m'buku la *Aefeso 3:14-21* amationetsa kuti Mzimu Woyeranso ndi Mulungu. Choonadi chimenechi chimatithandiza ife kumvetsetsa kuti Mzimu Woyera ndi Mulungu amene amakhala ndi kugwira ntchito mwa anthu.

Yesu Khristu anatiuza kuti kunali koyenera kuti Iye abwerere Kumwamba kwa Atate kuti Mzimu Woyera adze pansi pano *(Yohane 16:7-14)*. Pakuti Mulungu, Ambuye Yesu Khristu, anasankha kukhala munthu aliyense. Mzimu Woyera alibe cholepheretsa mwa njira imeneyi. Amakhoza kutumikira munthu aliyense ku malo aliwonse. Mzimu Woyera anadza kwa otsatira a Yesu Khristu patsiku la Pentekoste ndipo pamenepa chiyanjano cha Mulungu ndi anthu chinakhazikitsidwa.

Chiyanjano cha Mulungu ndi munthu chimalumikizidwa kudzera mumpingo. M'Chipangano Chakale, timaona kuti Mulungu adakonzekera kukhazikitsa Mpingo pamene adaika chihema chake pakati pa misasa ya anthu ake. Makalata a mtumwi Paulo ndi Yohane amationetsa kuti ichi chinali mwa anthu okhulupirira Mulungu *(1 Akorinto 3:16; Yohane 14:16)*.

## Kodi Ntchito Ya Mzimu Woyera Ndi Yotani?

Amagwira ntchito mwa anthu. Mzimuyo amagwira ntchito m'miyoyo yathu kutitsutsa chifukwa cha machimo athu ndi kutilimbikitsa kuti tilape. Pamene tilapa machimo athu, Mzimu Woyera amatitsogolera ndi kutidzudzula. Komanso amatilimbikitsa kuti tidzipereka kwathunthu kwa Mulungu. Pamene ife tipereka miyoyo yathu kwa Mulungu, ndi Mzimu

Woyera amene anatilandira ndi kutitsuka mitima yathu ndi mwazi wa Ambuye wathu Yesu Khristu ndipo amatidzaza ife ndi Mzimu wa Mulungu. Chifukwa cha ichi, Mzimu Woyera ndiye amene amatithandiza kuti tikhale ndi moyo wachigonjetso mu Chikhristu chathu. Iye amationgolera ife chimene tachimwa ndipo amatitsogolera ku chilungamo. Mzimu Woyera amatithandizanso ife kuti tikhale odzichepetsa, tilape ndi kutinso tisachimwe dala.

## Kodi Mzimu Woyera Amagwira Bwanji Ntchito M'moyo Mwanga?

Taphunzira kuti Mzimu Woyera amabwera kwa ife tisanapulumutsidwe ndiponso amatilimbikitsa kuti tilape. Chimenechi ndi chisomo cha Mulungu chopanda tsankho *(prevenient grace)*. Taona mwazi wa Woyera ndiye amene amatsanulira mwazi wa Ambuye wathu Yesu Khristu m'miyoyo yathu ndi kutipatsa ife chikhululukiro cha machimo. Ntchito imeneyi timaitcha CHIPULUMUTSO. Taonanso kuti Mzimu Woyera amakhala m'mitima yathu pamene ife tadzipereka kwathunthu kwa Mulungu. Ichi timachitcha CHIYERETSO. Pamene zimenezi zili kuchitika, Mzimu Woyera amagwiranso ntchito zina zambiri kwa ife.

Mzimu Woyera amatithandiza ife kuti tichite umboni weniweni wa Ambuye wathu Yesu Khristu. Yesu anauza ophunzira ake kuti adikire mu Yerusalemu kufikira Mzimu Woyera atadza pa iwo. Pamene tadzipereka kwathunthu kwa Mulungu, Mzimu Woyera nakhala mwa ife, tikatero tikhoza kukhala mboni zenizeni za Yesu. Miyoyo yathu imasinthidwa ndipo Mzimu Woyera amatipatsa ife nzeru ndi mphamvu zochitira Yesu umboni. (Onani ndi kusiyanitsa kuchokera m'mabuku awa: *Mateyu 4:1, 10; Luka 2:26; 12:12; Machitidwe 5:32; 13:4; 16:6.)*

Mzimu Woyera amatipatsa ife mphatso. Mphatso zimenezi ndi zomwe zimatithandiza kuti tigwire ntchito zofunikira mu Mpingo. Ena amakhala alaliki, ena aneneri ndiponso ena atumiki kapena aphunzitsi. Mzimuwo amatipatsa ife nzeru, kumvetsetsa, kuzindikira zinenero ndi zina zambiri monga m'mene Mzimu Woyera angaonere zosoweka za pampingo *(1 Akorinto 7:7; 12:4)*. Mphatso yopambana imene Mzimu Woyera amatipatsa ndi moyo wosatha ndi chikondi cha Mulungu *(Aroma 6:23; 1 Akorinto 13)*.

Ntchito yaikulunso imene Mzimu Woyera amachita m'miyoyo yathu

ndiyo kubala zipatso. Mphatso ndi chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiriro, chifatso, ndi chiletso *(Agalatia 5:22-23)*. Mzimu Woyera anapereka mphatsozi monga mwa kufuna kwake koma kukula kwa chipatso cha Mzimu m'moyo wa munthu ndi umboni woona kuti Mzimu Woyera amakhala mwa iye.

→ → → → → → →

# MUNTHU NDI CHIPULUMUTSO CHAKE

## Kodi Munthu Nchiyani?

Mfundo zitatu "Zoyenera kuzikhulupirira (Mwa Mulungu) "zimatiuza za munthu ndi vuto la uchimo. Mfundozi ndi izi: yachisanu (V), yachisanu ndi chimodzi (V1). Ndipo yachisanu ndi chiwiri (V11). Ndipo pano tikufuna kuti tifufuze za chikhulupiriro chathu muchaputala chimenechi.

### V. Tchimo Lobadwa Nalo

5. Timakhulupirira kuti tchimo lobadwa nalo ndi chikhalidwe choipa chochokera kwa Adamu, chifukwa cha ichi nkosatheka kuti munthu abadwe ndi chilungamo, monga m'mene adalengedwera munthu asanachimwe, ndipo chifukwa cha tchimo la Adamu aliyense wobadwa atsamira chikhalidwe cha uchimo. Ndipo tikhulupirira kuti tchimo limeDeli linakhalabe m'moyo mwa munthu wobadwanso kufikira atabatizidwa ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. *Genesis 3; 6:5; Yeremiya 17:9-10; I Akorinto 3:14; Yobu 15:14; Marko 7:21-23; Agalatiya 5:16-25; Salimo 51:5; 1 Akorinto 3:1-4; Aroma 1:18-25; 5:12-14; 7:7; 8:9.*

### V1. Chiombolo

6. Tikhulupirira kuti Yesu Khristu, chifukwa cha kusautsidwa kwake pokhetsa mwazi wake, ndi imfa yake ya pamtanda yomvetsa chisoni adatiombola ku uchimo wonse wa mtundu wa anthu, ndikuti chigonjetso chimenechi ndicho maziko a chipulumutso chathu ndipo ndichokwanira kuchipulumutso cha ana osalakwa komanso kwa iwo amene angathe kusankha pakati pa chabwino ndi choipa, ndi chokwanira kwa amisinkhu amene adafika pamsikhu wokhala ndi udindo wa iwo eni, pokhapokha atalapa ndi kukhulupirira. *Yesaya 53:5-6,11; Aroma 3:21-26; 1 Timoteo 2:3-6; Marko 10:45; 4:17-25; 5:16-21; Tito 2:11-14; Luka 24:46-48; Akolose 1:19-23; Ahebri 2:9; Yohane 1:29; 1 Akorinto 6:20; 9:11-14; 13:12; 3:14-17; 2 Akorinto 5:14-21; 1 Petro 1:18; Machitidwe 4:10-12; Agalatia 1:3-4; 2:19-25; 3:13-14.*

7. Tikhulupirira kuti munthu adalengedwa m'chifanizo cha Mulungu kuphatikizapo ufulu wakusankha chabwino kapena choipa ndi kupyolera m'kugwa kwa Adamu munthu sangathe kubwerera ndi kudzikonzanso pa yekha ndi kudziitanira payekha Mulungu wake. Koma tikhulupirira chisomo cha Mulungu mwa Yesu Khristu kwapatsidwa kwa anthu onse kuti tibwerere kuchoka ku tchimo kupita ku chilungamo ndi kukhulupirira Yesu Khristu kuti akhoza kutisambitsa ndi kutikhululukira tchimo lathu, ndi kutsata ntchito zabwino ndi zokondweretsa pamaso pa Mulungu.

Tikhulupirira kuti munthu atakhala nacho chidziwitso cha kubadwa kwatsopano ndi kuyeretsedwa akhoza kugwa ndi kusiyana nacho chisomo cha Mulungu, koma pokhapokha atalapa tchimo lake, ndipo ngati satero akhoza kukhala wotayikiratu. Malembo a Udindo wa Mulungu ndi Chilungano Chake: *Genesis 1:26-17; Salimo 8:3-5; Mika 6:8; 2:16-17; Yesaya 1:8-10; Aroma 1:19-20; 2:1-16; Deuteronomo 28:1-2; Yeremia 31:29-30; 14:7-12; 30:19; Ezekieli 18:1-4; Agalatia 6:7-8; Yoswa 24:15.*

Malembo Onena Za Kulemphera Kwa Kusakha Chifukwa Cha Kupsinjika: *Yobu 14:4; 15:14; Yohane 3:6a; Aroma 3:10-12; 5:12; 5:12-14, 20a; 6:14-25; Salimo 14:14; 51:5.*

Malembo A Chisomo Cha Ulere Ndi Ntchito Ya Chikhulupiliro: *Ezekieli 18:25-26; 1 Akorinto 2:9-14; 2 Timoteo 4:10a; Yohane 1:12-13; 3:6b 10:1-12; Tito 2:11-14; Machitidwe 5:31; 2 Akorinto 5:18-19; Ahebri 2:1-3; Aroma 5:6-8, 18; Agalatiya 5:6; 3:12-15; 6:4-6; 6:15-16, 23; Aefeso 2:8-19; 10:26-31; 10:6-8; 11:22; Afilipi 2:12-13; Yakobo 2:18-22; Akolose 1:21-23.*

## Kodi Munthu Ndi Cholengedwa Cha Mulungu?

Timakhulupilira kuti Mulungu analenga munthu m'chifanizo chake. Anthu ambiri lero amati munthu ali chimodzimodzi ndi zolengedwa zina zonse koma amasiyanitsa kuti munthu ali ndi nzeru kuposa nyama zina. Manenedwe otcrewa amatsimikizira kuti pali mgwirirafo pakati pa munthu ndi zolengedwa zina. Pali ubwino, wina woti kulakwa ndi kuchimwa kwa munthu zimangoganiziridwa kuti ndi umbuli. Kufanizira munthu ndi nyama nkosayenera. Akhristu ndiwo amene amatanthauza momveka bwino za ubale wa munthu ndi Mulungu. Mulungu analenga

munthu m'chifanizo chake. Chifukwa chakuti munthu analengedwa m'chifanizo cha Mulungu, chilengedwe choterechi chimamukweza munthu kusiyana ndi nyama zina zonse komanso chimatsimikiza kuti zolakwa za munthu ndi tchimo.

Mulungu atatsiriza kumulenga mwamuna ndi mkazi anati, "zinali zabwino ndithu" *(Genesis 1:31)*. Izi zitanthauza kuti chiwalo chilichonse mwa munthu chimene chinalengedwa – monga thupi, maganizo, machitidwe ndi mzimu wake – Mulungu adatsimikiza kuti "zinali zabwino".

Mulungu analenga munthu "m'chifanizo chake". Izi zitathauza kuti makhalidwe a munthu ndi ofanana ndi a Mulungu. Munthu sanapangidwe mwa ngozi monga zinthu za m'dziko zimasinthika, koma Munthu analengedwa kudzera muluso ndi chifuniro cha Mulungu wamphamvu zonse. Monga Mlengi wake, munthu ali ndi udindo ndipo ayenera kukhala mokwaniritsa cholinga ndi kugwira ntchito pamodzi ndi Mulungu. Ndi chifukwa chake munthu amakhala ndi chosowa pamene iye alekana ndi Mulungu.

## Kodi Munthu Ali Ndi Ufulu Wochita Zimene Afuna?

Munthu ndi cholengedwa. Ndipo pokhala iye cholengedwa, mphamvu ndi nzeru zake zili ndi malekezero. Ngakhale zili choncho, Mulungu adampatsa munthu mwai wosankha. Izi sizongokamba chabe ayi koma ndi zoona. Mwai umenewu ndi wosankha pakati pa zinthu ziwiri kapena zingapo. Kusankha kumeneku kungakhalenso koipa ndipo kusankha chinthu choipa mwadala ndi tchimo. Choncho munthu akhoza kusankha kuchita chabwino kapena choipa.

Mulungu ndi wamphamvu zonse ndipo amadziwa zonse. Iye siwofooka ayi kuti angaopsyedwe ndi munthu, yemwe ndi cholengedwa chake, amene adampatsa ufulu wotha kusankha. Mulungu ali ndi ulamuliro wonse ngakhale adapatsa munthu mwai wakusankha. Chidamukomera Mulungu kupanga munthu ndi kumpatsa munthuyo mtima wodzisankhira. Mulungu anafuna kuti anthu akhale abwino kuchokera pansi pa mitima yawo osati chifukwa cha kulondedwa ayi.

Kusankha chabwino kapena choipa ndi maziko a chiphunzitso cha Wesley. Choyamba, chifukwa chakuti munthu ali ndi mwayi wodzisankhira, zotsatira za kusankha kwake ndi mphotho ya munthuyu.

Choncho munthu akhoza kulunjika makhalidwe ake kuti akhale munthu "wabwino" Kapena "woipa". Chachiwiri, chifukwa chakuti munthu amadzisankhira, izi zitanthauza kuti machitidwe ake ndiwo amene amakonza tsogolo lake. Aneneri a ku Israeli anali kulalikira za choonadichi. Iwo anali kuwauza anthu kuti ngati anthu alapa machimo awo, tsogolo lawo lidzasinthika. Ngati kusankhaku kunali kosafunikira, panalibe chifukwa choti alape.

## Kodi Munthu Ndi Wochimwa?

Inde, mosachita kufunsa munthu ndi wochimwa. Ndizoona kuti munthu analengedwa wangwiro koma lero munthu ali ndi machimo ambiri. Vuto linayamba pamene munthu woyamba, komanso anthu onse obwera pambuyo pake, anasankha kupandukira Mulungu. Kupanduka kumeneku kunawononga munthu ndipo ubale wake ndi Mulungu unasokonekera.

Mwachitsanzo, munthu wina anapanga galimoto yokongola. Chilichonse cha pagalimoto chinali bwino ndithu, kotero kuti mwini wakeyo anayenera kukondwera nayo. Mwini wake akaiyendetsa galimotoyo, panalibe vuto lina lililonse. Tsiku lina mwini galimotoyo anaganiza kuti idziyenda yokha opanda oyiongolera ndipo inachita ngozi. Zotsatira zake, galimotoyo inawonongeka chifukwa galimotoyo singayende payokha. Tsopano, kuti galimotoyi iyendenso pafunika zinthu zitatu: Poyamba, iyenera kupita kugalaja kuti ikakonzedwe. Kachiwiri, ndikofunika kuti pakhale woyiongolera kuti igwire ntchito yake moyenera. Ndipo kachitatu, ndikofunika kuti zitsulo zina zikawonongeka aziyikonza mwamsanga, kumayitsira mafuta ndi kumayitsuka monga m'mene galimoto zina zikhalira.

Chitsanzo cha galimotochi chikutionetsa momveka bwino mavuto amene amamugwera munthu. Iye analengedwa wangwiro ndithu. Nthawi zonse munthu anali woyenera kukhala pafupi ndi Mulungu kuti akwaniritse cholinga ndi zosowa za moyo wake. Koma iye adasankha kuchita zofuna zake ndipo adataya ulemerero wa Mulungu. Munthu adachimwa. Tsopano iye sakhoza kukhalanso wangwiro ndi kukwaniritsidwa pazimene ali nazo pamoyo wake.

Yesu Khristu anadza kudzatiyanjanitsanso ndi Mulungu. Choyamba, Yesu akufuna kutiombola ndi kutipulumutsa ife. Ichi ndi chifukwa chake adapachikidwa pamtanda - - kuti ife tikhululukidwe machimo athu ndi kutikhalitsa angwiro. Yesu amapempha onse omutsatira kuti athandize

pantchito ya chipulumutso - - monga ananena: "... ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wake, nanditsate Ine" *(Marko 8:34)*. Chachiwiri, Yesu amafuna kuti Mzimu Woyera azikhala mwa ife ndikulamulira miyoyo yathu. Ndichifukwa chake ife timalalikira za kufunika kwa chiyeretso. Mulungu ayenera kukhalanso wotilamulira, Yesu amafuna kuti Akhristu azikhala ndi kukula m'chiyanjano chawo ndi Mulungu, kudzera mwa Mzimu Woyera. Kumeneku ndi kukula m'chisomo ndipo ndi kofunikira pamoyo wa Chikhristu. Kuti munthu akule m'chisomo kumafunika mapemphero, kuwerenga Buku Lopatulika, kugwira ntchito ya Mulungu ndi kuthandiza anthu ena ndiponso kumakhalira pamodzi ndi Akhristu ena.

Izi sizikutathauza kuti anthu onse ndi oipa, koma kuti sakhoza kukondweretsa Mulungu nthawi zonse. Zomwe zitanthauza kuti anthu ayenera kukhululukidwa machitidwe awo, ndi kusinthidwa mitima yawo, kuti machimo achotsedwe m'miyoyo yawo (*Genesis 6:5; Yeremia 17:9-10; Aroma 3:9-10, 23; Aefeso 2:3)*.

## Kodi Tchimo Limachotsedwa Bwanji M'miyoyo Yathu?

Yesu ndi amene amachotsa tchimo m'moyo wathu. Mwazi wake umachita zinthu ziwiri kwa ife. Koyamba, mwazi wake umatsuka machimo athu, kubweretsa chikhululukiro, ndiponso amatipanga ife kuyamba kuyenda ndi Mulungu. Kachiwiri, mwazi wa Yesu umatsuka m'mitima yathu ndi kubweretsa chiyanjano ndi Mulungu, kotero kuti Mzimu wake amatilamulira chifukwa amakhala mwa ife.

Mutu wotsatirawo tidzaphunzira kusiyanitsa kwa ntchito ya Mzimu Woyera pakati pa kupulumutsa munthu ndi kuyeretsa. Kuchotsa machimo sintchito yokhayo ya chipulumutso ndi chiyeretso. Kuchotsa machimo kumakhudzanso kusintha kwa munthu m'chiyanjano chake ndi Mulungu, ndiponso anthu ena kuphatikizapo munthuyo payekha.

## Kodi Tchimo Likhoza Kubweranso Kwa Munthu Wokhulupirira?

Adamu adalengedwa wangwiro, ndipo padali mgwirizano weniweni ndi Mulungu, koma iye atayesedwa adachimwa. Palibe munthu amene anganene kuti sangachimwe chifukwa chakuti wakhala Mkhristu zaka zambiri kapenanso ali ndi udindo mumpingo. Tonsefe tikhoza kuyesedwa ndipo tonse tikhoza kusankha kuchimwa. Ngati tisankha kuchimwa,

tiyenera kulapa machimo athu. Ndikofunika kuzindikira kuti Mulungu sadzatitaya ife kutichotsa titachimwa. Iye anatitenga ife kukhala ana a m'banja lake ndipo pamene tachimwa amayembekeza kuti tilape machimo athu. Ngati ife tikakamira kuyenda njira zathu zoipa ndi kukana kulapa machimo athu, tidzilekanitsa tokha ndi Mulungu (*Ezekieli 18:24; Luka 8:13; Agalatiya 5:4; 2 Petro 3:17*). Ndikosafunika kuti tigwe m'chisomo. Yuda amatikumbutsa ife izi pamene anali kupemphera ndi kutipereka ife kwa Ambuye wathu Yesu Khristu amene akhoza "kukusungani kuti mungagwe m'machimo" (*Yuda vesi 24*).

## Kodi Chipulumutso Chimakhudzana Bwanji Pa Za Kumwamba Ndi Gehena?

Chipulumutso chathunthu chinasintha kwambiri moyo wanga tsopano. Chimandithandiza ine kuti ndikhale ndi gawo pantchito yotukula mpingo. Ndilibe nkhawa ina iliyonse. Ndimazindikira kuti ine, ndi anzanga ndife ofunika komanso Mulungu ndi wofunika koposa. Kusintha kumeneku ndi kodabwitsa ndithu. Yesu sanadze pansi pano monga munthu kudzatichitira zabwino pamoyo wa m'dziko. Cholinga cha Yesu ndikutipatsa moyo wosatha ndi kukhala naye komweko.

Moyo wathu sumatha pamene timwalira. Zoonadi, kuli moyo wosatha, ndipo anthu akamwalira chimakhala chiyambi cha moyo wosatha wokhala pafupi ndi Mulungu kapena kutali naye. Ngati ife tilapa machimo athu, tipulumutsidwa ndi mwazi wa Ambuye wathu Yesu Khristu ndi kusintha moyo wathu, ndiye kuti tidzakhala ndi Mulungu kumoyo wosatha. Koma ngati sititero, ndiye kuti tidzatalikirana ndi Mulungu kwa muyaya.

M'buku monga la Chivumbulutso, atumiki a Mulungu amationetsa masomphenya a moyo wangwiro umene tidzakhala ndi Mulungu Kumwamba. Atumiki amenewa adaona ndi masomphenya a KUMWAMBA, kumalo odabwitsa kumene tidzakhala ndi Mulungu. Nthawi zina, tikaona zinthu zina zochitika pa dziko lapansi zotitsimikizira kuti Mulungu ali nafe, timazindikira kuti Kumwamba ndi kwathu pakuti ndiko kumene kuli Mulungu.

Kudzeranso muzizindikiro zambiri atumiki a Mulungu akhala akuphunzira ndikutionetsa zithunzi monga za mazunzo, kuopsa, kuipa ndi chiwonongeko chomwe chimapezeka ku GEHENA chifukwa kulibe Mulungu. Gehena linakhazikitsidwa kuti Satana ndi angelo ake azikhalako

osati munthu ayi. Anthu okhawo amene safuna kusiyana ndi Satana amapita ku Gahena. Mulungu anagonjetsa Satana ndipo Iye anatitsegulira njira kuti ife tisalangidwe chifukwa cha machimo.

→ → → → → → →

# CHIPULUMUTSO NDI CHIYERETSO

## Zoyenera Kuzikhulupirira

Chaputala chino chifotokoza za "Zoyenera kuzikhulupilira (mwa Mulungu)" kuchokera pa mfundo yachisanu ndi chitatu (VIII), yachisanu ndi chinayi (IV), ndi yakhumi (X). Mfundo zimenezi zimafotokoza za kulapa, chipulumutso ndi chiyeretso.

### VIII. Kulapa

8. Tikhulupirira kuti kulapa, kumene kuli kusinthika kwenikweni kwa maganizo atatsutsidwa mumtima ndi kudzisankhira kutembenuka ndi kofunika kwa iwo amene azindikira kuti ndi ochimwa. Mulungu alamulira kuti onse ayenera kulapa. Mzimu wa Mulungu amapatsa anthu onse amene alapa m'chisomo ndi chifundo kuti akhulupirire ndi kutsatira moyo wa uzimu. *2 Mbiri 7:14; Marko 1:14-15; Masalimo 32:5-7; Luka 3:1-14; 13:1-5; 2 Petro 3:9; Aroma 2:4; 2 Akorinto 7:8-11; Yesaya 55:6-7; 1 Atesalonika 1:9; Machitidwe 2:38; 3:19; Yeremia 3:12-14; 5:31; 17:30-31; Ezekieli 18:30-32; 26:16-18; 33:14-16.*

### IX. Chilungamo, Kubadwanso, Kukhala Mwana Wa Mulungu

9. Tikhulupirira kuti chilungamitso ndi machitidwe a ntchito ya Mulungu ya chisomo imene adaipereka kuti timasulidwe kwathunthu kuchilango cha uchimo umene tidauchita, ndi kulandiridwanso monga olungama, ndipo onse amene akhulupirira mwa Yesu Khristu ndi kumulandira monga Mpulumutsi wawo ayanjana ndi Mulungu.

10. Tikhulupirira kubadwanso kuti ndi ntchito ya chisomo cha Mulungu, kuti moyo wolapa ndi kukhulupirira apatsidwa moyo wa uzimu ndi chikhulupiriro, chikondi ndi kumvera.

11. Tikhulupirira kuti kukhala mwana wa Mulungu ndi ntchito ya chisomo ya machitidwe a Mulungu, imene munthu wobadwanso ndi kuyanjanitsidwa amalandiridwa kukhala mwana wa Mulungu.

12. Timakhulupirira kuti chilungamitso, kubadwa kwatsopano, ndi kukhala mwana wa Mulungu zimachitika nthawi imodzi kwa

anthu ofunafuna Mulungu, ndipo zilandiridwa mwa chikhulupiriro, potsatiridwa ndi kulapa, ndipo Mzimu achitira umboni pantchito ya chisomo imeneyi. *Luka 18:14; 2 Akorinto 5:17-21; Yohane 1:12-13; Agalatia 2:16-21; 1 Petro 1:23; Tito 3:1-14; Machitidwe 13:39; Aefeso 1:6-7; 2:1, 4:5; 1 Yohane 1:9; 1 Akorinto 1:30; 6:11; Afilipi 3:3-9; 3:1-2 9; 3:7; Akolose 2:13; Aroma 1:17; 3:21-26, 28; 4:5-9, 17-25; 5:1, 9-13, 16-19; 6:4; 8:1, 15-17.*

## X. Chiyeretso Chathunthu

13. Tikhulupirira kuti chiyeretso chathunthu ndi ntchito ya Mulungu, imene imachitika kwa munthu atalapa, imene okhulupirira amamasulidwa kutchimo lobadwa nalo. Ndipo amakhala wodzipereka kwathunthu kuchifuniro chake cha Mulungu, ndipo pakumvera kuchiyero cha chikondi chimakhala changwiro. Ndipo izi zichitika ndi ubatizo wa Mzimu Woyera umene chidziwitso cha kutsukidwa kwa mtima kuchokera ku tchimo, ndipo Mzimuyo adzalandira, ndi kupereka mphamvu kumoyo wokhulupirira ndi kutumikira.

Chiyeretso chimenechi chinapatsidwa kupyolera m'mwazi wa Yesu, ndipo chilandiridwa nthawi yomweyo mwa chikhulupiriro, potsatiridwa ndi kudzipereka kwathunthu, ndipo pantchito imeneyi Mzimu Woyera achitira umboni.

Ndipo chidziwitso chimenechi chidziwika ndi maina awa "Ungwiro wa Chikhristu" (Chikhristu Changwiro)," Chikondi Changwiro", "Mtima Woyera", "Chidzalo cha Madalitso", ndi Chiyero cha Chikhristu".

14. Tikhulupirira kuti pali kusiyana pakati pa mtima woyera ndi kukula m'Chikhristu (Chikhristu chokhwima). Kuyera mtima kumachitika mwadzidzidzi monga zotsatira za chiyeretso chathunthu; kukula m'chikristu kumabwera monga zotsatira za kukula m'chisomo.

Tikhulupirira kuti chisomo cha chiyeretso chathunthu chimaphatikizana ndi kukula m'chisomo, ndipo kuti tikule m'chisomo chimenechi tiyenera kusamala bwino kuti tikule m'chikhalidwe komanso maonekedwe. Ndipo popanda kuchita izi ndi kukula ndi umboni woyenera wa Chikhristu chathu chisomocho chingatayike. *Yeremia 31:31-34; Aroma 6:11-13, 19; Afilipi 3:10-15; Ezekieli 6:25-27; 8:1-4, 14; 12:1-2; Akolose 3:1-17; Malaki 3:2-3; 2 Akorinto 6:14 - 7:1; Mateyu 3:11-12; Agalatia 2:20; 5:16-25; 5:23-24; Luka 3:16-17;*

*Aefeso 3:14-21; Ahebri 4:9-11; Yohane 7:37-39; 5:17-18, 25,27; 10:10-17; 12:1-2; 14:15-23; 17:6-20; 13:12; Machitidwe 1:5; 2:1-4; 15:8-9; 1 Yohane 1:7, 9.*

Ungwiro wa Chikhristu "ndi Chikondi Changwiro" *Deuteronomo 30:6; Aroma 12:9-21; 13:8-10; Ahebri 6:1; Mateyu 5:43-48; 1 Akorinto 13; 1 Yohane 4:17-18 22:37-40; Afilipi 3:10-15.* "Mtima Woyera" *Mateyu 5:8; Machitidwe 15:8-9; 1 Petro 1:22; 1 Yohane 3:3*

"Ubatizo wa Mzimu Woyera" *Yeremia 31:31-34; Malaki 3:2-3; Luka 3:16-17; Ezekieli 36:25-27; Mateyu 3:11-12; Machitidwe 1:5; 2:1-4; 15:8-9.* "Chidzalo cha Madalitso" *Aroma 1:29.*

"Chiyero cha Chikhristu" *Mateyu 5:1-7:29; Afilipi 1:9-11; 3:12-15; Ahebri 10:19-25; Yohane 15:1-11; Akolose 2:20-3:17; 12:14; 13:20-21; Aroma 12:1-15:3; 1 Atesalonika 3:13; 2 Akorinto 7:1 4:7-8; 5:23; 2 Petro 1:1-11; Aefeso 4:17-5:20; 2 Timoteo 2:19-22; 3:18; Yuda mavesi 20:21.*

## Kodi Chipulumutso Ndi Chiyeretso Zimatanthauza Chiyani?

Mawu akuti "chipulumutso" amatanthauza kuomboledwa m'mavuto amene amapezeka chifukwa cha machitidwe athu oipa. Mawu akuti "chiyeretso" amatanthauza kukhala woyera. Mawu awiriwa chipulumutso ndi chiyeretso amagwiritsidwa ntchito m'njira zosiyanasiyana m'chinenero cha Chikhristu. Tanthauzo lake lenileni la liwu lakuti "chipulumutso" limaphatikiza zonse zimene zimachitika pamene munthu waomboledwa kuchokera m'mavuto a uchimo. Liwuli limayamba ndi ntchito ya Mulungu yakumupulumutsa munthu, kudzera mwa Yesu Khristu ndi kumalizira kuchotsa machimo. Nthawi zina mawu akuti "chipulumutso" amatanthauzidwa m'njira zambiri – chipulumutso choyamba chimatanthauza kulapa ndi kukhululukidwa kwa machimo – chipulumutso chathunthu chimatanthauza kulandira Mzimu Woyera – ndipo chipulumutso chotsiriza chimatanthauza kupita Kumwamba.

Kawirikawiri mawu akuti chipulumutso amagwiritsidwa ntchito mofanana ndi mawu akuti kukhululukidwa kwa machimo. Iyi timaitcha kuti ntchito yoyamba ya chisomo. Mawuwa amatanthauzidwa m'njira zosiyanasiyana malingana ndi kazimidwe ka munthu m'Chikhristu chake. Izi tizifotokoza mwatsatanetsatane.

Liwu lakuti "Chiyeretso" nalonso lili ndi matanthauzo ambiri.

Chiyeretsochi chinabwera pambuyo pa kupulumutsidwa chifukwa chiyeretso chimatanthauza kutsukidwa kuti munthu akhale woyera, pamene chipulumutso chimatanthauza kumasulidwa kuchokera ku uchimo. Tikamayenda ndi Mulungu m'kuyeretsedwa ndi kupulumutsidwa, zonse zimachitika m'miyoyo yathu. Ndi chifukwa chake, mawu akuti "chiyeretso choyamba" amafanana ndi liwu lakuti chipulumutso pamene munthu apulumutsidwa (akhululukidwa machimo ake). Komanso kawirikawiri Anazarene amagwiritsa ntchito liwu la chiyeretso pofotokoza za m'mene munthu amvera mumtima mwake akamayeretsedwa. Nthawi zina chimenechi timachitcha "chiyeretso chathunthu" posiyanitsa ndi "chiyeretso choyamba". Mawu ena ambiri amagwiritsidwanso ntchito mosiyanasiyana kutanthauza chiyeretso.

## Kodi Ndani Angapulumutsidwe Ndi Kuyeretsedwa?

BUKU LOPATULIKA limatiuza kuti munthu aliyense amene amakhulupirira mwa Yesu Khristu angathe kupulumutsidwa ndi kuyeretsedwa. Mulungu anatipatsa ife kusankha. Tikhoza kusankha kukhulupirira ndipo pambuyo pake timapulumutsidwa. Chipulumutso ndi chosachita kugula kapena kuti tigwirire ntchito kuti tilandire. Koma chimene tiyenera ife kuchita ndicho kukhulupirira ndi kumvera Yesu Khristu. Kukhulupirira ndi kumvera zonsezi ndikofunikira kuti tipulumutsidwe (*1 Yohane; Mateyu 11:28; Yohane 1:9; 3:17; Aroma 1:20-21; 2:14-15; Tito 2:11; 2 Petro 3:9)*.

## Kodi Ndikofunika Kwa Ife Kuti Tilape?

Kulapa ndi chinthu chofunika choyamba kwa munthu wina aliyense amene afuna kukhala mwana wa Mulungu. Kulapa kumatanthauza kuti ndazindikira kulakwa kwanga ndi machimo anga ndipo ndifuna kuzisiya zonse ndi kutembenukira kwa Mulungu. Mzimu wa Mulungu amatizindikiritsa kuti ndife ochimwa ndipo amatilimbikitsa kuti tilape. Ntchito ya Mzimu Woyerayi timaitcha chisomo cha Mulungu chopanda tsankho (*prevenient grace)*–chisomo cha Mulungu tisanapulumutsidwe. Ngati tikana chisomo chimenechi sitingalandire chipulumutso chimene Mulungu akutipatsa.

Kulapa kumaphatikizanso kukonza zochimwa zimene tazichita. Liwu lakuti kukonza *(restitution)* ndilofunika kwambiri. Liwuli limatanthauza kuti ngati kukonzaku kungatheke mwa mphamvu zanga ndiyenera kutero. Kukana kukonza zochimwazi kumasonyeza kuti ndikufunabe kupitiriza

kuchita zoipazo m'malo mozisiya. Pamene Zakeyu anatembenuka mtima atakumana ndi Yesu Khristu, nthawi yomweyo anauza anthu kuti adzakawabwezera zimene anawabera. Iye anabweza kanayi zonse zimene anaba. Izi zinasonyeza chidwi chimene anali nacho atatembenukira kwa Mulungu *(Luka 19:8).* Ambuye Yesu anamuyankha ndi kunena kuti chipulumutso chagwera m'nyumba yake.

## Kodi Chisomo Cha Mulungu Ndi Chiyani?

Chisomo cha Mulungu ndi chifuniro chake chothandiza anthu, ngakhale kuti mavuto amene timapeza amadza chifukwa cha kulakwa kwathu. Mawu ena ofanana ndi chisomo m'Buku Lopatulika ndi chifundo ndi chikondi chopanda malire.

Chisomo cha Mulungu chimagwira ntchito kumbali zonse za miyoyo yathu. CHISOMO CHA MULUNGU CHOPANDA TSANKHO *(Prevenient Grace)* ndi chimene Mulungu anafika nacho kwa ife ndi kutipulumutsa pamene tinali ochimwabe. NTCHITO YOYAMBA YA CHISOMO *(First Work of Grace)* ndi pamene machimo athu amakhululukidwa ndipo ife timalandiridwa kukhala ana a Mulungu. NTCHITO YACHIWIRI YA CHISOMO *(Second Work of Grace)* ndi imene ife timadzipereka kwathunthu kwa Mulungu ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. KUKULA M'CHISOMO *(Growth in Grace)* kumachitika nthawi zonse kwa munthu amene ayenda ndi Mulungu. Kukula m'chisomoku kumayamba pamene Mulungu alankhula nafe koyamba (Prevenient Grace). ndipo kumapitilira kufikira tsiku la kutha moyo wathu wa pansi pano. Chofunika kuchita ndicho kumvera chomwe Mzimu Woyera atiuza.

## Kodi Ndi Chifukwa Chiyani Kuli Mawu Ambiri Onena Za Ntchito Yoyamba Ya Chisomo Ofanana Matanthauzo?

Liwu lililonse lonena ntchito yoyamba ya chisomo limatithandiza kumvetsa choonadi cha chisomochi.

> **Chipulumutso** ***(Salvation)*** Chimatanthauza kuti ife tinapulumutsidwa kuchokera kuchilango chomwe chinatigwera chifukwa cha machimo athu.
>
> **Chiombolo (*Redemption*)** Kumatanthauza kuti sitingathe ife kudzipulumutsa tokha kuchoka kumachimo athu koma kumafunika Yesu kutimasula kumakhalidwe athu a uchimo.

**Kubadwanso Mwatsopano** *(Born Again)*Kumatanthauza kuti chipulumutso chimakhala ngati kuyambanso moyo wina watsopano.

**Chilungamitso** *(Justification)* Chimatanthauza kuti Yesu watikhululukira ife machimo athu amene tikanayenera kulangidwa nawo.

**Kukhala Ndi Moyo Watsopano** *(Regeneration)* Kumatanthauza kuti moyo watsopano umabweranso m'mitima mwathu pamene takhululukidwa machimo athu.

**Kukhala Ana A Mulungu** *(Adoption)* Kumatanthauza kuti Mulungu amatilandira ife kukhala ana a m'banja lake. Ife timakhalira limodzi ndi Yesu Khristu ndipo timayembekezeka kukhala ndi makhalidwe oyenera ana a m'banja la Mulungu. Mawuwa ndiwo amene amafotokoza momveka bwino za chikondi cha mtengo wapatali cha Mulungu kwa ife (onani *Aroma 8:14-17)*.

## Chifukwa Chiyani Kuli Mawu Ambiri Onena Za Ntchito Yachiwiri Ya Chisomo?

Ntchito yachiwiri ya chisomo imatsiriza zinthu zambiri zokhudza miyoyo yathu. Mawu ambiri amagwiritsidwa ntchito posiyanitsa ntchito ya chisomoyi.

**Chiyeretso** *(Holiness)* Ndi mfundo imene Mpingo wa Nazarene umakhulupirira. Mulungu amanenetsa kuti anthu ake akhale oyera monga Iye ali Woyera *(Levitiko 11:44; 1 Petro 1:16)*. Kawirikawiri chiyeretsochi timachitcha chiyeretso cha Chikhristu chifukwa chimenechi chimachokera kwa Yesu Khristu, pakuti sitingathe kudziyeretsa tokha.

**Kuyeretsedwa** *(Sanctification)* Ndi liwu limene limagwiritsidwa ntchito kawirikawiri kunena zimene timaziona. Kuyeretsedwaku kumatanthauza kusinthika kwa mtima wathu kumene kumapangidwa ndi Mzimu Woyera. Iye amatsuka mtima wakuda kukhala wangwiro ndi woyera.

**Ungwiro Wa Chikhristu** *(Christian Perfection)* Amenewa ndi mawu amene a John Wesley amawakonda kwambiri. BUKU LOPATULIKA limatiuza kawirikawiri kuti anthu a Mulungu azikhala angwiro *(Afilipi 3:15; Ahebri 13:21: 1 Petro 5:10;*

*1 Yohane 4:17)*. Zoona ndi zakuti pamene munthu ayandikira kuunika kwa Ambuye wathu Yesu Khristu, munthuyo amazindikira kuperewera kwake. Chifukwa cha ichi, timakhala ndi nthumazi tikamawerenga mawu akuti "Ungwiro wa Chikhristu". Ngakhale zili choncho mawuwa ndi ofunikira, chifukwa amationetsera poyera ndi kuti cholinga cha Mulungu amafuna ife tikhale angwiro. Bambo Wesley anagwiritsa ntchito liwu lakuti Chikhristu mwanzeru kutidziwitsa ife kuti chimenechi siungwiro wamphumphu, koma mtima wachikulu, wopanda chibwana, womwe Mkhristu weniweni akhoza kuupeza.

**Mtima Woyera** *(Heart Purity)* Mawuwa amatsimikiza kuti Mzimu Woyera amagwira ntchito m'mitima yathu kusintha makhalidwe athu.

**Chidzalo Cha Madalitso** *(The Fullness of the Blessing)* mawu amenewa amatanthauza kuti kumasuka kwathu kumphamvu ya tchimo kumene timapatsidwa kudzera m'chisomo cha Mulungu sikumapezeka konse pamene ife takhululukidwa machimo athu ndi kubadwanso mwatsopano. Madalitso okwanirawa timawalandira kwathunthu pamene tavomera kuti mwazi wa Ambuye wathu Yesu Khristu utsuka mitima yathu.

**Kufa Ku Zofuna Zathu** *(Crucifixion of the Self)* **ndi Kudzipereka Kwathunthu** *(Full Surrender)* amenewa ndi mawu amene amafotokoza m'mene ife tingagwirire ntchito za Mulungu m'miyoyo yathu. Mawuwa amatsimikiza kuti munthu wokhulupirira azipereke kwathunthu kwa Mulungu pogwira ntchito pamodzi ndi Mulungu. Paulo kawirikawiri amanena kufa kumeneku kuti "Kufa kuthupi" *(1 Akorinto 15:31; Afilipi 1:21; Agalatia 2:20; 5:24; Aroma 6:6)*. Ambuye Yesu amachitiranso umboni ponena kuti "sichimene ndifuna ine, koma chimene mufuna inu" *(Marko 14:36)*.

**Ubatizo Wa Mzimu Woyera** *(Baptism with the Holy Spirit)* mawu amenewa amatanthauza kuti ndi Mzimu Woyera amene amatsiriza ntchito yachiwiri ya chisomo ndi kukhala m'mitima yathu. Pambuyo pake timanena kuti "Tadzazidwa ndi Mzimu Woyera". Mulungu akhoza kugwira ntchito kwa anthu ena kudzera mwa ife ndipo Mulungu akhozanso kusintha mitima yathu kuti tikhale monga m'mene Iye afunira.

## Kodi Chiyeretso Chathunthu Ndi Chiyani?

Chiyeretso chenicheni ndi ntchito imene Mulungu amaigwira kwa munthu amene wadzipereka kwathunthu. Mzimu Woyera amatsuka mumtima wa Mkhristu ndipo Iye amakhala momwemo. Pambuyo pake chikondi cha Mulungu chimalamulira munthuyo. Ndipo Mkhristuyo amafuna kuchita chifuniro cha Mulungu chokha. Mtendere ndi kukhutitsidwa kwa mtima zimasefukira m'chiyanjano ndi Mulungu nthawi zonse.

Kukhala ndi Mzimu Woyera kumatanthauza kuti tili ndi mphamvu ya Mulungu kuti tikhale m'mene afunira mwini ndiponso timakhala ndi mphamvu yakukwaniritsa chifuniro chake pa miyoyo yathu. Mphamvu imeneyi ndiyotipatsa ife moyo ndi kutumikira Mulungu osati yodzionetsera.

## Kodi Tingadziwe Bwanji Za M'mene Chilili Chisomo Chathu?

Mzimu wa Mulungu ndi mzimu wathu amachitira umboni za m'mene chilili chisomo chathu *(Aroma 8:16)*. Mulungu amachitira umboni m'mitima yathu, kudzera ku BUKU LOPATULIKA, kapenanso Akhristu anzathu amatidziwitsa kudzera mu umboni wawo kuti ife tinapulumutsidwa kapena kuyeretsedwa.

## Kodi Mkhristu Woyeretsedwa Amakumananso Ndi Zoopsa Mu Uzimu?

Chiyeretso sichimamupangitsa munthu kuti akhale woposa ena onse. Munthu woyeretsedwa atha kuyesedwa ndi kugwa mu uchimo. Chiyeretso sichimamuchinjiriza munthu kuti asalakwe. Koma ngati munthu alakwa, Iye ayenera kukonza kapena kulapa zolakwazo chifukwa ngati satero ndiye kuti kulakwa kwake kumakhala tchimo. Kalekale mneneri Mika anafotokoza zimene Mulungu anali kufuna kuti munthu achite *(Mika 6:8)*. Ndondomekowu uli ndi mfundo zitatu zofunikira. Mfundozi zili motere: "uchite chilungamo", "kukonda", "chifundo" ndiponso "kuyenda modzichepetsa ndi Mulungu wako". Kudzichepetsa ndi chizindikiro cha munthu amene amayenda ndi Mulungu.

→ → → → → → →

Mutu Wachisanu

# BUKU LOPATULIKA NDILO LIMATITSOGOLERA M'MOYO WATHU

## Kodi Buku Lopatulika Ndi Chiyani?

BUKU LOPATULIKA ndilo limene limatisonyeza chifuniro cha Mulungu pazonse zofunikira za Mulungu kuti tipulumutsidwe. BUKU LOPATULIKA ndilo maziko a chiphunzitso cha umulungu *(theology)* ndi kakhalidwe ka anthu. (Zoyenera Kukhulupirira Kwa Mulungu pamfundo yachinayi IV).

**IV. Buku Lopatulika**

4. Tikhulupirira kuuziridwa kwa Buku Lopatulika ndi Mzimu Woyera, m'mene mabuku okwana 66 a Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano, amene adapatsidwa kwa ife ndi utsogoleri wa Mulungu, nationetsera chifuniro cha Mulungu pa ife pa za chipulumutso chathu, ndipo chilichonse chimene mulibe ndi chosayenera kuchikhulupiriro chathu. *Luka 24:44-47; 1 Akorinto 15:3-4; 1 Petro 1:10-12; Yohane 10:35; 2 Petro 1:20-21; 2 Timoteo 3:15-17.*

## Kodi Buku Lopatulika Ndi Mawu A Mulungu?

Inde, Buku Lopatulika ndi Mawu a Mulungu, ndiponso buku la MAWU OYERA. Munalembedwa mawu ochokera kwa Mulungu olankhula ndi anthu. Mzimu Woyera ndiye adawatsogolera anthu polemba mawu onse.

## Kodi Buku Lopatulika Ndi Lamatsenga?

BUKU LOPATULIKA silamatsenga ayi. Mulungu sapanga matsenga. Kutchula mawu ochokera m'BUKU LOPATULIKA sikumaumiriza Mulungu kuti achite zimene munthu afuna. Mulungu amachita zomwe Iye mwini afuna.

Banja lokhala ndi BUKU LOPATULIKA sindiye kuti banjalo ndi loyera ayi. Ngakhale kuyenda ndi BUKU LOPATULIKA sikutanthauza kuti munthuyo ndi woyera. BUKU LOPATULIKA likakhala m'sitolo sindiye kuti sitoloyo ikhala yoyera ayi. Kugwira BUKU LOPATULIKA pamene munthuyo akunena bodza sindiye kuti munthuyo adwala. BUKU

LOPATULIKA silamatsenga.

## Kodi Buku Lopatulika Linalembedwera Anthu?

Inde, BUKU LOPATULIKA ndi la ife anthu. Bukuli linalembedwa ndi anthu. Wolembawo amadziwika ndi kalembedwe kawo. M'Bukuli munalembedwa za madandaulo, nyimbo, nthano, malamulo ndi zina za chipangano. Mulinso, za ndondomeko za mbiri yakale ya kumabanja achifumu, mbiri yakale, maulaliki, makalata, masomphenya, miyambi, maphunziro ndi zina zambiri. Zomwe timapeza m'BUKU LOPATULIKA ndi za umunthu ndi za umulungu monga m'mene adalili Yesu Khristu.

## Kodi Buku Lopatulika Tidalipeza Bwanji?

BUKU LOPATULIKA lidalembedwa zaka pafupifupi zikwi ziwiri zapitazo. Ndikovuta kuzindikira kuti ndi mbali ziti za m'BUKU LOPATULIKA zimene zinalembedwa kale kuposa zinzake chifukwa m'BUKUMU sananene zambiri zotidziwitsa kuti linalembedwa liti, kuti, kapena ndi ndani.

Mose analemba, ndi kusonkhanitsa mabuku ena oyamba a m'BUKU LOPATULIKA. Mabuku amenewa anasungidwa mosamala ndi Aisraeli ndi Ayuda m'malo osiyanasiyana.

Timawerenga kuti BUKU LOPATULKIKA linagwiritsidwa ntchito kuposa Aneneri kapena Mkulu wa ansembe m'buku la *2 Mafumu chaputala 22.* Mfumu Yosia adali ndi chidwi mu Mawu a Mulungu pamene adamuwerengera mawu ochokera m'buku la Chipangano limene lidapezeka m'kachisi yemwe anali kumangidwanso kachiwiri.

CHIPANGANO CHAKALE chinakonzedwa katatu asanasindikize. Poyamba anasanthula ndi kuvomereza mabuku asanu omwe adalembedwa ndi Mose; mabukuwa adawatcha MALAMULO a Mulungu. Izi zinachitika panthawi imene Aisraeli anali m'chipululu.

Gawo lachiwiri m'Chipangano Chakale limene linavomerezedwa ngati Mawu a Mulungu linali la mabuku okamba za aneneri ndiponso olembedwa ndi aneneri a Mulungu (mabukuwa timawatcha mbiri yakale). Mawu akulu pamabuku onsewa ndi akuti "Atero Ambuye". Panthawi ya Ambuye Yesu mabukuwa ankawatchula kuti Mabuku a ANENERI.

Gawo lotsiliza lachitatu la Chipangano Chakale amalitcha ZOLEMBEDWA kapena MASALIMO. M'gawoli muli nthano, nyimbo

ndi miyambo. Gawo limeneli silinavomerezedwe msanga kufikira patapita zaka makumi asanu ndi limodzi kuchokera pamene Ambuye wathu Yesu Khristu anafa.

Mabuku a Chipangano Chakale anali kusungidwa ku Aigupto, ku Babulo ndi ku Yerusalemu. Mabuku amene adasungidwa ku Yerusalemu anawonongeka pamene Aroma adapasula kachisi wa ku Yerusalemuko. Koma mabuku amene anasungidwa ku Babulo ndiwo amene anasindikizidwa kuti tikhale ndi Chipangano Chakale. Mabuku amene anasungidwa ku Aigupto amene anali kuwatcha SEPTUAGINT anawatanthauzira m'chinenero cha Chigriki ndipo Akhristu oyamba a Chigriki adawagwiritsa ntchito mabukuwa ngakhale mabuku ena anali ataonjezedwa. Mpingo wa Aroma umagwiritsa ntchito mabuku a septuagint mpaka lero m'Chipangano Chakale chawo. Ndi chifukwa chake pali kusiyana pakati pa Chipangano Chakale chimene Akatolika amagwiritsira ntchito ndi Chipangano Chakale chimene mipingo ina imagwiritsira ntchito.

CHIPANGANO CHATSOPANO sichinatenge nthawi yayitali monga Chakale kuti chilembedwe. Chipangano Chatsopanochi chinalembedwa m'zaka zana (100) kuchokera pamene Ambuye wathu Yesu Khristu anafa. M'mene zakazi zimadzafika mazana anayi unasankha mabuku amene anali oyenera kukhala m'Chipangano Chatsopano. Chipangano Chatsopanochi chili ndi mauthenga abwino a (mbiri ya Yesu Khristu), makalata, mbiri ya mpingo woyamba ndi masomphenya.

## Kodi Tingasankhe Bwanji Buku Lopatulika Lotanthauzidwa Bwino?

A Bible Society amayesetsa kutanthauzira bwino Bukuli. M'chinenero cha Chingerezi anthu amavomereza kuti amene anatanthauzira Buku Lopatulika lotchedwa King James Version m'chaka cha 1611 analitanthauzira bwino. Chingerezi chimene adagwiritsa ntchito nthawi imeneyi tsopano ndi "cha makedzana". Tsopano kuli mabuku amene atanthauziridwa bwino posachedwapa monga *Revised Standard Version* (1952), *New American Standard Bible* (1960), ndi *New International Version* (1978). Mabuku onsewa anatanthauziridwa ndi mabungwe a anthu ophunzira kwambiri. Akatswiri a Mpingo wa Nazarene anathandiza kutanthauzira mabuku awiri otsiliza amene alembedwa pamwambapa.

## Kodi Buku Lopatulika Limatiuza Choonadi?

Inde, BUKU LOPATULIKA ndilo Mawu a Mulungu. Mzimu Woyera anatsogolera anthu olemba Bukuli kuti asalakwitse. Amenewa ndi mawu a chikhulupiriro. Chikhulupiriro chimenechi ndicho chofunikira umboni. Ngakhale zili choncho, m'Buku Lopatulika munalembedwa zambiri zotitsimikizira kuti Bukuli limatiuza zoona. Zitsanzo zina ndi izi:

* Anthu zikwizikwi akhala akuchitira umboni kwa zaka 2000 za choonadi cha BUKU LOPATULIKA.
* Masomphenya amene analembedwa m'Buku Lopatulika okamba za mtsogolo ambiri achitika kale.
* M'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku timaona kuti ngati timvera kapena kusamvera zomwe BUKU LOPATULIKA linena zotsatira zake zimakhala momwe BUKULI limatiuzira.

## Chifukwa Chiyani Pali Matanthauzo Ambiri A Buku Lopatulika?

BUKU LOPATULIKA limakhudza za umunthu ndiponso za Mulungu. Izi zitanthauza kuti nthawi zina likhoza kutanthauzidwa molakwika. Tiyenera kuphunzira kutanthauzira BUKU LOPATULIKA molondola osati mosokoneza ayi. Mwachitsanzo, pamene Yesu anati "Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi", sananene kuti Iye ndi kandulo kapena nyali ya mafuta kapenanso nyali ya magetsi. Yesu amatanthauza kuti choonadi chimene akubweretsa m'dziko chidzabweretsa kumvana ndi umodzi.

## Tingalimvetsetse Bwanji Buku Lopatulika?

Ndikofunika kuti Mkhristu aliyense aphunzire kumvetsetsa BUKU LOPATULIKA. Pali njira zambiri zimene tingazitsatire kuti tilimvetsetse Bukuli. Ndondomeko zimene zinalembedwa ndi a Africa Nazarene Publications zikhoza kutithandiza kuphunzira kumvetsetsa BUKU LOPATULIKA lonse kapena mabuku amene tingawasankhe kuchokera m'BUKU LOPATULIKA. Ndondomeko zina zotithandiza kuphunzira Buku Lopatulika ndi izi:

1. Tsatiramo BUKU LOPATULIKA molondola. Bukuli ndi Loyera osati mankhwala osiyanasiyana a uzimu kapena buku lamatsenga lotithandiza kuchotsa zoipa.

2. Panokha muziwerenga BUKU LOPATULIKA ndi kuphunzitsa kulimvetsetsa. Mabuku ena othandiza kumvetsetsa Bukuli alipo, koma sindiwo mlowa m'malo wa BUKU LOPATULIKA ayi.

3. Werengani nkhani yonse ya m'BUKU LOPATULIKA osati vesi limodzi lokha ayi. Nkhani imene muli vesi lanulo ndiyo yofunika kwambiri kuti inu mumvetsetse tathauzo la vesilo.

4. Santhulani nkhani imene mwawerengayo ndipo pezani nkhani yofunikira. Amvetsetseni mawu ofunikirawo.

5. Funsani mafunso. Ngati mufunsa motere: Kodi akuti chiyani? sZinachitika kuti, liti, motani? Chifukwa chiyani? Nanga ndi ndani anachita zimenezo? Mukatero mudzamvetsetsa bwino zimene mwawerenga.

6. Tanthauzirani mayankho anu. "Kodi zimenezi zikutanthauza chiyani?" Ili ndi funso loyenera kuyankhidwa pamene mukuwerenga BUKU LOPATULIKA.

7. Chongani mayankho anu. Onetsetsani kuti mfundo zomwe mwasankha zikugwirizana ndi choonadi cha m'BUKU LOPATULIKA. Ngati sizikugwirizana, muyenera kukonzanso mfundo zanu.

## Kodi Mzimu Woyera Amatithandiza Kumvetsetsa Buku Lopatulika?

Ambuye Yesu Khristu adatiuza kuti Mzimu Woyera akadzabwera, adzationgolera ku choonadi *(Yohane 16:13)*. Izi zimatanthauza kuti Mzimu Woyera adzatithandiza mothandizana ndi Ambuye Yesu yemwe ALI CHOONADI. Zimatanthauzanso kuti Mzimu Woyera adzatithandiza kumvetsetsa Mawu a Mulungu.

Kupemphera ndi kusanthula Mawu a Mulungu zimayendera limodzi. Ife tiyenera kuchita mbali yathu kuphunzira BUKU LOPATULIKA momvetsetsa bwino kuti tizindikire m'mene Mzimu Woyera angatithandize potiphunzitsa. Tiyeneranso kukhala ndi nthawi yapadera yopemphera pamene tikuwerenga Mawu a Mulungu kuti Mzimu Woyera atithandize kumvetsetsa. Choonadi chimene tingachipeze m'BUKU LOPATULIKA tiyenera kuyamba kuchigwiritsa ntchito m'miyoyo yathu. Ndipo pambuyo pake tikhoza kugwiritsa ntchito choonadi kwa anzathu mwa chikondi.

**Kodi Zonse Zolembedwa M'buku Lopatulika Ndi Zofunikira Kwa Ine?**

BUKU LOPATULIKA lonse ndi Mawu a Mulungu choncho nkoyenera kuti tililemekeze. BUKU LOPATULIKA limatiuza mosiyanasiyana malingana ndi m'mene zinthu zilili. M'buku la Miyambo timaphunzira kuti chinsinsi cha kupambana ndi kuchita bwino nthawi yoyenera. Tiyenera kusiyanitsa pakati pa choonadi cha mfundo imodzi ndi choonadi cha nthawi zonse. Choonadi monga chimene chinalembedwa pa *Eksodo 20*, cha Malamulo Khumi a Mulungu ndi choonadi cha nthawi zonse. Koma choonadi chimene chinalembedwa pa *Deuteronomo 22:8* nchakuti munthu ayenera kuika mpanda padenga la nyumba yake ndi choonadi chimene chili chomveka kwa anthu amene amamanga nyumba motero.

Choonadi china chinakhala chokhudza fuko la anthu ndipo mafuko ena sangachigwiritse ntchito. Komanso choonadi china chimakhala chokhudza mitundu yonse ya dziko lapansi. Choonadi china chimakhala chanthawi yochepa pamene china chimakhala cha nthawi zonse. Izitu ndi zoona ndipo zimakhudzanso ngakhale BUKU LOPATULIKA. Chitsanzo chabwino chofotokoza izi ndi cha chikwangwani chosonyeza kuti "imani" chimakhala cha mbali yokhayo kuli msewu umenewo koma monga chonena kuti magalimoto asamathamange kupitirira liwiro lakuti-lakuti ndi cha kulikonse. Chikwangwani chotidziwitsa kuti msewu akuukonza chimakhala cha nthawi yochepa koma chotidziwitsa kuti kuli phompho muyende pang'onopang'ono ndi chanthawi zonse.

## Kumvera Choonadi

Wina akhoza kuphunzira Mawu a Mulungu kwa nthawi yaitali koma osalimvetsetsa BUKU LOPATULIKA. Komabe mwachangu timaphunzira zoonadi zambiri. Chofunikira kwambiri ndi kumvera choonadi chimene Mzimu Woyera amatithandiza kumvetsetsa. Mwanjira imeneyi tikhoza kuyenda bwino ndi Mulungu ndi kukula m'miyoyo yathu ya uzimu. Kutsutsana ndi choonadi chimene Mulungu amationetsa zotsatira zake ndi kufa kumoyo wa uzimu.

→ → → → → → →

# ANAZARENE AMAKULA M'CHISOMO

## Mzimu Woyera Amatithandiza Kukula M'chisomo

Umoyo wa Chikhristu sumakhala pamodzimodzi ayi. Nthawi zonse timakhala ndi mwayi wosankha. Ngati tisankha kuchita bwino, chotsatira chake tidzakula muuzimu. Koma ngati tisankha kuchita choipa, timachoka m'manja mwa Mulungu. Mzimu Woyera anaperekedwa kuti azithandiza kusankha moyenera. Mzimu Woyera akhoza kugwira ntchito mwa ife makamaka ngati machimo athu anakhululukidwa ndi kumalola Mzimuyo kulamulira miyoyo yathu. Timakula koposa tikayeretsedwa.

## Kodi Kukula Muuzimu Ndi Chiyani?

Kukula muuzimu ndi kusinthika kwa ubwino m'makhalidwe athu pamaso pa Mulungu ndiponso anzathu. Mulungu amafuna kuti ndikhale wabwino mu umunthu wanga osati chifukwa cha kuopa kulondedwa. Zipatso za moyo wanga wa uzimu zimaonetsa m'mene ndikukulira muuzimu.

## Kodi Kukhala Wamkulu Muuzimu Ndi Kutani?

Yesu anati, "Koma amene aliyense akafuna kukhala wamkulu mwa inu, adzakhala mtumiki wanu" *(Mateyu 20:26)*. Pa *Afilipi 2:1-11* timawerenga kuti Yesu anadza kuchokera Kumwamba kudzakhala mtumiki. Yesu anatipempha ife kuti tikhale ngati Iye. Mtumiki wabwino amayesetsa kuti amene akuwatumikira awachitire zabwino koposa. Bambo Mazithulele analemba kuti: "Udindo wanga woyamba ndi kuthandiza mnzanga kuti akhale wopambana."

## Kodi Kutumikira Kumatanthauza Kuti Anthu Ena Alamulire Miyoyo Yathu?

Tiyenera kukhala otsogozedwa ndi Mzimu Woyera osati ndi anthu ena. Yesu amafuna kuti tizifunafuna ubwino wa anthu ena. Ili ndilo tanthauzo la "chikondi" chomwe chinalembedwa ku *I Akorinto 13.* Ambuye Yesu amatiuzanso kuti ife sindife akapolo koma abwenzi chifukwa Iye anatiuza zolinga zake zonse *(Yohane 15:15)*. Ife tiyenera kugwiritsa ntchito mphatso zimene tinapatsidwa. Uku ndi kugwira ntchito

limodzi ndi Mulungu. Zimenezi zimatithandiza ife kumvetsetsa kuti kutumikira kumene Yesu ankanena sikuchita chinthu chifukwa chakuti talamulidwa kutero koma kuti ndi makhalidwe othandiza anzathu amene tayandikana nawo.

## Kodi Ndingakule Bwanji M'chisomo?

Mulungu amafuna kuti ife timudziwe kotero kuti Iye akhoza kutiyang'anira *(Masalimo 32:8)*. Mzimu adzatithandiza ife kuti tikhale ndi ubale wotere ndi Mulungu. Mzimu Woyera amatithandiza kukula modzisunga ndi kutiongolera.

KUDZISUNGA *(Discipline)* kumatanthauza kudzimana pazofuna zanga. Pali zinthu zina zimene ndikhoza kudzimana pakusankha moyenera. Palinso zinthu zina zimene sindikhoza kudziletsa koma Mzimu Woyera amandithandiza kudziletsa. Izi zitanthauza kuti m'makhalidwe athu tiyenera kulola mphamvu monga ya mapemphero, kuwerenga Buku Lopatulika, kusonkhana pamodzi ndi anthu a mumpingo kuti zimenezi zizitithandiza pamoyo wathu. Kudzisunga kumatanthauzanso kuti zimene zingawononge miyoyo yathu tiyenera kuzipewa. Tiyenera kupewa choyipa, zosangalatsa zomwe zingatitengere kutchimo kapenanso mabuku oyipa. Tiyenera kusankha abwenzi athu mosamala. Tiyeneranso kupewa kumwa mankhwala osokoneza bongo, kapena pokhapokha ngati dokotala atatiuza kuti tizimwa. Kutchuka kwa mankhwala monga mowa ndi fodya sizitanthauza kuti ndi zovomerezeka. Ndipo Mzimu Woyera yekha ndi amene angatithandize ife kudziletsa.

KUDZISUNGA *(Discipline)* kumatanthauza kungoleka maganizo athu ndi machitidwe athu. Mtumwi Paulo akutikumbutsa kuti tiyenera kukhala ndi Mzimu Woyera nthawi zonse kuti tikhoze kupewa dama *(1 Atesalonika 4:3)*. Yakobo akutikumbutsanso kuti popanda Mzimu Woyera sitingathe kulilamulira lilime lathu *(Yakobo 3)*. Lamulo la Mulungu limatitsogolera ndipo chikondi chake chokhala m'mitima yathu chimatipatsa ife chilakolako chosunga malamulo ake. Mzimu Woyera amatithandiza ife kudzisunga kumaganizo ndi machitidwe athu ndi kutithandiza kusankha moyenera.

KUDZISUNGA *(Discipline)* kutanthauza kuti Mulungu akufuna kuti ife titenge mbali pa zochita zomwe zingakuze miyoyo yathu ndi

ya anthu ena.

Machitidwe amathandiza kuchotsa mzimu wotsutsa. Ndipo Mzimu Woyera safuna kuti muzu wa zoipa uphuke m'miyoyo yathu *(Ahebri 12:15)*.

## Ndingagwire Bwanji Ntchito Ndi Mzimu Woyera?

Pali zinthu ziwiri zomwe ndiyenera kuchita kuti Mzimu Woyera agwire bwino ntchito yake m'moyo wanga pambuyo populumutsidwa ndi kuyeretsedwa. Choyamba ndicho kukhala ndi nthawi yopemphera ndi kuphunzira Buku Lopatulika ndipo chachiwiri ndicho kutsimikiza kuti ndikukhala monga chiwalo cha Thupi la Khristu, chomwe ndi Mpingo.

## Chifukwa Chiyani Ndiyenera Kupemphera Ndi Kuwerenga Buku Lopatulika?

Pemphero ndi kuphunzira Buku Lopatulika ndi zogwirizana. Timaphunzira za m'Buku Lopatulika kuti timve Mulungu akulankhula nafe. Kupemphera ndiko kulankhula ndi Mulungu.

Pemphero lili m'mitundu isanu - Kutamanda, kuthokoza, kuvomereza, kupembedzera ndi kupempha. Mulungu ndi woyenera KUTAMANDIDWA chifukwa ndi wabwino ndi wachifundo. KUTHOKOZA kukhale kochokera mumtima osati kungolankhula chabe. Tikulimbikitsidwa kuti tikhale othokoza nthawi zonse *(1 Atesalonika 5:18)*. TIMAVOMEREZA machimo athu pamene tipempha Ambuye kuti atipulumutse ndi kutiyeretsa. Tiyeneranso KUVOMEREZA pamene tachimwa kapena kulakwira anzathu. Mulungu satichotsa ife m'banja lake, koma ngati ife tionetsabe mtima wosagonja, tidzazilekanitsa tokha ndi Mulungu. PEMBEDZERO ndilo pemphero lomwe timapemphera m'malo mwa anthu ena. Pemphero LOPEMPHA ndi limene timamupempha Mulungu kuti atipatse zosowa zathu. Mulungu akutiuza ife motsimikiza kuti tipemphe. Ndi Mulungu wachifundo ndi wopatsa komanso ndi amene amadana ndi kudzikonda ndi umbombo.

## Kodi Kupempha M'dzina La Yesu Kumatanthauza Chiyani?

Mawu onena kuti, "m'dzina la Yesu" sali ngati matsenga omuumirizira Mulungu kuti achite zimene anthu akufuna. Pemphero limathandiza munthu kuti alinganize maganizo ndi chifuniro chake monga afunira Mulungu. Yesu anati, "Kufuna kwanu kuchitidwe" osati "Muchite

chifuniro changa Mulungu." Pa *Yohane 14:14* akuti, Ngati mudzapempha kanthu m'dzina langa, ndidzachita." Mawuwa atanthauza kuti ngati tipempha mogwirizana ndi m'mene amachitira Yesu (M'dzina lake) adzachita. Yesu sadzachita choyipa kapena cholakwa kwa munthu amene apempha m'dzina lake. Ngati titamvetsetsa m'mene Yesu amafunira, ndi kukhala ndi moyo wofanana naye, tikatero timapempha "m'dzina lake."

## Mzimu Woyera Amatitsogolera Kupyolera M'thupi La Khristu

Mpingo ndiwo thupi la Khristu. Mwa chitsanzo, nkono sungagwire ntchito paokha ngati utadulidwa kuchoka kuthupi, chimodzimodzinso Mkhristu sangakhale payekha kulekana ndi Akhristu ena. Kukhala chiwalo cha thupi kutanthauza kuti timapembedza, kuphunzira, kupemphera pamodzi ndi anzathu. Thupi limathandiza ndi kulimbikitsa chiwalo chilichonse koma zonse ziyenera kugwirira ntchito pamodzi. Chiwalo chimodzi chikapweteka, thupi lonse limamva ululu. Komanso pamene chiwalo chimodzi chikhala ndi mphamvu, thupi lonse limalimbikitsidwa.

Mzimu Woyera anapereka mphatso kwa aliyense mumpingo kuti tithandizane wina ndi mnzake *(Aefeso 4:12)*. Paulo anagwiritsa ntchito mphatso yake ya ulamuliro pomanga mpingo *(2 Akorinto 10:8)*. Ngati sitilabadira zimene anthu omwe ali ndi mphatso ya mzimu yotithandiza, monga abusa ndi atsogoleri ndiye kuti tikukana kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

## Kodi Masakaramenti A Mpingo Ndi Chiyani?

Pali zinthu ziwiri zomwe zimachita m'thupi la Khristu zomwe timazitchula kuti masakaramenti. Izi ndi zizindikiro zopatulika. Izi sizikutanthauza kuti masakaramentiwa ali ndi mphamvu ya matsenga. Sitingapulumutsidwe chifukwa chochita izi. Masakaramentiwa ndi Mgonero wa Ambuye ndiponso Ubatizo.

> MGONERO ndi chikumbutso cha moyo ndi ntchito ya Yesu. Aliyense wolapadi ndi kumukonda Yesu molemekeza adye mkate ndi kumwera chikho zomwe zimatikumbutsa moyo wake ndi imfa yake *(1 Akorinto 11)*. Mu Mpingo wa Nazarene tiyenera kulandira mgonero kamodzi pa miyezi itatu iliyonse.
>
> UBATIZO siupulumutsa munthu. Yesu anabatizidwa ndi

Yohane m'madzi. Akutilamulira kuti tibatizidwe monga chizindikiro choti ndife otsatira ake. Munthu yemwe wabatizidwa adzapita Kumwamba pokhapokha ngati wavomereza Yesu monga Mpulumutsi wake. Buku Lopatulika silinena kuti ubatizo weniweni ndi uti, choncho timavomereza njira iliyonse yobatizira kaya ndi ubatizo wowaza madzi, wokhuthulira kapena womiza. Ubatizo womiza ndi womwe umadziwika kwambiri. Sitikana ubatizo wa ana chifukwa BUKU LOPATULIKA silikaniza ubatizowu. Ubatizo supulumutsa mwana aliyense, koma umangotanthauza kuti makolo akufunitsitsa kumulera mwana wawo kuti atsatire Khristu. Nthawi zambiri timampereka mwana kwa Ambuye.

## Kodi Mulungu Amaitana Mkhristu Aliyense Wodzipereka Kuti Amutumikire Kunthawi Zonse?

Inde, Yesu amaitana Mkhristu aliyense kuti amutsatire. Akufuna ife tifanane naye ndi kuchita chifuniro chake. Yesu amanenanso kuti ife tonse ndife mboni kuntchito yomwe waigwira m'miyoyo yathu. Saitana munthu aliyense kuti akhale mlaliki, wamishoni kapena mlaliki woyendayenda.

MBONI. *Machitidwe 1:8* amanena kuti ophunzira adzakhala mboni. Kukhala mboni kumatanthauza kuuza ena zomwe ukuzidziwa. Miyoyo yathu ndi mawu athu zidzachitira umboni za chikondi cha Mulungu ndi zomwe anachita posintha miyoyo yathu.

KUITANIDWA KUTI TIKALALIKIRE. Mulungu amaika kuitana m'mitima ndi kuti zina zonse zikhale zachiwiri ndi kudzipereka tokha pofalitsa Uthenga Wabwino. Kwa oterewa, amawapatsa mphatso ndi chisomo zosiyanasiyana. Amayembekeza kuti tivomereze kuitanaku ndi kukonzekera kuti tikwaniritse maitanidwe.

KUITANIDWA KUNTCHITO YA MISHONI. Mulungu amaika m'mitima ndi m'maganizo mwa antnu ambiri powaitana kuti akamtumikire popita ndi Uthenga Wabwino kwa anthu a mitundu ina ndi malo osiyanasiyana. Anthu otere akhoza kutumikira muntchito zosiyanasiyana malinga ndi kusowa kwa anthu ogwira ntchitozo. Ayenera kukonzekera mokwanira kuti akagwire ntchito yotereyi. Akhristu athu amalimbikitsidwa kuti azivomera kugwira ntchito yotereyi yomwe imathandiza kuti ntchito yofalitsa uthenga wabwino ikwaniritsidwe *(Mateyu 28:19-20)*.

## Kodi Akhristu Oyeretsedwa Amapezana Ndi Mavuto?

Inde, Yesu anawapempherera ophunzira ake *(Yohane 17)* kumpempha Mulungu kuti atisunge pamene tikukhala padziko lapansi, koma sanatiphimbe kuzovuta za padziko lapansi. Yesu analonjeza kuti zosowa zathu za tsiku ndi tsiku zidzakwaniritsidwa tikafuna Ufumu Wakumwamba choyamba *(Mateyu 6:33)*. Adatipanga kukhala oyang'anira. Sanatilonjeze kuti tidzakhala achuma. Satinyengelera ndi chuma, umoyo wabwino, kapena mphamvu kuti tikhale otsatira ake.

Mzimu Woyera akakhala nafe timakhala ndi mtendere ndi chimwemwe. Uwu ndiwo moyo wabwino. Tikamasamalira malamulo a Mulungu timakhala ndi umoyo wabwino, koma Mulungu analonjeza kuti adzatisunga kuti tisakhale ndi mzimu woyipa tikapezana ndi mavuto. Anaika madokotala oti atithandize. Nthawi zina Iye amawakhudza anthu m'njira yodabwitsa. Timakhulupilira kuti ndi kulakwa kufuna machiritso m'matsenga, monga kwa sing'anga. Ngati timvera Mulungu, adzagwiritsa ntchito mavuto omwe timakumana nawo kuti atilimbikitse m'miyoyo yathu ndi kulimbikitsanso ena.

→ → → → → → →

## Mutu Wachisanu Ndi Chiwiri

# KUONA ZOKHUDZANA NDI MOYO

Tili m'dziko lovuta lomwe timachitirana zinthu zosiyanasiyana ndi anthu amene satumikira Mulungu, ndi enanso amene amalimbana naye. BUKU LOPATULIKA limatitsogolera pa zinthu zomwe timakumana nazo.

### Malamulo A Mulungu Ndi Otani Pa Moyo Wa Munthu?

Yesu ananena mwachidule za malamulo motere: "Udzikonda Ambuye wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndipo uzikonda mnzako monga m'mene udzikondera iwe mwini." Pa malamulo awiri amenewa pali Lamulo lathunthu la Aneneri *(Mateyu 22:37-40)*. Mtumwi Paulo akutipatsa phunziro labwino patanthauzo la chikondi pa *I Akorinto 13*. Chikondi ndi lamulo limene limatsimikizira malamulo a Mulungu. Malamulo Khumi a pa *Eksodo 20* ndi chidule cha malamulo a Mulungu.

### Kodi Mkhristu Ayenera Kusunga Malamulo A Mulungu?

Inde, malamulo amene Mulungu anapereka ndi otitsogolera ndi kutithandiza pokumana ndi zovuta za tsiku ndi tsiku. Yesu anadza kuti chikondi cha Mulungu ndi maziko a malamulo, zikhale m'mitima yathu. Amatisintha ife kukhala anthu ofunika kuyenda m'njira ya Mulungu. Poonetsetsa za Malamulo Khumi, timaona kuti amatithandiza pa mavuto a masiku ano.

### Usakhale Nayo Milungu Ina

Ambuye yekha ndi Mulungu. Ayenera kukhala patsogolo kuposa banja, dziko kapenanso zinthu mathu. Iye yekha ndiye woyenera kumpembedza. Chizolowezi chomwe timakhala nacho chofuna kudziteteza ndi zida, chuma kapena mphamvu ndi choipa. Ndi Iye yekha angatiteteze, kutipatsa mphamvu ndi moyo.

### Osapanga Mafano

Mafano ndi zifanizo zopangidwa zinali zinthu zimene anthu ankagwiritsa ntchito popempha milungu yawo kuti iwachitire zofuna

zawo, kapena kumpangira Mulungu malire molingana ndi m'mene iwo amadziwira. Mulungu akunena kuti kumeneku ndi kulakwa. Palibe matsenga amene angamuumirize Mulungu kuchita zimene anthu akufuna kuti achite. Munthu sangamupangire Mulungu malire. Tikamapempherera "oyera mtima" (*saints*) kuti iwo atipempherere kwa mizimu, kumenekonso ndi kupembedza mafano. Kupembedza mizimu ya makolo ndi kukhulupirira kuti ikhoza kutithandiza zimene tisowa. Mulungu amene amanena kuti kumeneku ndikulakwa. Sikulakwa kuwakumbukira anthu ndi kuphunzira zina pazomwe anachita, koma sitingawagwiritse ntchito kuti atichitire zina ndi zina kwa Mulungu.

## Musatchule Dzina La Mulungu Pachabe

Mulungu ndi woyenera kumulemekeza. Dzina lake tisamangolitchulatchula. Sitiyenera kutemberera. Ndi kulakwa kwakukulu kunena kuti "Mulungu wandiuza kuti ndichite izi", pamene tikungonena zomwe tikufuna. Zomwe amachita anthu pogwiritsa ntchito dzina la Mulungu sizilemekeza Mulungu.

UFITI ndi zomwe zimachitika pofuna kulamulira mphamvu ya Mulungu kapena munthu pogwiritsa ntchito "mphamvu ya mizimu". Izi ndi zoyipa, palibe kanthu kaya ndi zozitchinjirizira kapena zochitira ena zoyipa. Mawu a Mulungu amanena momveka kuti, Iye amatsutsa ufiti (wosamalira mitambo, wosamalira kulira kwa mbalame, wanyanga, wotsirika, wobwebweta, wopenduza, wofunsira akufa, alosi) wa mtundu wina uliwonse *(Eksodo 22:18, Deuteronomo 18:10, Mika 5:12, Agalatiya 5:20)*. Uku ndikulakwira Mulungu. Wokhulupirira mphamvu ya Mulungu asamaopsedwe ndi zinthu zotero.

## Muzikumbukira Tsiku La Sabata Kuti Likhale Lopatulika

Buku la *Ahebri* limafotokoza kufunika kwa Sabata kwa Akhristu. Sabata ndi chizindikiro cha chikhulupiliro chathu mwa Mulungu kuti akhoza kutipulumutsa kwathunthu. M'buku la *Ahebri* mitu 3 ndi 4 imafotokoza kuti sitikhala okwanira pokhapokha pamene tayeretsedwa. Ndipokhapo pamene timaona mpumulo umene Mulungu amafuna kuti anthu ake audziwe. Izi zikutanthauza kuti lamulo lachinayi lingawerengedwe motere, "Muzikumbukira kupereka moyo wanu kwa Mulungu kukulola kuti Mzimu wake akuyeretseni."

Sabata ndi tsikunso la chizindikiro lomwe linaikidwa kuti

tizilemekeza Mulungu. Ndi tsiku lolemekeza ndi kuphunzitsa za Mulungu. Yesu anati tsikuli linapangiridwa munthu *(Marko 2:27)*. Iye anatinso limeneli ndi tsiku lochita zabwino *(Mateyu 12:12)*. Akhristu a masiku ano analisintha tsikuli kuchoka pa tsiku Loweruka kufika patsiku Lamulungu chifukwa chakuti ndi tsiku limene Yesu anauka kwa akufa, tsiku lapadera lokondwerera kuuka kwa Ambuye Yesu. Tiyenera kusunga tsikuli polemekeza Mulungu pakuphunzira za Iye.

## Lemekeza Atate Wako Ndi Amako

Kulemekeza akuluakulu athu kumapangitsa kuti anthu akhale okhazikika ndi opirira. Kusalemekeza kumasokoneza zinthu. Ngakhale m'Malamulo, Mulungu akufotokoza izi pogwiritsa ntchito kulemekeza kumeneku ndi kutalika kwa "masiku amene Mulungu anatipatsa kuti tikakhale m'dzikolo" *(Eksodo 20:12)*.

## Usaphe

Yesu akutifotokozera pa *Mateyu 5:21* kuti chiyambi cha kupha ndi udani. Ngati titasunga udani pa lamuloli mpaka kalekale, ndiye kuti sitiyenera kukhala ndi udani. Izi zingatheke pokhapokha ngati titalola Mzimu wa Mulungu kutisambitsa m'mitima yathu ndi kutidzaza ndi chikondi chake.

## Usachite Chigololo

CHIGOLOLO NDI CHIWEREWERE. Pa *Mateyu 5:27-32* Yesu akutifotokozera kuti chigololo chimayamba ndi chilakolako ndipo tizipewa zinthu zotere. Paulo akutikumbutsa ife (pa *1 Atesalonika 4:3)* kuti tiyenera kuyeretsedwa kuti chilakolako chathu cha dama chigwirizane ndi chifuniro cha Mulungu.

KUSUDZULA NDI MITALA. BUKU LOPATULIKA limanena kuti ukwati ndi wopatulika, "Ine, ndimadana ndi kupasuka kwa ukwati" anatero Ambuye *(Malaki 2:16)*. Ukwati umalumikiza mwamuna ndi mkazi kukhala amodzi (*Marko 10:8)*. Izi zikutanthauza kuti sichikonzero cha Mulungu kuti munthu akhale ndi akazi oposa m'modzi. Ndi chifukwa chake Mpingo wa Nazarene umakaniratu za kusudzulana ngakhalenso mitala. (*Manual* ndime 34)

**B. Ukwati Ndi Kulekana**

**34.** Banja Lachikhristu, lamangika pamodzi kupyolera mwa Yesu

Khristu, ndi pakati pa chikondi, chiyanjano, ndi kupembedza chifukwa tili kukhala m'dziko limene maanja amapasuka msanga komanso mosavuta. Ndipo tikulimbikitsa abusa ndi anthu onse a mpingo wathu kuti aphunzitse ndi kupereka chitsanzo choyenera chimene chingathe kulimbikitsa maanja a anthu ena. Ukwati unakhazikitsidwa ndi kudzozedwa ndi Mulungu panthawi imene munthu anali asanachimwe, ndipo malinga ndi uphungu wa Atumwi, wonena kuti "ukwati ndi wolemekezeka m'zonse" ndipo uli mwa anthu awiri mwamuna m'modzi mkazi m'modzi m'chiyanjano ndi kuthandizana kwawo ndi kupitiriza kuchulukitsa mtundu wa anthu. Anthu athu ayenera kusamalira chinthu ichi choyera monga iwo ali Akhristu, ndipo ayenera kukwatira kapena kukwatiwa ali Akhristu, ndipo ayenera kukwatira kapena kukwatiwa atapemphera ndi mtima wonse kolimba kuti Mulungu awatsogolere, ndipo ndi okwanitsidwa kuti kukwatirana kwawo nkoyenera ndi zofunikira pa za uzimu. Ayeneranso kufunafuna madalitso amene Mulungu anakhazikitsa ndi kuwadzodza monga, chiyanjano chawo pamodzi, kukhala makolo ndi kukondana kwenikweni ndi kumanga banja lawo pamodzi. Pangano la ukwati limakhalabe lomangika pa iwo awiri ngati onse awiri ali ndi moyo, ndipo chifukwa cha ichi awiriwo asalekane. *(Genesis 1:26-28, 31; 2:21-24; Malaki 2:13-16; Mateyu 19:3-9; Yohane 2:1-11; Aefeso 5:21-6:4; 1 Atesalonika 4:3-8; Ahebri 13:4)*

BANJA. Ukwati uyenera kupanga banja la chikondi, lotetezedwa momwe muli mwamuna, mkazi ndi ana. Amuna amalangizidwa kuti azikonda ndi kusamalira akazi awo *(Aefeso 5:25)*. Akazi ayenera kulemekeza amuna awo *(Aefeso 5:33)*. Ana aziphunzitsidwa kumvera *(Aefeso 6:1)*.

KUTAYA PATHUPI. Mpingo wa Nazarene umazindikira kuti nthawi zina pamakhala mavuto omwe amafunika kuti munthu ataye pathupi, koma tikutsutsa zotaya pathupi monga njira yoti munthu asadziwike kuti anali ndi pathupi. (*Manual* ndime 35)

### C. Kutaya Pathupi

35. Tikukhulupilira kuti kutaya pathupi kungathe kuchitika pokhapokha pamene pali chifukwa choyenera, ngati odziwa za mankhwala (dokotala) ataona kuti maiyo kapena mwana wosabadwayo angaone vuto pamoyo wake. Koma ife tikuletsa kutaya pathupi chifukwa cha kuchepetsa mtundu. Ife

tikutsutsanso malamulo amene amalola kuti pathupi padzitayidwa ngati munthu wamkazi afuna kuchita izi popanda chifukwa chenicheni. Pakhoza kukhala mimba zina zimene zingathe kuchotsedwa molingana ndi malangizo oyenera a dokotala, koma zimenezi ziyenera kuchitika molingana ndi ulangizi wokwanira bwino wa anthu odziwa za mankhwala ndi iwo amene ali ndi udindo woyang'anira mpingo. *Eksodo 20:13; Yobu 31:15; Salimo 139:3-16; Yesaya 49:5; Luka 1:31, 41-44; Aroma 12:1-2.*

KUKHALIRA PAMODZI (KUCHITA DAMA KWA ANTHU OFANANA, MWAMUNA NDI MWAMUNA KAPENA MKAZI NDI MKAZI. BUKU LOPATULIKA limatsutsana ndi njira iliyonse ya dama yomwe ndi yosaloledwa *(Aroma 1:26, 27)*. Zoterezi ndi zosiyana kwambiri ndi Chikhristu ndipo zimadzetsa mkwiyo wa Mulungu. (*Manual* ndime 36).

**D. Chigololo Pakati Pa Amuna (Kapena Akazi) Okhaokha**

**36.** Ife tidziwa bwino lomwe zomwe zipangitsa kuti amuna (kapena akazi) azichita chigololo, koma pakutsimikizadi monga m'mene Buku Lopatulika likutiphunzitsira pakuchita mchitidwe wa tchimo limeneli zimadzutsa mkwiyo wa Mulungu. Tikukhulupirira kuti chisomo cha Mulungu chili chokwanira kuti mchitidwe wa tchimo limeneli tiulewe *(1 Akorinto 6:9-11)*. Ife tikuletsa mchitidwe uliwonse kapena kunena chilichonse chimene sichimasiyanitsa pakati pa makhalidwe a Chikhristu ndi chigololo cha amuna (kapena akazi) okhaokha. Ndipo tikulimbikitsa kuti tiyenera kulalikira poyera za chiphunzitso cha Buku Lopatulika pa zinthu zimenezi. *(Genesis 1:27; 19:1-25; Levitiko 20:13; 1 Akorinto 6:9-11; Aroma 1:26-27; 1 Timoteo 1:8-10.)*

KUWERENGA NDI KUONA ZITHUNZI ZOLAULA. Ife timatsutsa kwambiri makhalidwe osokoneza omwe anthu, makamaka achinyamata, amachita. Makhalidwewa ali monga kuonera kanena, wa zithunzi zosayenera, kuwerenga mabuku omwe ndi nkhani zolaula.

## Usabe.

Ndikosatheka kukhala Mkhristu nkukhalanso wakuba, kaya ndi kuthyola nyumba kapena kuchita chinyengo. Mulungu amafuna anthu ake azikhala oona.

## Usachite Umboni Wonama

Yesu anati, "'Inde' wanu akhale 'inde' ndipo 'ayi' wanu akhale 'ayi' zina zonse ndi za Satana" *(Mateyu 5:37)*. Kuona mtima kuzikhala kwenikweni. Akhristu azinena zoona. Asamanene bodza, miseche, kapena chinyengo. Ndi Mzimu Woyera yekha amene angalisunge lilime *(Yakobo 3)*.

## Usasilire

Kusilira ndiko kulakalaka kanthu kena koma kali kamwini. Uku ndiko kutsutsana ndi utumiki. Mtumiki weniweni amafuna kuthandiza ena osati kuwatengera. Kusilira kumachotsa ulemu, banja limawonongeka komanso miyoyo. Mzimu Woyera akufuna kutithandiza kuti tikhale atumiki osati anthu osilira.

## Mitu Ina Yomwe Mpingo Ukunena

UFULU WA MUNTHU. Timakhulupilira kuti ufulu wa ndale ndi chipembedzo zonse zimachokera m'Buku Lopatulika palamulo lonena za munthu ndi m'mene angakhalire. Timalimbikitsa anthu athu kuti azimvera malamulo a dziko lawo ndi malamulo a m'Buku Lopatulikali (*Manual* ndime 904.5 timawerenga kuti:)

**904.5.** Ife, pa Msonkhano Waukulu wa chiwerengero cha khumi ndi chisanu ndi chitatu wa Mpingo wa Nazarene, tikulakalaka ndi kutsimikiza kupitiriza kusamalira chomwe tidalandira ndi kutengera kumpatuko kuti zizisamalidwa ndi kusungidwa ndi kumvetsa bwino, ndi kukumbutsa anthu athu kuti zonse pamodzi, ufulu wa ndale ndi mpingo zakhazikika malinga ndi Buku Lopatulika pachikhazikitso cha munthu monga zolengedwa ndi Mulungu pamodzi ndi chiyero cha chikumbumtima cha aliyense. Tikukhulupirira kuti malo a mpingo ndiko kunenera ndi cholinga chokumbutsa anthu kuti "chilungamo chikuza mtundu" (1972).

KUPANGA MIPINGO YA CHIYERETSO. M'zaka zapitazo, mipingo yoposa khumi ndi isanu ndi umodzi (16) yakhala ikugwirizana ndi kukhala mpingo umodzi wotchedwa Nazarene. Dokotala Phineas F. Bresee wa ku Los Angeles, California ku America anali m'modzi wa atsogoleri amenewa anakhazikitsa Mpingo wa Nazarenewu.

MAPHUNZIRO. Timakhulupilira kuti aliyense ayenera kuphunzira. Maphunziro a anthu onse ayenera kuthandizidwa ndi maphunziro omwe ali a Chikhristu kunyumba ndi kumpingo. (*Manual* 32.5).

MITUNDU NDI TSANKHO. Timakhulupilira kuti Mulungu analenga anthu onse ndi magazi amodzi. Anthu onse ayenera kukhala ofanana pachilamulo, maphunziro ndi mwayi wa ntchito. Mamembala a Mpingo wa Nazarene akhoza kupembedza tchalitchi lina lililonse la Nazarene mosaganizira za mtundu kapena khungu. (*Manual* ndime 904.3).

MANKHWALA OSOKONEZA BONGO. Sitigwiritsa ntchito mankhwala osokoneza bongo, koma mankhwala okhawo amene anganene dokotala kuti ndi oyenera. Timatsutsa kulima, kusamalira zogwiritsa ntchito, kapena kugulitsa fodya ndi mowa poti zimenezi ndi zosokoneza bongo. (*Manual* 33.5, 6).

33.5. Zakumwa zoledzeretsa ndi kuzigwiritsa ntchito pakuzigulitsa kapena pakuitanira ena, kapena pakupereka chilolezo pogulitsira zinthu zoterezo; kapena mankhwala oletsedwa monga chamba ndi kugulitsa; kugwiritsa ntchito fodya; kulima, mwanjira ina iliyonse, kapena kugulitsa (904.4). Malembo Oyera (Buku Lopatulika) ndi kakhalidwe ka miyoyo ya anthu zikuchitira umboni kuti kumwa zinthu zoledzeretsa ndi kuchimwira Mulungu pamodzi ndi mtundu wa anthu.Lamulo la Chikhristu kwa aliyense likhale lopewa kugwira kapena kumwa zoledzeretsazi. (Muone English *Manual*) *Miyambo 20:1; kuyambira 23:29 mpaka 24:2; Habakuku 2:5; 1 Akorinto 6:9-12, 19-20; Agalatiya 5:21; Aefeso 5:18).*

(Vinyo popanda zosakanizira ndi mkate wopanda chotupitsa ndizo ziyenera pa Mgonero wa Ambuye.) [115.10, 103.6, 404, 802]

33.6. Kugwiritsa ntchito zinthu zosokoneza bongo, ndi zoledzeretsa zina, zogonetsa ndi kugwiritsa ntchito mosayenera mankhwala olamulidwa. Koma mankhwala amene ali ndi malangizo oyenera tiyenera kuwagwiritsa ntchito moyenera. *(Mateyu 22:37-39; 27:34; 1 Akorinto 6:19-20; 9:24-27; Aroma 12:1-2).*

JUGA NDI MASEWERA A MWAYI. Muziyesa kukana moyo

uliwonse umene Mulungu safuna kuti anthu ake azikhala. Ife timatsutsa zimenezi. (*Manual* 33.2)

ZOSANGALATSA. Anazarene azionetsetsa ndi kusankha zosangalatsa, zomwe zina mwa izo ndi zowerengawerenga, ndi kupita ku madansi, ndi zina zotere. Tisamalole zinthu zoipa kukhala m'nyumba mwathu (*Manual* 33.1).

33. Ife tikulimbikitsa kuti zimene tazilemba pano ziyenera kupewedwa kotheratu.

33.1. Zosangalatsa zimene zikutsutsana ndi chikhalidwe cha Chikhristu. Akhristu athu ayenera kudzisunga mwanjira zitatu. Choyamba ndiko kukhala mtumiki wa Khristu panthawi yopuma. Chachiwiri ndiko kudziwa kukhala ndi makhalidwe oyenera Chikhristu chathu m'banja mwathu. Pakuti tili kukhala m'nthawi ya zosokoneza zambiri zimene zingathe kutilepheretsa Chikhristu m'maanja mwathu mwanjira zosiyana monga mabuku ena, mawayilesi omvera mawu ndi mawayilesi a kanema, ndipo nkofunikadi kukhala ndi malamulo okhwima kuti tipewe zinthu zotere. Chachitatu ndicho kudziletsa tokha kumakhalidwe oipa otisangalatsa kapena kuzotikopa ndi kutifunitsa kuchita zoyipa, kuti ife tidzikanize tokha, tiyenera kupeza zina zabwino zoyenera m'malo mwa zoyipazo. Zina zimene tiyenera kupewa ndi kuonera kanema ndi zina zoitanitsira malonda, ndi zina zolaula, ndi zionetsero zina zoipa zimene ziletsa chikhalidwe choyera cha Mulungu m'moyo ndi m'mitima ya anthu. [904.9] *(Aroma 14:7-13; Aefeso 5:1-18; 1 Akorinto 10:31-33; Afilipi 4:8-9; 1 Petro 1:13-17.*

MPINGO NDI BOMA. Mulungu anakonza kuti boma lizikonza malamulo ndi zoti anthu azikhala bwino. Ndi udindo wa Anazarene "kupereka kwa Kaisara" zomwe ndi zake. Komanso ndi udindo wathu wa ife Anazarene kumvera boma. (*Manual* 904.2, 5.)

MPINGO NDI KUSINTHA. Sitivomereza mchitidwe woukira pofuna kudzetsa mtendera padziko. Timatsimikiza kuti Yesu anadza kudzasintha anthu ndi kutikonzera Kumwamba. Choncho, Akhristu ayenera kulisintha dziko. Kusintha kotero kumakhala kwa phindu pamene munthu wayamba kusinthika m'kati mwake. Odziwa mbiri yamakedzana amanena kuti dziko la England linasinthika chifukwa

cha chitsitsimutso chomwe anabweretsa a Bambo Wesley. Ukapolo unaletsedwa. Kugwiritsa ntchito ana aang'onoang'ono kunaletsedwa ndi zinanso zinaletsedwa. Komanso pali mgwirizano waukulu pakati pa kutha kwa ukapolo ku America ndi chitsitsimutso cha Chiyeretso chomwe chinali m'kati mwa zaka za m'ma 1850.

→ → → → → → →

# MPINGO WA CHIKHRISTU

## Mpingo Wa Chikhristu Unayamba Bwanji?

Mpingo unayamba Tsiku la Pentekoste Mzimu Woyera atatsanulira otsatira a Yesu ndipo anawapanga kukhala mpingo umodzi Maziko a mpingo ali ku Israeli. Mulungu anatha zaka akulenga malo abwino oti abadwire mwana wake Yesu Khristu. Yesu, amene anabadwira ku Betelehemu, nakula ndi kunyozedwa ku Galileya, anasonkhanitsa gulu la anthu amene Iye anawaphunzitsa zaka zitatu. Anapitapita nachita ntchito zabwino, koma pambuyo pake anapachikidwa chifukwa cha machimo athu. Gulu lake la ophunzira linasokonezeka ndi zochitikazi. Linadzayambanso atauka ndipo linadzakhala mpingo litatsanulidwa ndi Mzimu Woyera.

Okhulupilira 120 okha omwe anasonkhana m'Chipinda Chapamwamba, koma patapita masiku chifikire Tsiku la Pentekoste chiwerengero chinakwera kufika pa 5,000. Chiwerengero chinakula ku Palestina konse, mpaka dera lalikulu la Ufumu wa Aroma ndi kumadera akutali.

## Timatanthauza Chiyani Tikanena Kuti Mpingo Wa Atumwi (Apostolic Church)?

Kuyambira pa Tsiku la Pentekoste kufikira pamene adafa wophunzira womaliza wa Ambuye Yesu, mpingo unkatchedwa wa Atumwi *(Apostolic)*. Timakhulupilira kuti Tomasi anapita ndi uthenga wabwino ku India. Nduna yaikulu ya ku Ethiopia inapita ndi uthenga wabwino kudziko lake. Ena mwa ophunzira anakalalikira ku Babulo, kumpoto kwa Africa, ku Europe ngakhalenso ku China. Kufalikira kunachitikanso chifukwa cha kuzunzidwa komwe kunadza ndi atsogoleri a Ayuda. Yakobo anadulidwa mutu, Petro anaikidwa m'ndende. Paulo, yemwe anali mmodzi wa akuluakulu ozunza, anatembenuka mtima ndi kukhala mtsogoleri wolimba, yemwe anadzakhala wamishoni wa anthu amitundu.

## Mpingo Unakula Bwanji?

Pamene Mpingo unakula, unayamba kusintha. Yerusalemu, Aroma, Aefeso ndi Aigupto, awa adakhala malo ofunikira komwe mpingo

udakhazikika. Nthawi zina pankakhala kusagwirizana pakati pa magulu osiyanasiyana. Kuzunza kunayambanso, ndipo nthawi imeneyi anayambitsa ndi Akaisara a ku Roma. M'chaka cha 250 A.D. (Yesu atabadwa kale) anatsimikiza zofafaniza Chikhristu pakupha, kuzunza ndi kuwagwira okhulupilira kuti akhale akapolo. Mpingo unakula bwino m'malo omwe kuzunzaku kumachitika kwambiri. Aroma anayamba kunena kuti mwazi wa anthu osalakwa amene anaphedwa *(Martyrs)* ndi umene unayambitsa Chikhristu. Mfumu Constantine anavomereza Chikhristu, ndipo m'chaka cha 392 Chikhristu chinavomerezeka kuti ndicho chipembedzo cha anthu onse. Izi zinadzetsa kupita mtsogolo kwa maphunziro, zabwino mundale ndi chikhalidwe cha anthu, komanso m'malo moti anthu azidalira Mulungu, anayamba kudalira boma.

## Mipingo Yosiyanasiyana Inayamba Bwanji?

M'zaka zambiri zapitazo mipingo yosiyanasiyana inayamba. Mpingo uliwonse unali ndi dera lake. Mpingo wa Orthodox wa ku Syria, womwe unati Thomasi ndiye mtsogoleri wake unayambira ku Babulo mpaka ku India. Mpingo wa Coptic unapaza kumpoto kwa Africa. Mpingo wa Ethiopia ndi umene ankaupatula, unali kumadera okwera a ku Ethiopia. Mpingo wa Katolika unafalikira ku Ufumu wa Aroma, koma unagawanikana kukhala Eastern ndi Western Catholics chifukwa nawonso ufumu unagawikana.

Mamembala a Mpingo wa Eastern Catholics ankadzitcha kuti a Orthodox ndipo anadzagawikana kukhala Eastern, True, Greek ndi Russia. Mamembala a Western Catholics anachuluka kwambiri, ndipo anadzakhala amodzi pansi pa Mpingo wa Aroma. Posachedwa anayamba kutchedwa Roman Catholics Church (Mpingo wa Akatolika). Mtsogoleri wawo, Papa anakhala mtsogoleri wamphamvu ku ulaya *(Europe)* pa za ndale.

Nthawi imeneyi panafikanso chipembedzo cha Asilamu. Ankhondo odzipereka anafika ku Middle East ndi ku North Africa nati dzikolo linali la Asilamu. Mpingo wa ku North Africa ndi wa ku Babulo unali pafupi kutha. Vuto linali lakuti nzika zonse zinafunika kukhala Akhristu ndipo ochepa okha ndi amene anali Akhristu enieni.

## Kodi Mpingo Unalidi Wokhulupirika Kwa Mulungu?

M'zaka za Middle Ages (1000-1400 A.D.), Mpingo unatenga

mphamvu muchikhalidwe, maphunziro, ndale, ndi ntchito ku Ulaya (Europe). Europe anali kukula mwamphamvu, ndipo pakati penipeni pamphamvu zake panali Papa. Mphamvu ya uzimu inachoka mumpingo. Chisokonekero chinayambira kwa Papa kufikira kwa ansembe. Ansembe anayamba kugulitsa chikhululukiro cha machimo ngati mtengo wake unali woyenera. Papa ankasonkhanitsa ndalama zomangitsira tchalitchi ku Roma pogulitsa chikhululukiro cha machimo amene anatsala pang'ono kuchitika. Mulungu anangotsala pang'ono kusintha zinthu.

## Chiyambi Cha Mpingo

Mpingo wa Aroma womwewo anthu ena sanakondwere ndi chisokonekerocho. Omwe anatsutsa anaphedwa mwa nkhanza, ndipo Papa anali wosachimwa. A Martin Luther, Mjeremani, anali woyamba kupambana ndi mtsutso wake. Iye anali wansembe yemwe anatsutsa poyera za kugulitsa chikhululukiro cha machimo amene ankayembekezeka kuchitidwa. Anaitanidwa kumulandu ndipo anadulidwa mumpingo. Akhristu Achijeremani ambiri, anthu wamba ndi atsogoleri omwe anagwirizana ndi Luther. Kusintha kwa a Mpatuko *(Protestant Reformation)* kunayambika. Kutsutsa kwa Luther kunakhazikitsa BUKU LOPATULIKA, osati Papa, monga wolamulira wa chiphunzitso cha Chikhristu. Luther anamasulira Buku Lopatulika m'chilankhulo cha Chijeremani kuti onse akhoze kuwerenga.

## Kodi Mipingo Yosiyanasiyana Ya Mpatuko Inayamba Bwanji?

M'mene Luther ankalankhula, atsogoleri ambiri a Mpatuko anaoneka. Onse anavomerezana kuti BUKU LOPATULIKA ndilo linali ndi mphamvu yolamulira Akhristu, ndipo linayamba kumasulidwa muzinenero zosiyanasiyana. Mipingo yosiyanasiyana inayamba motsogozedwa ndi atsogoleri ambiri, koma anatenga BUKU LOPATULIKA monga mtsogoleri.

MPINGO WA LUTHERAN unayamba motsatira Martin Luther ndipo unakhala wamphamvu ku Jeremani ndi ku Scandinavia.

Buku la INSTITUTE OF THE CHRISTIAN RELIGION linalembedwa ndi a John Calvin ndipo linathandiza kwambiri pantchito ya a Mpatuko. Chiphunzitso cha a Calvin chinayambitsa REFORMED CHURCHES monga DUTCH REFORMED ndi

PRESBYTERIAN CHURCH.

MIPINGO YA'BAPTIST inkalalikira kuti ubatizo ndi umene umamuyenereza munthu kukhala Mkhristu. Anagwiritsa ntchito maudindo ambiri, ngakhale kuti ena ambiri anatsatira Reformed School.

Atsogoleri a Mpingo wa Katolika ku England anatsutsa kwambiri Luther. Papa anapereka ulemu waukulu kwa Mfumu ya ku England woti, "Mtetezi wa Chikhulupiriro" (Defender of the Faith") chifukwa chotsutsana ndi a Luther. Kenako, kusagwirizana pachipembedzo ndi ndale pakati pa Mfumu ndi Papa kunadzetsa kulekana kwa Mpingo wa England ndi Roman Catholics. Anayamba kudziwika ndi dzina loti MPINGO WA ANGLICAN ndipo sanasiyane kwambiri ndi chiphunzitso cha Mpatuko.

BUNGWE LODZIPEREKA KWATHUNTHU KWA MULUNGU. Mipingo ina ya Mpatuko inaona kuti ungwiro ndi kukhulupirika ndi zofunika m'Buku Lopatulika. Amanyoza miyambo ndi zizindikiro. Analimbikitsa ndi kumvera Mawu a Mulungu. A QUAKERS ku England ndi a MORAVIANS ku Jeremani anali otere.

## Kusintha Kumeneku Kunakhudza Bwanji Mpingo Wa Katolika?

Poyamba Mpingo wa Katolika unalimbikira kuti uthetse za Mpatuko. Panali nkhondo. Mpatuko unachoka ku Italy ndi ku Spain ndi anthu ofufuza. Reformed Church inachotsedwa ndi Afalansa ndi nkhondo ya Bartholomew Woyera. Ngakhale zinali choncho, chipembedzo cha Mpatuko chinapita patsogolo. Ena a mu Mpingo wa Katolika anapempha kuti asinthe ndipo panali "Catholic Reformation" pomwe zambiri anazisintha.

## Chiphunzitso Cha Wopatuka Makamaka Chinkaphunzitsa Chiyani?

Mpatuko makamaka unabweretsa chilakolako (chidwi) chatsopano pa za chiphunzitso. Choonadi chenicheni chomwe chinali ndi mfundo zinayi chinakhazikitsidwa.

1. Kuti Buku Lopatulika ndilo linali chiphunzitso champhamvu osati Papa.

2. Kuti Akhristu onse ndi ansembe omwe akhoza kulankhulana ndi Mulungu.

3. Kuti tinapulumutsidwa mwachisomo mwa Yesu Khristu osati ndi ntchito zabwino kapena kupereka ndalama ku Mpingo.

4. Masakaramenti si matsenga kuti angapangitse chikhululukiro koma ndi zizindikiro za ntchito ya Mulungu mumtima mwa wokhulupirira.

## James Arminius

James Arminius, yemwe anali wophunzira wa Dutch Reformed, anaona cholakwika mumfundo za Bambo Calvin. Otsatira a Bambo Calvin anaphunzitsa kuti Mulungu anasankhiratu anthu okapulumuka ndi okawonongeka. Arminius anaona kuti izi sizinali kugwirizana ndi Buku Lopatulika. Choncho, anaphunzitsa kuti Mulungu, kudzera mwa Mzimu Woyera, anampatsa munthu mphamvu yosankha.

## John Wesley

John Wesley, yemwe anali wansembe wa Anglican anafuna mgwirizano weniweni ndi Mulungu, anadza motsogozedwa ndi Arminius ndi gulu la Moravian. Anasinthika mwa uzimu nakhala mtsogoleri wamkulu wa chipembedzo. Chitsitsimutso chinafalikira ku England ndi ku America ndipo otsatira ake anatchedwa Amethodist chifukwa cha chiphunzitso chawo, ndi ntchito zawo za Chikhristu. Anakana motsimikiza kufunika kwa "Ungwiro wa Chikhristu" m'miyoyo ya otsatira a Yesu Khristu.

## Mipingo Ya Chiyeretso (Holiness Churches) Inayamba Bwanji?

M'zaka za m'ma 1900 chitsitsimutso chachikulu cha Chiyeretso chinakwanira ku America ndi ku Britain konse. Atsogoleri anachokera ku mipingo yosiyanasiyana - a Andrew Murray, Beverley Carradine, Samuel Logan Brengle, Asa Mahon, Phoebe Palmer, Seth Rees, A.B. Simpson, Daniel Steele, Hannah Smith, A.M. Hills, pongotchula pang'ono chabe.

Mabungwe a Chiyeretso omwe ankatumikira m'mipingo onse anafika. Misonkhano ya misasa, ndi ya Keswick inayamba. Akuluakulu a mipingo ina yokhazikika sanakondwere ndi anthu a "Chiyeretso", kotero kuti anawachotsa m'mipingo yawo. Mipingo ya Chiyeretso inayambika

m'malo ambiri. Matchalitchi amenewa anakonza mabungwe ndi mipingo. Mpingo waukulu wokhazikitsidwa unali Mpingo wa Nazarene.

## Kodi Mipingo Ya Pentekoste Ndi Ya Chiyeretso Inagwirizana Bwanji?

Poonetsetsa chiyambi chake. magulu a Pentekoste ndi a Chiyeretso *(Holiness)* anali ovuta kuwalekanitsa. Popita panthawi kunaoneka kuti mipingo ya Chiyeretso inakaphunzitsa za ntchito ya Mzimu Woyera yosintha moyo wa munthu pomwe a Pentekoste ankaphunzitsa za zizindikiro zooneka zonse ankati zinkaoneka Mzimu Woyera akatsanulira. Mpingo wa Nazarene unachotsa mawu oti "Pentekoste" pa dzina lake m'chaka cha 1919 kuti udziwike bwino kuti ndi Mpingo wa Chiyeretso.

→ → → → → → →

## Mutu Wachisanu Ndi Chinayi

## MBIRI YA MPINGO WA NAZARENE

### Anayambitsa Mpingo Wa Nazarene Ndani?

Sitinganene kuti Mpingo wa Nazarene anauyambitsa ndi munthu m'modzi. Panali atsogoleri a madera ambiri a m'maiko a America ndi Britain amene anayambitsa mpingo wathu. Komabe, Dokotala Phineas F. Bresee ndi amene amaganiziridwa kuti ndiye tate wa mpingowu chifukwa chakuti anagwira ntchito yaikulu.

### Dokotala Bresee Anali Yani?

Iye anali mtumiki wa Mpingo wa Methodist yemwe anathandiza mipingo yomwe ankaitumikira ku Iowa ndi ku California kuti ikule. Ku Iowa mipingo inaonjezereka ndi mamembala okwanira 678 pomwe ku California m'mipingo itatu munalowa mamembala atsopano okwanira 856. Dokotala Bresee ankalimbikitsa kwambiri za maphunziro kotero kuti amathandiza pokhazikitsa sukulu zazing'ono ndi sukulu zapamwamba za Yunivesite komanso anali mukomiti yapamwamba ya Yunivesite of Southern California. Patatha zaka zokwana 37, anaumirizidwa kuti asankhe chinthu chimodzi, kutumikira anthu a pamishoni pake Los Angeles kapena kutumikira Mpingo wa Methodist womwe unali wolemera. Ndi mtima wodzala ndi "chisoni chachikulu" anaona kuti kunali kofunika kusiya Mpingo wa Methodist, ndipo anasankha kutumikira pamishoni. Ndipo bwenzi lake lapamtima, Dokotala J.P. Widney anagwira naye ntchito pamodzi. Mishoniyo anaitcha dzina loti Mpingo wa Nazarene. M'zaka zotsatirazo, Dokotala Bresee anagwira ntchito mosatopa kugwirizanitsa mpingo wake ndi mipingo ina ya chiyeretso ku America kuti akhale amodzi.

### Mipingo Ya Chiyeretso Yoyamba Ku America Kuphatikizapo Wa Nazarene

Mpingo wa Chiyeretso woyamba komanso wokhazikika womwe unakhala gawo la Mpingo wa Nazarene unali wa kuchigawo cha Rhode Island m'chaka cha 1887. Mpingowu womwe mtsogoleri wake anali a F.A. Hillery, unagwirizana ndi mipingo ina ku New York ndi kukhala mpingo umodzi ndipo mpingowu unatchedwa kuti Mgwirizano wa

Mipingo ya Pentekoste ku America *(Association of Pentekostal Churches of America)*. Pomwe ankafika chaka cha 1907 anali ndi matchalitchi 48 ndipo mamembala analipo 2371. M'modzi wa atsogoleriwo anali wachinyamata ndiponso wanzeru yemwe dzina lake anali H. F. Reynolds. Iye ndi yemwe anayenera kudzakhala Tate wa ntchito za Mishoni mu Mpingo wa Nazarene. Mpingo womwe uyambira mu "Nkhokwe ya Ulemerero" ya a Bresee ku Los Angeles m'chaka cha 1895 unakula kwambiri ndi kuyambitsanso matchalitchi ena atsopano. Alaliki oyendayenda monga a Bud Robinson ndi a C.W. Ruth, nawonso anathandiza. M'mene chinkakwana chaka cha 1898, panaoneka kuti mgwirizano unafika ndipo a Bresee anapanga BUKU loyamba LA MALAMULO NDI MAYENDETSEDWA A MPINGO WA NAZARENE *(Manual)*. M'chaka cha 1904, mpingo anaugawa muzigawo (madisitirikiti) ndipo anakumana ku Msonkhano Waukulu *(General Assembly)*. Pofika chaka cha 1907, matchalitchi analipo 45 ndipo mamembala anakwana 3,827. Atsogoleri a m'mipingo yonseyi anaona kuti kunali koyenera kuphatikizana ndi kukhala mpingo umodzi. Umodzi umenewu unachitikadi m'chaka cha 1907 pomwe magulu awiri anakonza Msonkhano Waukulu *(General Assembly)* ku Chicago. Bungwe latsopanoli analitcha kuti Mpingo wa Nazarene, ndipo ulamuliro woyimiliridwa ndi anthu ambiri, ndipo tikana ndi kupewa ulamuliro wopangidwa ndi munthu m'modzi yekha.

## Mpingo Wachiwiri Wa Chiyeretso Womwe Unaphatikizana Ndi Wa Nazarene

Nkhondo yomwe inali pakati pa chigawo cha kumpoto ndi kum'mwera ku United States of America inadzetsa mpatuko waukulu pakati pa anthu a ku America. Anthu a kum'mwera sankakondweretsedwa ndi anthu a kumpoto omwe ankatchedwa kuti Ayankee. Uthenga wa Chiyeretso unachita zazikulu kum'mwera. M'chaka cha 1894 Mpingo wa Khristu wa Chipangano Chatsopano *(New Testament Church of Christ)* unayambika ndipo mtsogoleri wake anali Bambo R.L. Harris. M'chaka cha 1901 Bambo C.B. Jernigan anayambitsa Mpingo wa Independent Holiness. Mipingo imeneyi inagwirizana m'chaka cha 1905 kupanga mpingo umodzi wa Holiness Church of Christ. Unafalikira kwambiri kum'mwera ndipo pasanapite nthawi anadzakumana ndi anthu enanso okhulupirira za chiyeretso a kum'mawa ndi kumadzulo kwa dzikolo. Pa 8 October, 1908, nthumwi za Mpingo wa Holiness Church of Christ

zinakumana ku Pilot Point ku Texas ndikukambirana zopanga mpingo umodzi. Chimwemwe chitafika pachimake chifukwa cha chiyanjano chomwe chinayambanso pakati pa anthu a kum'mwera ndi a kumpoto, mipingoyi inachita masankho ndi kugwirizana kuti dzina la mpingo likhale Pentecostal Church of the Nazarene. Tsopano mamembala a mpingowu anakwanira 10414. Akuluakulu oyamba a mpingowu, Atsogoleri Akuluakulu *(General Superintendents)* anali P.F. Bresee a kumadzulo, H.F. Reynolds a kum'mawa ndi a E.P. Ellyson a kum'mwera. Poopa kuti angayambe kufanana ndi gulu lina la Pentekoste m'chaka cha 1919 anachotsa mawu oti "Pentekoste" omwe linali pa dzina la.

## Mipingo Ina Yomwe Inaphatikizana Ndi Wa Nazarene

M'zaka zingapo zotsatira, mipingo ina ndi mabungwe ena analowa Mpingo wa Nazarene. Mwa magulu ena odziwika ndi awa:

Mpingo wa PENTECOSTAL CHURCH OF SCOTLAND womwe mtsogoleri wake ndi a George Sharpe unaphatikizana ndi Mpingo wa Nazarene m'chaka cha 1915. Ataphatikizana adakayambitsa Mpingo wa Nazarene ku Great Britain. Amishoni awo a David ndi a Kanema Hynd, ndi omwe anayambitsa chipatala cha Mpingo wa Nazarene ku Manzini m'dziko la Swaziland.

Mpingo wa PENTEKOSTAL MISSION unalowa m'chaka cha 1915. Mipingo yawo inali m'madera ambiri kum'mwera kwa United States of America.

Bungwe la LAYMEN'S HOLINESS ASSOCIATION linalowa m'chaka cha 1922.

Mpingo wa INTERNATIONAL HOLINESS MISSION wa ku England womwe unali ndi ntchito yaikulu kum'mwera kwa Africa unalowa m'chaka cha 1952.

Mpingo wa CALVARY HOLINESS CHURCH wa ku England unalowa m'chaka cha 1958.

Mpingo wa GOSPEL WORKER'S CHURCH wa ku Canada unalowa m'chaka cha 1958.

Magulu ndi mipingo yomwe inaphatikizana ndi Mpingo wa Nazarene kuyambira pachiyambi kufikira tsopano ali gawo lofunika kwambiri mu Mpingo wa Nazarene chifukwa ndi amene asonkhanitsa anthu

okhulupirira Chiyeretso padziko lonse lapansi.

## Kukula Kwa Mpingo Wa Nazarene Ku America

M'zaka makumi awiri zoyamba Mpingo wa Nazarene unkakula ndi 13% *(percent)* pachaka, anthu ankaonjezeka kuchoka pa 10,000 kufika pachiwerengero cha 100,000. Chiwerengerochi chinkakwera chifukwa cha mipingo kapena magulu ophatikizana ndi mpingowu komanso kukweraku kunkachitika chifukwa cha matchalitchi ena omwe ankapita patsogolo. Kukulaku kunapitirirabe koma popita pazaka zinthu sizimapita patsogolo kwenikweni. M'chaka cha 1958 mpingowu unali ndi mamembala okwanira 350,000 ndipo m'chaka cha 1985 mamembala analipo pafupifupi 800,000. Chiwerengero chachikulu chili ku America ngakhale kuti m'maiko enanso chiwerengero chikupita patsogolo kwambiri.

## Mayendetsedwe Ake A Ntchito Ya Mpingo Wa Nazarene

Mulungu anawatsogolera anthu omwe anali akuluakulu oyamba a Mpingo wa Nazarene kuti akhoza kukonza njira yoyendetsera mpingo paulamuliro womwe ungakhale m'manja mwa anthu komanso kukhala ndi mawu kapena mwayi wotha kudzisankhira zoyenera kuchita ndi zomwe zinapangitsa kuti atsogoleri ndi mipingo ya Presbyterian, Methodist, Anglican, Congregational, ndi ena kuti avomereze. Tchalitchi lililonse limadzisankhira lokha mbusa, koma amayenera kusankha mbusa yemwe ali ndi makalata omuyenereza ochokera kulikulu la chigawocho *(district)*, ndiponso kuti chisankho chawo chivomerezedwe ndi mtsogoleri wa chigawo *(district superintendent)*. Misonkhano yonse kapenanso mabungwe opanga malamulo a mpingo, mumakhala mamembala a mpingo ndi abusa chifukwa chakuti timakhulupirira kuti siabusa okha omwe ali ndi mgwirizano ndi Mulungu komanso mamembala onse.

## Mpingo Umatumikira Osowa

Matchalitchi ambiri amayambira kumadera omwe kuli anthu osowa. Uthenga wa Chiyeretso unagonjetseratu zoipa zambiri zimene zimawapangitsa anthu kuti akhale osowa. Chifukwa cha ichi inafika nthawi pamene matchalitchi athu sanakhalenso osowa. Nthawi zambiri mpingo wathu umakhazikitsa matchalitchi kumalo kumene kulibe matchalitchiwo, ndipo padakali pano pali kusoweka kuti mpingo ufike kumizinda ina ya padziko lapansi komwe ntchito ya Ambuye kulibe.

## Mpingo Wa Nazarene Umalimbikiranso Za Maphunziro

Mpingo wa Nazarene wakhala ukulimbikitsa kwambiri za maphunziro a achinyamata. BUKU LOPATULIKA limanena kuti tiziphunzitsa achinyamata athu njira ya Mulungu. Izi timazilimbikiradi. M'chaka cha 1908 kunali sukulu zapamwamba zokwana zisanu ku America zomwe anthu amakaphunzira kuti apeze degree. Masiku ano pali sukulu za Yunivesite zokwanira 8, sukulu za ubusa *(Bible College)*, ndi Graduate Seminary ku America komanso pali sukulu zina za yunivesite zokwana 20, Graduate School ndi makoleji ena a za ubusa *(Bible College)* mbali zosiyanasiyana padziko lapansi. Sukulu zitatu za yunivesite ndi sukulu za ubusa *(Bible College)* zisanu ndi ziwiri (7) zinakhazikitsidwanso kuno ku Africa. Bungwe Lalikulu Loyendetsa Ntchito Za Mpingo Wonse *(General Board)* likukonzanso zokhazikitsa Sukulu ya magraduate kuno ku Africa.

## Anazarene Amalimbikitsa Ntchito Yolemba Mabuku

Mpingo ukukhudzidwa kwambiri ndi ntchito yokonza mabuku a Chiyeretso. M'chaka cha 1908, mabuku osiyanasiyana okwanira asanu ndi atatu anapangidwa. Kenaka adadzawaphatikiza kukhala buku limodzi nalitcha kuti *"Herald of Holiness"* kutanthauza kuti Uthenga wa Chiyeretso. Buku limeneli lathandiza kwambiri pofalitsa nkhani za mpingo. Nyumba yosindikizira mabuku inakhazikitsidwanso, yomwe inayamba kupanga zipangizo zogwiritsira ntchito mu Sande Sukulu, ntchito ya mpingo, sukulu za ubusa komanso zipangizo zogwiritsira ntchito ya mapemphero. Masiku ano Mpingo wa Nazarene womwe ukudziwika kwambiri ndi dzina la mabuku a nyimbo *"Lillenas"* komanso mabuku ogwiritsira ntchito zosiyanasiyana odziwika ndi dzina loti *"Beacon Hill"*, ndi umodzi mwa mipingo ikuluikulu yomwe ikupanga mabuku. Bungwe la Africa Nazarene Publications limapanga mabuku ogwiritsira ntchito mu Sande Sukulu, mabuku a achinyamata ndi a ntchito zina ndi zina za mpingo, mabuku ena a za uzimu ndi nyuzipepala kapena ya chigawo chino cha Africa ya *TRANS AFRICAN*.

## Anazarene Amalimbikitsa Kufalitsa Uthenga

Chiyeretso ndi kufalitsa uthenga zimayendera limodzi. M'chaka cha 1910 m'madera asanu ndi awiri a padziko lapansi munali amishoni. Maderawa ndi a Africa, India, Japan, Mexico, Guatemala, Cape Verde ndi Cuba. Bungwe lalikulu loyendetsa ntchito za mpingo la General Board

linakhazikitsidwa kuti likhoze kuyendetsa ntchito yofalitsa uthenga yomwe inkakula kwambiri. M'chaka cha 1985 mpingo unali utakula ndi kukhazikitsidwa m'maiko okwanira makumi asanu ndi awiri ndi mphambu zisanu, (75) ndipo zigawo *(districts)* zinalipo 137 ndipo amishoni analipo (620).

## Atsogoleri Ofunikira Kwambiri Mu Mbiri Ya Mpingo Wa Nazarene

Ena mwa atsogoleri odziwika kwambiri anali:

DR. PHINEAS F. BRESEE, mlaliki wamphamvu yemwe ankafunitsitsa kuti ulemelero wa Mulungu udzikhala pakati pa anthu ake.

BAMBO JAMES B. CHAPMAN omwe anakhala chitsanzo cha m'mene General Superintendent amayenera kugwirira ntchito yake.

MAYI SUSAN B. FITKIN omwe anatsitsimutsa amayi kuti akhale ndi mphamvu pantchito yofalitsa uthenga padziko lapansi ndi kukhazikitsa ntchito za mpingo ndi zipatala.

BAMBO M. LUNN omwe anathandiza kwambiri pokhazikitsa ndi kuyendetsa ntchito za nyumba yosindikizira mabuku ya Nazarene Publishing House.

BAMBO HIRAM F. REYNOLDS omwe anali ndi zaka zakubadwa zochepa kwambiri poyerekeza ndi atsogoleri akuluakulu a Mpingo wa Nazarene *(Generals)* ndipo iwowa anali mkulu woyang'anira ntchito za mishoni za mpingo kwa zaka zokwanira makumi awiri ndi mphambu zisanu (25).

BAMBO ROBINSON, omwe ankatchulidwanso kuti amalume a Bud *("Uncle Bud")*, anali mlaliki woyendayenda wodziwika kwambiri yemwe anagonjetsa zolepheretsa zina pofalitsa mwamphamvu Uthenga Wabwino mumpingo. Zolepheretsa zomwe anazigonjetsa zinali za maphunziro ndi zinenero.

BAMBO STEPHEN S. WHITE adapangitsa kuti magazini ya *HERALD OF HOLINESS* (kutanthauza kuti Uthenga wa Chiyeretso) ikhale yofunika kwambiri mu Mpingo wa Nazarene.

BAMBO H. ORTON WILEY, omwe anali mphunzitsi, woyendetsa

ntchito komanso wophunzira kwambiri za Mulungu, ankadziwa kuthetsa mavuto ndiponso ndi amene anapanga maziko a sukulu ya ubusa mu Mpingo wa Nazarene.

→ → → → → → →

# CHIGAWO CHA AFRICA

## Kodi Chigawo Cha Mpingo Wa Nazarene Cha Africa Ndi Chotani?

M'chigawo cha Africa muli maiko ndi zilumba za mu Africa kupatulapo maiko omwe achita malire ndi nyanja ya Mediteranean. M'modzi wa Atsogoleri a mpingo wonse *(General Superintendent)* ali ndi udindo woyang'anira ntchito za chigawochi. Mkulu Woyang'anira mpingo ku Africa *(Regional Director)* amafotokozera bungwe loyendetsa ntchito la General Board ndi kwa akuluakulu *(General Superintendents)* m'mene ntchito za Mpingo wa Nazarene m'chigawochi zikuyendera. Bungwe lalikulu la muchigawo *(Regional Council)* limakumana pakatha zaka zinayi kuona momwe angapititsire patsogolo ntchito.

## Maofesi A Chigawo *(Regional Offices)* Anamangidwa Kuti?

Maofesi amenewa anamangidwa pamsewu wopita ku Mbabade ku Manzini, m'dziko la Swaziland, dziko lomwe Mpingo wa Nazarene udayambira m'chigawo cha Africa.

## Ntchito Za Mu Chigawochi Zimayendetsedwa Bwanji?

Chigawo cha Africa chinagawidwanso kasanu: Kumadzulo kwa Africa *(Africa West)*, ku'mawa kwa Africa *(Africa East)*, pakati pa Africa *(Africa Central)*, kum'mwera cha kum'mawa kwa Africa *(Africa Southeast)*, ndi kum'mwera kwa Africa *(Africa South)*. Maofesi a zigawozi anamangidwa ku Abidjan, Nairobi, Harare, Manzini ndi ku Florida. Chigawo *(Field)* chilichonse chili ndi woyang'anira wake yemwe amafotokozera Mkulu wa Mpingo kuchigawo chonse cha Africa (Regional Director) m'mene ntchito ikuyendera.

## Kodi Mpingowu Uli Ndi Mautumiki Otani Mu Africa?

Udindo woyamba wa chigawo chilichonse ndi wokhazikitsa matchalitchi ndi kugawa madistrict kuti afalitse bwino Uthenga Wabwino. Zigawo *(districts)* zikamapita patsogolo zimakhala ndi mtolo waukulu wofalitsa Uthenga Wabwino m'madera ake. Mpingo Wonse *(General Church)* umapitiriza kuthandiza pophunzitsa anthu otsogolera mumpingo.

Utumiki wothandiza anthu ovutika *(Compassionate Ministries)* umachitika malingana ndi zosowa za anthu komanso malinga ndi m'mene thandizo lingapezekere mumpingo. Ena mwa mautumiki athu ndi a masukulu, zipatala, za ulimi, njala ndi mavuto ena, ndi kuthandiza anthu ena powapatsa zinthu zofunikira pamaphunziro awo.

## Kayendetsedwe Ka Ntchito Mu Chigawo *(District)*

Matchalitchi mu "field" iliyonse adagawidwa "m'madistrict". Pamakhala makhwerero anai disitilikiti ikayambika. Ndondomeko yake ndi yotere:

DERA LOYAMBA LATSOPANO *(Pioneer Area)* limakhala dera longoyamba kumene pantchito ya mpingo ndipo limayambira ndi gulu la amishoni.

CHIGAWO CHOYAMBA CHATSOPANO *(Pioneer District)* amakhazikitsidwa matchalitchi akangokwana awiri. Deralo likhoza kumagwira ntchito zake monga m'mene imakhalira district komabe mtsogoleri *(Superintendent)* amakhala m'modzi wa amishoni.

CHIGAWO AMENE AKULAMULIDWA NDI AMISHONI NDI ENI NTHAKA PAMODZI *(National Mission District)* amakhazikitsidwa chigawochi chikakhala ndi matchalitchi okwanira asanu ndi kukhala ndi mamembala okwanira 250 komanso ngati angakhoze kupeza 25% *(percent)* ya ndalama zoyendetsera chigawocho.

CHIGAWO AMENE ALI KUDZITHANDIZA PAMODZI NDI AMISHONI *(Mission District)* kuti district ifike pamenepa iyenera kukhala ndi mamembala okwanira 500, 20% *(percent)* ya matchalitchiwo akhale odzithandiza okha (self suport) ndipo adzipereka 50 percent ya ndalama zoyendetsera ntchito ya district. District yotere imadzisankhira yokha mtsogoleri (Superintendent) ndipo imakhala ndi mwayi wotumiza nthumwi ku Msonkhano Waukulu *(General Assembly)* pokhazikitsanso mtsogoleri wa chigawo *(District Superintendent)*.

CHIGAWO CHA ENI NTHAKA *(Regular District)* chikhoza kuyambidwa ngati district ili ndi mamembala okwanira 1000 ndiponso ngati ingakhale ikupeza ndalama zonse zofunikira poyendetsa ntchito ya mpingo mu district yawo. District yotere

imayendetsedwa ntchito yake mofanana ndi madistrict ena opezeka padziko lonse lapansi.

### Makoleji Athu Ophunzirira Za Ubusa *(Theological Colleges)*

M'chaka cha 1986 makoleji ophunzirira za ubusa m'chigawo cha Africa analipo khumi ndipo ophunzira analipo 511. Koleji iliyonse ili ndi bungwe lakelake loyendetsa ntchito zake ndipo bungwelo limaimilira zigawo zonse *(districts)* zomwe kolejiyo ikuthandiza. Mkulu woyendetsa ntchito za maphunziro a makoleji a za ubusa *(Theological College Coordinator)* amathandiza kuti makolejiwa adzigwira ntchito pamodzi kuti akhale ndi phindu muchigawo *(Region)*. Nthawi imeneyi, panasoweka makoleji atsopano kuti athandize maiko omwe ali muzigawo *(fields)* za kum'mawa ndi kumadzulo kwa Africa.

## NTCHITO YA MPINGO WA NAZARENE INAYAMBA WANJI MU CHIGAWO CHA AFRICA?

### Cape Verde

Ntchito yoyamba ya Mpingo wa Nazarene kuno ku Africa inayambika pa zilumba za Cape Verde m'chaka cha 1901. Bambo John Diaz anapita ku America pasitima ya pamadzi yomwe inkachokera ku zilumba za Cape Verde, ndipo adakali ku America komweko anapeza kwa nthawi yoyamba mpingo wolalikira za chiyeretso. Anabwerera kuzilumba za Cape Verde kukayamba ntchito yaikulu komanso yovuta yokhazikitsa Mpingo wa "Chiprotestant" kumalo komwe kunali Mpingo wa Akatolika. Ntchito yake inali ya phindu. Masiku ano Mpingo wa Nazarene ndi mpingo waukulu kuposa mipingo ina yonse ya "Chiprotestant" pazilumba za Cape Verde.

### Kukhazikitsidwa Kwa Mpingo Ku Swaziland

Bambo Harmon Schmelzenbach ndi mkazi wao Lulu, komanso a Etta Innis anabwera ku Africa m'chaka cha 1908. Mpingo wao utaphatikizana ndi wa Nazarene anapemphedwa kuti akhazikitse Mpingo wa Nazarene ku Africa. Iwo anasankha zoyamba ntchitoyi ku Endingeni m'dziko la Swaziland. Kuyambira nthawi imeneyo, mpingo wafika m'maiko oposa khumi ndi asanu a mu Africa. Chiyambi chake sichinali champhamvu

koma khama la gulu la amishoni oyambawo linapangitsa kuti ntchito ikhazikitsidwe ku Piggs Peak, ku Manzini ndi ku Siteki. Mbusa Schmelzenbach anadzipereka kwathunthu kuyamba mpingo m'dera lomwe linali la matenda a malungo kotero kuti iye anamwalira m'chaka cha 1928. Nthawi imeneyo, mpingo unali utafika kumalire a dziko la Swaziland, Mozambique ndiponso dziko la South Africa.

NTCHITO YA CHIPATALA. Dr. David Hynd anali atayamba kugwira ntchito pamodzi ndi antchito ena ndipo anatsekula chipatala ku Manzini, chomwe chakhala chothandiza kwambiri kwa anthu a ku Swaziland pa ntchito ya umoyo.

SUKULU YA UBUSA *(Bible College)*, inayamba ku Pigg's Peak, ndipo chifukwa cha kukula kwa ntchitoyi zipangizo zinali zosakwanira ndipo anaisamutsira ku Siteki.

MASUKULU ankagwira ntchito kulikonse komwe anakhazikitsidwa chifukwa chakuti maphunziro anali ofunika kwambiri.

## Gawo Loyamba La Kukula Kwa Ntchito

Kumigodi ya golide ya kum'mawa kwa Transvaal ndi Johannesburg ndi mizinda yomwe ntchito ya mpingo inkayenda bwino kwambiri chifukwa chakuti anthu omwe ankagwira ntchito kumigodiyi ankachokera m'maiko onse a kum'mwera kwa Africa. Mbusa ndi Mayi J. F. R. Penn anapita ku Sabie kukakhazikitsa ntchito ya Mpingo wa Nazarene. M'mene migodi inasiya ntchito yake chifukwa cha kutha kwa golide ntchito ya mpingo inasamukira ku Acornhoek komwe kunkakhala anthu. Ntchito inanso inayamba m'migodi ya ku Johannesburg komwe anthu mazanamazana a ku Mozambique ankagwira ntchito. Ena mwa anthuwa anatembenuka mtima nabwereranso kwawo kukafalitsa Uthenga Wabwino. M'chaka cha 1925 Mbusa ndi Mayi C. S. Jenkins anapemphedwa kuti apite ku Mozambique kukawathandiza anthuwa kukhazikitsa mpingo. Posatenga nthawi ntchito yatsopanoyi inayamba kuyenda bwino kwambiri, ndipo unakhala umodzi wa mipingo yamphamvu kwambiri ku Africa.

Mavuto ena a padziko lonse lapansi komanso nkhondo inabwezera pambuyo ntchito yomwe imayenda bwinoyi kuyambira chaka cha 1930 mpaka 1945. M'zaka zimenezi mpingo unakula kwambiri muuzimu. Abusa a m'maikowa sanasiye ntchito ngakhale kuti samalandira thandizo

la ndalama. Amishoniwo anayamba kugawana malipiro awo ndi abusa omwe anali eni dziko. Ichi chinali chiyambi cha kupita mtsogolo kwa ntchito.

## Gawo Lachiwiri La Kukula Kwa Ntchito

M'chaka cha 1948 Mpingo wa Nazarene womwe unali wodzala ndi mzimu unatsitsimuka ndi mphamvu yaikulu yomwe inapitirira zaka zokwanira makumi awiri. Anthu akuda ndi angerezi (azungu) anagwira pamodzi ntchito yotengera anthu uthenga wabwino. Zonse zinayamba chifukwa cha pemphero. Zolinga zinakhazikitsidwa m'chaka cha 1943 ndipo mpingo wonse unauzidwa kuti upemphere. Mulungu anayankha modabwitsa. Amishoni anabwera ambiri kuchokera kumaiko a kutsidya la nyanja komanso atsogoleri a mpingo omwe anali a m'maiko momwemo anavomereza kuitana kwa Mulungu. Mipingo inakhazikitsidwa kuchokera ku Malawi ndi ku Zambia kupita ku Cape Point.

NTCHITO PAKATI PA ACHIZUNGU. Mbusa C. S. Strickland anafika ku South Africa m'chaka cha 1948 kuyamba kugwira ntchito pakati pa Azungu malo omwe poyamba ankapemphera anthu akuda okha.

NTCHITO YA MAKALADI inayamba ndipo masiku ano zigawo *(districts)* zinali za makaladi ndi Amwenye, zomwe zili ku Johannesburg, Durban, Port Elizabeth, ndi Cape Town ndi zomwe zikukula kwambiri kuposa zigawo zina zonse za ku South Africa.

Abusa a m'dziko la Swaziland anavomera pempho loti alowe m'mizinda yomwe ikukula kwambiri ku South Africa.

Ntchito yayambanso pakati pa anthu a mtundu wa APEDI ku Transvaal komanso kumizinda yambiri. Anthu a ku Swaziland komweko omwe akugwira ntchito komanso a ku Eastern Transvaal ndi omwe anathandiza kuti izi zitheke.

A INTERNATIONAL HOLINESS MISSION analowa Mpingo wa Nazarene m'chaka cha 1952. Ntchito yawo ya mishoni kumpoto kwa dziko la Mozambique idawachititsa chidwi a Mpingo wa maiko a pakati mu Africa.

Mpingowu unalowa m'dziko la MALAWI m'chaka cha 1956. M'dziko limenelinso, amishoni a mtundu wa Chiswazi a ku Swaziland

ndi a ku Eastern Transvaal anapita kukaphunzitsa kusukulu ya ubusa ndi kukhalanso abusa a m'matchalitchi. Masiku ano tili ndi zigawo zitatu ku Malawi zimene zili zamphamvu.

Kuchokera ku Malawi mpingo unapita ku ZAMBIA ndi ku ZIMBABWE. Kumaikowa anamanga matchalitchi ndi kuthandiza kukhazikitsa zigawo.

M'zaka zimenezi, mpingo wa ku Africa wakhala ukukula kotero kuti njira zina zimene umayendetsera ntchito zake zinayenera kusinthidwa. Panatenga nthawi yaitali yokonzanso zinthu mwatsopano pokonzekera khwerero lina la kupambana.

## Gawo Lino Limene Ntchito Ikukula Mokondweretsa

Chikonzero chomwe tafotokoza mundime yoyamba *(Region Africa)* chomwe chinakonzedwa pakayendetsedwe ka ntchito chinayamba kugwiritsidwa ntchito m'chaka cha 1980. Uku ndiko kunakhala kuyamba kwa gawo lina la kupita mtsogolo kwa ntchito ku Africa. Kuyenda bwino kwa zinthu kwangoyamba. Pali zina zambiri zoti zichitike. Tsopano pakusoweka amishoni oti ayambe ntchito m'madera atsopano, anthu a m'maiko momwemo kapenanso ochokera kumaiko ena, chosowachi, ndi chachikulu kuposa poyamba.

Ntchito ya mpingo inafikanso ku BOTSWANA ndi NAMIBIA, maiko omwe ali ogwirizana pantchito yomwe inayambika kale. Kayendetsedwe ka ntchitoyi kakhala kabwino ndi kolimbitsa mtima.

KENYA, dziko lomwe lili kumpoto, kutali ndi komwe ntchito inayamba kale, ntchito ya mpingo inayambika kumeneko ndipo ntchito ikuyenda bwino kwambiri kotero kuti mpingo wakhala wodabwa ndi kupita patsogolo kwa ntchitoyo. Pali chikonzero chomanga Seminale mu Africa m'dziko la Kenya.

KUMADZULO KWA AFRICA mpingo wangofika kumene. Tsopano tayamba ntchito ya mpingo wathu ku maiko a Cote de Ivoire, Nigeria ndi ku Cape Verde.

Mwina chopambana kwambiri ndi chokondweretsa ndicho KUKULA kwa mpingo pa CHIWERENGERO cha anthu ndi NDALAMA izi zikuchitika mu chigawo chonse cha Africa. MULUNGU ALI NDI CHIKONZERO CHACHIKULU KU MAIKO A MU AFRICA.

# ANAZARENE AMAGWIRA NTCHITO PAMODZI

## Mpingo Monga Thupi La Khristu

Yesu ali ndi ntchito yoti agwire m'dziko lapansi. Ife ndife thupi lake; ndife amene tingaigwire ntchitoyi m'malo mwake. Ndikofunika kwambiri kuti thupi lonse ligwire ntchito pamodzi. Kuti izi zitheke tiyenera kukhala ndi chikonzero chomwe chingatidziwitse bwino za mgwirizano ndi ntchito, malamulo ndi cholinga. BUKU LA MALAMULO NDI MAYENDETSEDWE AKE *(Manual)* ndi lomwe lingatipatse ife mawu otitsogolera.

## M'mene Imayendera Ntchito Ya Mpingo Wa Nazarene

Pali makhwerero atatu oyendetsera ntchito mu Mpingo wa Nazarene. Khwerero loyamba limatchedwa MPINGO PAOKHA *(Local Church).* Ili ndilo la Akhristu onse a mpingo paokha kuphatikizapo ntchito yomwe umagwira pakati pa anthu omwe ali nawo pafupi. Iyi ndiyo ntchito yoyamba pantchito ya Khristu.

Khwerero lachiwiri ndi la CHIGAWO; bungwe la matchalitchi a paokha lonse lothandiza ndi kulimbikitsana wina ndi mnzake ndi kugwira ntchito pamodzi yokhazikitsa matchalitchi kumalo oyandikana nawo komwe kulibe mpingo.

Khwerero lachitatu ndi la MPINGO WONSE *(General Church).* Zigawo *(districts)* zimakumana ku Msonkhano Waukulu (*General Assembly)* kukambirana za atsogoleri, malamulo, kayendetsedwe ka ntchito, ngakhalenso Zoyenera Kuzikhulupilira kwa Mulungu. Ntchito yofalitsa Uthenga Wabwino kudziko lonse lapansi, kumatchalitchi ndi mautumiki ake kuzigawo *(districts)* ndi a paokha, monga za opuma pa ntchito, zosindikiza mabuku, za Sande Sukulu; kufalitsa Uthenga Wabwino ndi za wailesi zonse zimachokera pakhwerero limeneli. Likulu la Mpingo padziko lonse lapansi lili ku Kansas City, ku Missouri m'dziko la America, ndipo maofesi a chigawo *(Region)* a likulu la mpingo, monga chigawo chathu chino cha Africa chomwe maofesi ake ali ku Manzini, m'dziko la Swaziland, ali m'malo odziwika bwino padziko lonse lapansi.

## Likulu La Mpingo

Likulu la Mpingo *(General Church)* lili ndi magawo atatu: Msonkhano Waukulu *(General Assembly)*, Bungwe Lalikulu Loyendetsa Ntchito Za Mpingo Wonse *(General Board)*, ndi Bungwe La Atsogoleri A Mpingo Wonse *(General Superintendents)*.

**Msonkhano Waukulu** ***(General Assembly)*** ndi msonkhano wa nthumwi zochokera kuzigawo za Mpingo wa Nazarene zopezeka padziko lonse lapansi. Uwu ndi msonkhano waukulu kwambiri mumpingo, ndipo umachitika pakatha zaka zinayi.

Anthu zikwizikwi omwe sinthumwi za kumsonkhanowo amapita kukaonera ndi kukhala nawo pamisonkhano ya chikondwerero.

Theka la chiwerengero cha nthumwi za ku Msonkhano Waukulu chimayenera kukhala cha mamembala a mpingo, ndipo theka linalo limakhala abusa odzozedwa. Akulu ochokera ku Mpingo Wonse (General Church) ndi amene amakhala mamembala a kumsonkhanowo.

Kumsonkano Waukuluwu Zomwe Zimachitika Ndi Izi:

Kusankha Atsogoleri A Mpingo Wonse *(General Superintendents)* oyang'anira ntchito za mpingo padziko lonse lapansi.

Kusankha mamembala a Bungwe Lalikulu Loyendetsa Ntchito Za Mpingo Wonse *(General Board)* ndi mabungwe ena komanso akuluakulu otumikira Mpingo Wonse.

Kukonzanso malamulo ena monga momwe zigawo *(Districts)* zapemphedwa kuti zisinthike M'BUKU LA MALAMULO NDI MAYENDETSEDWE AKE *(Manual)*.

**Bungwe La Atsogoleri A Mpingo Wonse** ***(General Superintendents)*** mumakhala abusa odzozedwa *(ordained elders)* asanu ndi m'modzi ndipo amasankhidwa ku Msonkhano Waukulu *(General Assembly)*. Anthu amenewa amayendetsa ntchito ya mpingo padziko lonse lapansi. Iwo amakhala apampando a misonkhano ikuluikulu, mabungwe ndi zigawo zina za mpingo. Amakhalanso apampando a misonkhano ya pachaka ya kuzigawo. Mwinanso udindo wawo waukulu ndi kudzoza anthu amene msonkhano wa pachaka wa chigawo wavomereza kuti akhale abusa odzodzedwa *(elders)* kapena a atumiki odzodzedwa *(deacons)*.

**Bungwe Lalikulu Loyendetsa Ntchito Za Mpingo Wonse** *(General Board)* limakhala ndi chiwerengero chofanana ndi cha mamembala a mpingo ndi abusa odzozedwa *(elders)*. Apampando ake amakhala Atsogoleri A Mpingo Wonse *(General Superintendents)*. Bungweli lili ndi mphamvu yopanga malamulo a mpingo pa Msonkhano Waukulu utachitika kale komanso wotsatira usanachitike. Kuti malamulowa ayambe kugwira ntchito ku Likulu La Mpingo *(General Headquarters)*. Bungwe Lalikulu Loyendetsa Ntchito Za Mpingo Wonse *(General Board)* ndi lomwe limalemba anthu a ntchitowa ndi kuona m'mene akugwiritsira ntchito ndalama.

LIKULU LA MPINGO *(General Headquarters)* ndi gulu la antchito lomwe limathandiza a Bungwe la Atsogoleri A Mpingo Wonse *(General Superintendents)*, Bungwe Lalikulu *(General Board)*, ndi ogwira ntchito ku ofesi ya ku Likulu la mpingo *(General Church)*. Likululi linagawidwa muzigawo, ndipo chigawo chilichonse chili ndi woyang'anira *(director)*, woona zosowa za mpingo ndi zofunika zina. Chigawo cha "Missions Division" ndicho chachikulu kwambiri chifukwa ndi chimene chimayang'anira amishoni pafupifupi 6,000 padziko lonse lapansi, ndi kayendetsedwe ka ntchito yongoyambika kumene *(Pioneer, National Mission, ndi Mission Districts)*.

CHIGAWO *(Region)* changogawidwa kumene. Chigawo cha Africa ndi chitsanzo chabwino cha m'mene ikuyendera ntchito ya chigawo. Maofesi amenewa ndi nthambi ya ku Likulu la Mpingo *(General Headquaters)*, ndipo ofesi ya chigawo *(Region)* ndi yomwe imagwira ntchito m'malo mwa Likulu la Mpingo *(General Church)* ndi matchalitchi mu zigawo (madistrict) ndi matchalitchi mu Africa. Maofesiwanso ndi gawo limodzi la *"World Mission Division"* ku Likulu la Mpingo padziko lonse lapansi.

## Chigawo *(District)*

Chigawo cha Mpingo wa Nazarene chili ndi zochitika zitatu: Msonkhano wa Pachaka, Mtsogoleri wa Chigawo, ndi Mabungwe ena a Chigawo. Apa tikufotokoza malamulo amene zigawo zomwe ndi madistrict a Eni Nthaka *(Regular Districts)* zimayendera. Zigawo zatsopano (Dera Loyamba Latsopano, Malo Oyamba Atsopano, Malo Amene Akulamulidwa Ndi Amishoni Ndi Eni Nthaka Pamodzi, Malo Amene Ali Kudzithandiza Pamodzi Ndi Amishoni) zimayamba ndi

kabungwe kakang'ono ndipo chigawo chikhoza kukula kwenikweni pokhapokha chitayenerezedwa kukhala Madisitilikiti A Eni Nthaka *(Regular Districts).*

**MSONKHANO WA PACHAKA WA CHIGAWO *(District Assembly)*** ndi kukumana komwe kumachitika chaka chilichonse, ndipo zimakumana ndi nthumwi zochokera kumatchalitchi a paokha onse a chigawocho kuti adzamve m'mene ntchito ikupitira patsogolo ndi kuchitanso zina zofunika mu chigawo. Nthawi zonse tizikumbukira kuti ntchito yaikulu yomwe imachitika muchigawo ndi yofalitsa Uthenga Wabwino. Tchalitchi iliyonse imasankha mamembala omwe amakhala nthumwi kumsonkhanowo. Anthu omwe ali ndi maudindo akuluakulu (monga mtsogoleri wa NWMS, Mtsogoleri wa Sande Sukulu, Mtsogoleri wa (NYI) m'matchalitchi apaokha aliwonse amakhala nthumwi za kumsonkhanowo popanda chisankho. Abusa onse odzozedwa, abusa amalayisensi, atumiki odzozedwa, akulu a district, ndi amishoni omwe ndi mamembala a mpingo m'chigawocho, amakhala mamembala a kumsonkhano wapachakawo, ndipo amakhala ndi mwayi woti nkulankhula ndi kuchita nawo chisankho monga nthumwi.

Ntchito yaikulu ya Msonkhano wa Pachaka wa chigawo ndi:

Kusankha Mtsogoleri wa Chigawo.

Kusankha mamembala a m'mabungwe ndi m'makomiti osiyanasiyana a mu chigawo.

Kukonza ndondomeko wa m'mene ndalama zigwiritsidwire ntchito ndi kuyendetsa msonkhano wa chigawo monga m'mene limanenera BUKU LA MALAMULO NDI MAYENDETSEDWE AKE *(Manual)*

Kupereka makalata a zilolezo zowayenereza *(licenses)* kwa abusa kulalikira, komanso makalatawa amaperekedwa kwa alaliki oyendayenda, komanso ena omwe amatumikira mu mpingo omwe ndi osadzozedwa.

Kuchita chisankho cha anthu omwe ali ndi zowayenereza ndipo avomerezedwa ndi bungwe loyenera m'chigawocho kuti iwo asankhidwe ndi msonkhanowo kukhala abusa odzozedwa kapena atumiki odzozedwa *(deacons).*

Kusankha nthumwi zokaimira Msonkhano Waukulu *(General*

*Assembly).*

**MABUNGWE A CHIGAWO** *(District Boards)* Chigawo chikakhalachachikulu mabungwe akhoza kukhazikitsidwa. Zigawo zomwe zakhazikitsidwa ziyenera kukhala ndi mabungwe osachepera awiri: Bungwe La Alangizi La Chigawo (District Advisory Board) ndi Bungwe Losungitsa Mwambo Mu Mpingo *(District Ministerial Credentials Board).*

BUNGWE LA ALANGIZI *(Advisory Board)* likhoza kugwira ntchito m'malo mwa bungwe lina lililonse kupatula Bungwe La Alangizi *(Ministerial Credentials).* Bungweli limathandiza mtsogoleri wa chigawo poyendetsa ntchito za chigawo. Bungweli mamembala ake amakhala a mpingo ndi abusa odzozedwa.

BUNGWE LOSUNGITSA MWAMBO MU MPINGO *(Ministerial Credentials Board).* Bungwe limeneli limakhala la abusa odzozedwa okhaokha. Ntchito yake ndi yoona ngati mbusa kapena mtumiki yemwe wapempha chilolezo chogwirira ntchito *(license)* kapena wapempha kuti adzozedwe ali ndi mphatso ndi chisomo zoonetsa kuti waitanidwadi ndipo iye wakonzekeradi.

**MTSOGOLERI WA CHIGAWO** *(District Superintendent)* ndiyemweamayang'anira ntchito ya chigawo. Iye ali ndi udindo wolangiza abusa ndi matchalitchi, kuyamikira kapena kusankha abusa, kulandira ndi kuyang'anira matchalitchi a muchigawo chake. Iye ndi mtsogoleri yemwe masomphenya ndi cholinga chake zimapititsa ntchito ya chigawocho mtsogolo. Amathandiza abusa a muchigawocho kuti azichita ntchito yabwino.

## Tchalitchi La Palokha *(Local Church)*

Tchalitchi ndilo gawo lofunika kwambiri pakayendetsedwe ka mpingo. Zina zilizonse zomwe zimachitika ndi zothandiza kuti ntchitoyi ipite patsogolo. Pamenepa ndipo pamakhala kupembedza, kulemekeza, kuchitira umboni ndi kulangiza. Pamenepa Mulungu ndi munthu amakumana pamodzi ndipo chotsatira chake ndi chiombolo. Tchalitchi lililonse limatsogozedwa ndi mbusa. Mbusayo amathandizidwa ndi Komiti ya pa Tchalitchi kapenanso bungwe lina lililonse lomwe lingathandize. Pakhoza kukhala mabungwe ambiri. Mbusa ndi mabungwe ena onse, ndi akuluakulu ena a mpingo amayankha mafunso pa Msonkhano wa Pachaka

wa pa Tchalitchi.

**MSONKHANO WA PATCHALITCHI** womwe umaona ntchito za mpingo pa tchalitchi, ndipo uyenera kuchitika kamodzi pachaka. Mabungwe ndi atsogoleri amasankhidwa ndipo malipoti a m'mene ikuyendera ntchito amaperekedwa. Kumasankhidwanso nthumwi za misonkhano yapadera ngati mpingo ukufuna kuitana mbusa. Mamembala onse a Mpingo paokha akhoza kuchita chisankho pamisonkhanoyi.

BUNGWE (KOMITI) LA PA TCHALITCHI *(Church Board)* wapampando wake amakhala mbusa ndipo bungweli limaona za malipiro a anthu ogwira ntchito patchalitchi, ndondomeko ya m'mene ndalama zingagwiritsidwire ntchito, kuyang'anira malo ndi nyumba za patchalitchipo. Ntchito yoyamba ya bungweli ndi yoona kuti tchalitchi ikukwaniritsa cholinga cha Mulungu pa anthu ake.

BUNGWE LA MOYO WA CHIKHRISTU NDI SANDE SUKULU *(Board of Christian Life and Sunday School)* lili ndi udindo woyambitsa ndi kugwiritsa ntchito mapologramu omwe anthu a mutchalitchi angawafune. Zochitachita za Sande Sukulu ndi za achinyamata ndizo zili patsogolo m'bungwe limeneli.

BUNGWE LOFALITSA UTHENGA PADZIKO LONSE LAPANSI *(NWMS)* limagwira ntchito mogwirizana ndi Bungwe La Moyo Wa· Chikhristu, komanso makamaka masomphenya ake amakhala cholinga cha mpingo kufalitsa

Uthenga Wabwino padziko lonse lapansi. Patchalitchi pakhoza kukhala makomiti kapena mabungwe ambiri molingana ndi m'mene Tchalitchi La Palokha laonera kuti ndi kofunika.

**MBUSA** ndiye mtsogoleri wa patchalitchi. Ali ndi udindo woona za moyo wa mumpingo kuuzimu ndi wa kuthupi. Amatsogolera, kulangiza ndi kuphunzitsa anthu ake. Amawauza anthu ake Mawu a Mulungu. Tchalitchi Lapalokha likhoza kukhala ndi abusa angapo.

Iye ayenera kulalikira Uthenga Wabwino, kuchititsa mapemphero kawirikawiri, kuchezera anthu, kulangiza, ndi kuwavomereza Akhristu kuti akhale mamembala a mpingo. Amatumikira kuzosowa za nkhosa zake. Ndi udindo wake kubatiza Akhristu, kuwakwatitsa ndi kuikitsa malipiro.

Tchalitchi la Palokha *(Local Church)* lili ndi udindo wosamalira mbusa wawo. Ayenera kumpatsa malipiro, nyumba, thandizo lakupuma pantchito *(pension)* ndi kumuthandiza akamagwira ntchito yake.

**MEMBALA WA MPINGO.** Mkhristu aliyense ayenera kukhala membala wochirimika mumpingo. Aliyense azipeza mbali ya utumiki kumpingo pamene akhoza kuchita mbali yake monga chiwalo cha thupi la Khristu. Mutu wotsirizawu ukufotokoza zinthu zimene ife tingachite potumikira.

→ → → → → → →

## Mutu Wakhumi Ndi Chiwiri

## AFRICA ADZIWE YESU

### Lamulo La Yesu Khristu

Yesu anawauza ophunzira ake m'mabuku awa: *(Mateyu 28:19-20, Marko 16:15, 16, Luka 24:47)* kuti apite kudziko lonse lapansi kuti akachite izi:

Akalalikire Uthenga Wabwino kwa munthu aliyense—kuti apulumutsidwe.

Akaphunzitse munthu aliyense njira za Mulungu—kuti akadziwe choonadi.

Akawalangize okhulupirira—kuti amutsate Yesu.

Akawabatize okhulupirira—kuti akakhale amodzi monga thupi lake.

Yesu anauza mpingo wake zoti uchite: *(Machitidwe 1:8)*

Yerusalemu— mupite kwa iwo amene ali pafupi nanu.

Yudea—mupite kwa anansi anu.

Samaria—muwatsate anansi anu omwe saganiziridwa.

Dziko lonse lapansi—Uthenga Wabwino ndi wa anthu onse.

Yesu sananene kuti choyamba tifike kumadera onse a ku Yerusalemu tisanapite kumadera ena. Akunena momveka bwino kuti uthenga wake ndi wa aliyense ndipo masomphenya athu asamangokhala pa ife tokha. Komanso sikuti ankangolankhula ndi atumwi okha, koma kwa otsatira ake onse. Ntchitoyi ili kwa ife tonse.

### Ntchito Ya Mpingo Kufalitsa Uthenga Wabwino Pa Dziko Lonse Lapansi

Chiyambire, Mpingo wa Nazarene uli ndi udindo kufalitsa Uthenga Wabwino pa dziko lonse lapansi. Timakhulupilira kuti Anazarene onse ayenera kugwira ntchito yotumikira Mulungu m'matchalitchi apaokha mwawo ndipo azitenga mbali pofalitsa Uthenga Pa Dziko Lonse Lapansi. Bungwe lathu Lofalitsa Uthenga Pa Dziko Lonse Lapansi

*(NWMS–Nazarene World Mission Society)* limatiyikira patsogolo mtolo wogwira ntchito ya Mulungu padziko lapansi, kutiuza kuti titenge nawo mbali. Pali maiko ambiri amene akusowekabe kumva Uthenga wa Chiyeretso *(Aroma 15:20)*. Mabungwe a pa tchalitchi la palokha pathu ayenera kumalimbikitsa ndi kumapereka mwayi wothandiza kumadera awo.

## Ntchito Yathu M'maiko A Mu Africa

M'maiko omwe tili ndi matchalitchi ndi awa:

| | | | |
|---|---|---|---|
| Angola | Botswana | Cape Verde | Ciskei |
| Côte d'Ivoire | Eritrea | Ethiopia | Ghana |
| Kenya | Lesotho | Liberia | Madagascar |
| Malawi | Mozambique | Namibia | Nigeria |
| Rwanda | Senegal | South Africa | Swaziland |
| Tanzania | Uganda | Zaire | Zimbabwe |
| Zambia | | | |

M'maiko momwe tikufunika kulowamo ndi awa:

| | | | |
|---|---|---|---|
| Ascension | **Burkina Faso** | **Benin** | **Burundi** |
| Cameroon | Central Africa Republic | Chad | Guinea |
| Comoros | **Congo Republic** | Gabon | Mali |
| Gambia | Equatorial Guinea | Mauritius | Niger |
| St Helena | Guinea Bissau | **Togo** | **São Tomé** |
| Niger | Mauritania | Sudan | Somalia |
| Seychelles | Western Sahara | | |

Maiko omwe talemba mowala kwambiriwa ndi amene tikuyembekezera kulowamo posachedwa. Ntchito imene ili patsogolo pathu ndi yaikulu, ndipo ikhoza kugwirika pokhapokha ngati mamembala a chigawo chino cha Africa atatenga mbali.

## Kodi Ntchito Ya Mpingo Ikundikhudza Bwanji Ine?

Lamulo la Yesu likundipempha kuti ndipite kwa anthu oyandikana nawo, m'dziko langa, Africa ndi dziko lonse lapansi. Umenewo ndi mtolo wanga. Palibe m'modzi wa ife amene akusowa kukumbutsidwa kuti dziko lapansi ladzala ndi zoyipa. Tili ndi mayankho pachifukwa chomwe tikufunira kukhala ndi nyumba zolongosoka, anthu oona mtima, boma la chilungamo ndi mtendere wa padziko lonse lapansi. Izi si zongopeka, ndi zoonadi. Tiyenera kufotokozera dziko lapansi mayankhowa motsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

## Ndingachite Chiyani?

Pali zinthu zinayi zoti tizionetsetse. Choyamba, ndiyenera KUKHALA MUNTHU wamakhalidwe amene Mulungu akufuna kuti ndikhale. Chachiwiri, ndiyenera KUGWIRA NTCHITO zimene Mulungu akufuna kuti ndigwire. Chachitatu, ndiyenera KUPEREKA monga m'mene Mulungu afunira. Chachinayi, ndiyenera KUMVERA Mulungu akandiitana ku utumiki wapadera.

## Umunthu Wanga

Ndikufuna kwambiri kukumbukira kuti chimene Mulungu amafunitsitsa m'moyo mwanga sikuti ndizikhala wotanganidwa, koma kuti nthawi zonse ndizilola Mzimu Woyera azindithandiza kuti ndikhale monga Yesu. Mzimu wotumikira womvera ndi wofunika. Munthu wonyada ndi wosamvera kapena wamkwiyo ndi wotsutsa, sangathandize Thupi la Khristu kuti likhale lochita bwino kapenanso kuthandiza pantchito yake!

## Ntchito Zochita

Mphatso zimene Mzimu Woyera anatipatsa *(Aefeso 4:11-15)* zimatithandiza kudziwa malo a utumiki omwe tingakhale nao mumpingo. Zosowa za mumpingo zikhozanso kundisonyeza ine zinthu zomwe ndiyenera kuzichita chifukwa ndiyenera kuchita zinthu zomwe zili zofunika. Zina zomwe ndingachite ndi izi:

KUPHUNZITSA. Pakusoweka anthu odzipereka omwe ali ndi mphatso ya uphunzitsi kuti agwire ntchito mu Sande Sukulu ndi maphunziro a m'Buku Lopatulika.

KUCHEZERA ODWALA. Anthu ambiri akudwala, ndi

kusungulumwa, kapenanso kusowa chilimbikitso. Zingathandize patakhala munthu wokawasangalatsa ndi kuwauza mawu odzetsa mtendere.

UKHONDO NDI KUKONZA. Ndi utumiki wofunika mumpingo. Ntchitoyi ndi yapafupi komanso ndi yofunika kwambiri chifukwa imalemekeza Mulungu ndi kukondweretsa aliyense mumpingo.

KUPEMPHERA. Utumiki wopempherera atsogoleri athu, misonkhano ya m'tchalitchi, ndi ena omwe ali ndi zosowa kuthupi ndi kuuzimu ndi utumiki womwe ungachitike ndi Akhristu okhudzidwa. Gulu la anthu opemphera limalimbikitsa mpingo.

KULANDIRA ALENDO. Mpingo uliwonse umasowa anthu olandira alendo, omwenso mitima ndi nyumba zawo zili zotseguka polandira anthu osowa abwenzi, pokhala ndi chakudya.

KUCHITIRA UMBONI KWA MUNTHU WINA NDI MNZAKE *(Personal Evangelism)*. Akhristu omwe ali ndi mphatso yogwira ntchito ndi anthu oyenera kuphunzitsa anthu ndi kuwayendera anthu powauza Uthenga Wabwino. Anthu otere akusoweka mumpingo ndi m'mautumiki ena opita kwina ndi kwina.

ZOIMBAIMBA. Maimbidwe abwino m'mawu ndi zida amakhala dalitso lalikulu. Ndi mwayi wapadera kukhala ndi dalitso lotere. Kuimba kwa m'tchalitchi sichionetsero koma ndi utumiki. Kuimbaku kumafunika kukonzekera ndi kupemphera kuti kukhale njira yomwe Mzimu Woyera akhoza kudalitsira.

CHIMWEMWE NDI CHISANGALALO. Mkhristu aliyense akhoza ndipo ayenera kumathokoza. Munthu yemwe amadzetsa chimwemwe ndi chisangalalo nthawi zonse ndi munthu amene amakhala dalitso mumpingo. Mzimu womangodandaula ndi wamtsutso umakhala wowononga. Imodzi mwa njira zomwe ndingatumikire nazo mpingo wanga ndizo kukhala wachimwemwe.

## Kupereka

Anazarene ndi anthu omwe amapereka chifukwa Mzimu Woyera amatitsogolera ku moyo wopereka. Timayembekeza kuti Anazarene azipereka chachikhumi ndi zopereka zina kwa Ambuye mokondwera, komanso ndi kuthandiza zosowa za mbusa wawo. Chuma chathu

timachisunga muntchito ya chigawo, pophunzitsa achinyamata kulalikira Uthenga Wabwino ndi kukwaniritsa zosowa za padziko lapansi. Zimangotivuta kuti tilibe zambiri zoti nkupereka. Pofuna kukwaniritsa zosowa zonse za ntchito yake, tiyenera kupereka. Pamene tipereka, mbusa wa patchalitchi adzakhala ndi mphotho yoyenera, tidzasunga ndi kusamala bwino tchalitchi lathu, ndiponso Uthenga Wabwino udzakhala ukufalitsidwa. Taonani *Malaki 3:10.*

Sitimangopereka ndalama zokha, komanso zokolola ndi ziweto zathu. Tiyenera kukhala ndi mzimu wopereka ndiponso kumapereka nthawi yathu, mphatso zathu *(talent)* komanso zinthu zomwe tili nazo. Pali mwayi woti tikhoza kupereka pothandiza patchalitchi lathu komanso kuchigawo ngakhalenso kugulu logwira ntchito ndi kuchitira umboni *(Work and Witness Team)* padziko lonse lapansi.

## Kupita

Nthawi zina Mulungu amatiitana kuti tigwire ntchito yapadera mumpingo. Zikatero, Mulungu ndi amene amapitiriza kuitanako. Mpingo uyenera kuchitira umboni woti munthu amene akunena kuti waitanidwayo ali ndi mphatso ndi chisomo zoyenera pokwaniritsa maitanidwe akewo.

## Kodi Ndi Maitanidwe Otani Omwe Mpingo Wa Nazarene Umawazindikira?

Timazindikira maitanidwe a mitundu itatu: Kulalikira, kukhala Wamishoni, ndi Utumiki *(deacon)*. Kuitanidwa kuti tikalalikire amafuna Mulungu kuti tivomereze udindo wopita kukafalitsa Mawu a Mulungu. Kumeneku ndiye kukhala mbusa wa tchalitchi la palokha *(local Church)*. Mbusa wovomerezeka akhoza kukhala mlaliki woyendayenda *(evangelist)*, kapenanso akhoza kusankhidwa kuti akhale mtsogoleri wa chigawo *(district superintendent)* kapenanso mtsogoleri wamkulu wa mpingo pa dziko lonse lapansi *(General Superintendent)*. Munthu wotere amatchedwa MBUSA WODZODZEDWA *(Elder)*.

Munthu akaitanidwa kukhala WAMISHONI *(Missionary)* yenera kudzipereka popita ndi Uthenga Wabwino kwa anthu ndi malo osiyanasiyana. Amishoni akhoza kukhalanso abusa, a deacon kapenanso mamembala a mpingo omwe akugwira ntchito mu utumiki wothandiza osowa.

## Ndingadziwe Bwanji Kuti Mulungu Wandiitana?

Palibe chizindikiro chilichonse chosonyeza kuti Mulungu wandiitana. Chitsimikizo chanu ndi m'meme mumaonera pachisankho chanu izi ndi gawo lopambana pa maitanidwe anu. Mulungu akhoza kupereka masomphenya kapena chizindikiro chapadera koma izi sizichitika nthawi zonse. Nthawi zambiri kuitanaku kumangooneka m'kati mwa mtima. Nthawi zambiri atsogoleri a mpingo amatithandiza potitsimikizira za maitanidwewa.

## Mulungu Akandiitana Ndichite Chiyani?

Ndiyenera kumvera maitanidwe a Mulungu ndikuvomereza kuti m'moyo mwanga ndikhale ndi cholinga chokwaniritsa. Khwerero loyamba ndilo kulankhula ndi mbusa wanga. Adzanditsogolera pondiuza zomwe ndiyenera kuchita. Ndiyenera kukhalanso wochilimika kutchalitchi kwanga, kuonetsa kuti ndinedi woitanidwa. Tchalitchi langa likakhutiradi kuti ndaitanidwa lidzandiyamikira kwa Mtsogoleri wa Chigawo *(District Superintendent)* ndi Bungwe La Alangizi La Chigawo *(District Advisory Board)*. Feimaitanidwe anga ndi a ntchito ya mishoni ndiyenera kuwalembera a Atsogoleri a Chigawo ndiponso ku ofesi ya Mkulu wa Mpingo Wa Nazarene Ku Africa *(African Region Director's Office)* ndipo adzandiuza zoyenera kuchita.

## Mulungu Akandiitana Ndiyenera Kukonzekera

Pa *2 Timoteo 2:15* akutiuza kuti tiyenera kukonzekera pakugwira ntchito yathu. Ndikakonzekera bwino ndidzakhala wa phindu pamaso pa Mulungu. Timalimbikitsa kwambiri maphunziro a ku Koleji ya ubusa (kapena *Extension)*. Kukonzekera koyenera kungakhoze kufuna zoposa izi.

Mulungu amatikonda ndipo akufuna tizikhala opambana. Safuna tizikhala ofooka muuzimu koma tikhale anthu amphamvu ndi olimba mtima. Tikhoza kumukhulupirira kuti atsogolere miyoyo yathu.

→ → → → → → →

# KUTSATIRA YESU PAMODZI

## Katekisimu Wa Mpingo Wa Nazarene Mu Africa

Mlembi: Dr. Theodore P. Esselstyn

English Title: Following Jesus Together
in Chichewa

Translated By:
Malawi Literature Office
P. O. Box 90566
Bangwe, Blantyre 9
MALAWI

Printed November 2000

ISBN 0-7977-0143-5

Published by
Africa Nazarene Publications
P. O. Box 1288, Florida
1710 Republic of South Africa

*Buku ili linatanthauziridwa ndi:*

| | |
|---|---|
| T. Mbendera | C. K. Phiri |
| D. Mbendera | L. K. Domoya, DS |
| F. Sabwera | R. B. Kalitera, DS |
| P. Katimba | N. Miller |